# CHIKUNJA CHICHITA MAZIKO M'CHI–ADVENTIST

## Utatu - Kulibe Mzimu Woyera – Masabata a Miyezi – Masiku A Zikondwerero – Masewero Auzimu – Mitu 7 Chibv. 17

### ZIPHUNZITSO ZA CHIKUNJA M'CHI – ADVENTIST

Zalembedwa m'munsimu zifunika nzeru zakuya kuti munthu azimvetsetse bwino. Nzochita kufuna kuwakonzetsera malingalirobwinobwino ngati wina akufunitsitsa kuphunzira izi mozama. Kwalembedwa: "Ife tiri ndi malamulo a Mulungu ndi umboni wa Yesu Khristu, zomwe ndi Mau a Mzimu wa Chinenero. Ngale zotsikitsitsa mtengo zimadziwika kudzera m'mau a Mulungu. Choncho onse ofufuza mau awa ayenera kutero m'nzeru yoyera yopanda chirema. Akhale opanda zilakolako zoipa m'kadyedwe ndi kamwedwe kao. Ngati sangatero, malingaliro ao adzanka akusokonekera; kotero kuti sangathe kupita chitsogolo pa ntchito yao yonka akufufuza mozama ndi mwachipambano kuti amvetsetse za zizindikilo zosonyeza kuyandikitsitsa kwa mapeto a mathedwe a mbiri ya dziko lapansi." {TM 114}

### CHIPHUNZITSO CHA UTATU

Chiphunzitsochi chikukhuza chikhalidwe ndi ntchito za "Mphamvu Zikuruzikuru Zitatu za Kumwamba."Bungwe la makono lokana za Utatu likunka likuphunzitsa kuti kulibe Utatu mu Umulungu. Limati Mzimu Woyera sigawo limodzi la Umulungu koma mphamvu ya machitachita oyera ya Mulungu Atate ndi Mwana. M'modzi wina woimira bungwe'li monama akufotokoza kuti, "Bukhu Lopatulika likuphunzitsa kuti pali magawo a Umulungu awiri okha omwe ayenera kupembedzedwa."

Chiphunzitsochi chimati (chikufotokoza) kuti, Yesu ndi Mwana wa Mulungu ngati momwe ali mwana wina aliyense wobalidwa, ndipo kukhala moyo kwake kunayambira pamene Atate anam'bala lye osati kuti ndi wamyaya monga Atateyo. Winanso wa bungwe'li akufotokoza kuti, "Ngakhale Atate ndi Mwana ali Mulungu m'modzi, koma ndi osiyana mphamvu." Ndipo ichi n'chifukwa chake Khristu, ndiye anafa osati Atate yemwe ndi mzimu ndipo nkosatheka lye kufa. Anthuwa amati chiphunzitso chaochi chiri ndi umboni kuchokera kwa a Adventist oyambirira omwenso anakana kuti kulibe utatu m'zaka za 1840 mpaka 1890.

Monga ziri ziphunzitso zolakwika zina zonse, chonchonso ndi maziko a chipunzitso cha Utatu. Ku msonkhano wa Nikaya m'chaka cha A.D. 325, bungwe la upapa linabvomereza chiphunzitso cha Utatu. Linagwirizana zoti Umulungu wapangidwa ndi mphamvu zitatu, zokhala ndi machitidwe ndiponso chikhalidwe



chimodzi, koma bungwe'li linatanthauzira Utatuwo kuthupi ndi m'nzeru ya umunthu.

Mwachitsanzo, pofotokoza za Utatu m'maphunziro a kalasi la ulimbitso, mpingo wa Katolika umati, "Mwana amachokera kwa Atate m'machitidwe a nzeru yakuya, otchedwa 'Kubadwa Nthawi Iri Yonse,' kutanthauza kuti nthawi iri yonse Atate amangokhalira kum'bala Mwana wake tsiku ndi tsiku ndiponso mphindi iri yonse, kotero kuti palibe nthawi imene Mwanayo samabalidwa." Bukhu lophunzitsira za ulimbitsoli likupitiriza kufotokoza kuti nkosatheka m'njira iri yonse Atate ndi Mwana kulekana, kotero kuti nthawi ija Mwana anali pa dziko lapansi pano, awiriwa anali limodzi osapatukana, chifukwa atangoti apatukane, kubadwa kwa Mwana kwa nthawi zonseko kungasokonekere, kosatheka kunka kukuchitika m'mphindi iri yonse. Kutero kungapangitse Mwana kusakhalako, komwe kutanthauzanso kuti Atate kulibe. Tsono popeza awiriwa ali mmodzi nthawi zonse, ndiye kuti Atate kapena Mwana sangakhaleko ngati m'modzi wa iwo atasowa kwa mnzake. (Alfred Mortimer, Catholic Faith and Practice). Momwe zikunenedweramu chingakhale chodabwitsa kuti a Adventist oyambirira anachikana chiphunzitso cha Utatuchi? A J. N. Andrew akuyankha, "Chiphunzitso ichi chikusokoneza chikhalidwe cha Mulungu ndi cha Mwana wake Yesu Khristu Ambuye wathu." (Review and Herald, March 6, 1855).

### Gawo: A – Utatu

Ngati tikufunitsitsa kuchitchinjiriza choonadi cha Utatu m'dzina la umodzi wa Umulungu, ndi bwino kutsatira chiphunzitso cha Bukhu Lopatulika chomwe chimautcha Utatawo Mulungu-Mmodzi-m'Utatu monga anachitira Ellen White nthawi zonse.

Mateyu 28:19 tinalamulidwa kubatiza okhulupirira "m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera." Liu "Dzina" likuimira khalidwe limodzi, kutanthauza kuti atatu omwe atchulidwawo ndi ofanana m'zonse, kuonjezera pakukhala kwao a mphamvu zofanana. Dzina Utatu'li likusonyeza kuti Atatu'wo m'umodzi wao ali Mulungu Mmodzi.

Pa Yohane 14:16 Yesu akulonjeza zotumiza "Nkhoswe ina." Liu "ina" likusonyeza wina wokhala ndi chikhalidwe ngati cha Yesuyo, komanso wofanana naye udindo.

Pa 2 Akorinto 13:14 tikuwerenga mau akuti "Chisomo cha Ambuye Yesu Khristu, ndi chikondi cha Mulungu, ndi chiyanjano cha Mzimu Woyera." Izi ndi mphatso zitatu zochokera ku Umodzi wopangidwa ndi Atatuwo.

1 Petro 1:2 akuti, "monga mwa kudziwiratu kwa Mulungu Atate, mchiyeretso cha Mzimu, ... ndi kuwaza kwa mwazi wa Yesu Khristu." Apa tikuona ntchito zitatu za aliyense wa okhala mu Utatu.

M'Mau a Mzimu Wachinenero muli maumboni ambiri ofotokoza za Utatu. Mwachitsanzo:

"Mphamvu zikuruzikuru zitatu za Kumwamba" (8T 254). "Amoyo atatu a Utatu wakumwamba." (Ev 615). "Iwo olemekezeka a myaya akumwamba – Mulungu, ndi Khristu, ndiponso Mzimu Woyera" (Ev 616). " Mphamvu za zikuruzikuru za kumwamba – Atate, ndi Mwana, ndi Mzimu Woyera." (Ev 617).

### Gawo B: – Mzimu Woyera

Pali umboni wokwanira m'Malembo kuti Mzimu Woyera ali Mphamvu yokhala ndi umwini ndi moyo payokha koma ali chikhalire mmodzi wa Utatu.

Pa Aefeso 4:30 Mzimu Woyera amamva chisoni. Pa 1 Akorinto 12:11 Mzimu amagawira mphatso "yense pa yekha monga afuna." Pa machitidwe 16:6-7 Mzimu analetsa Paulo kulalikira m'Asia ndi Bethania. Pa Machitidwe 15:28 "Chinakomera Mzimu Woyera ndi ife" kupanga chiganizo choyenera. Tizindikire kuti Mzimu Woyera ali Wamoyo monga anali atumwi. Pa Machitidwe 5:3-4 Ananiya ananyenga "Mzimu Woyera," komwenso kunali kunyenga "Mulungu."

"Mzimu Woyera, yemwe ali m'chikhalidwe monga Mulungu, amapezeka paliponse m'mabwalo awa." "Mzimu Woyera ali ndi umwini monga ali Mulungu." (Ev 616-617).

Tiyenera kusamalitsa pofotokoza za Mzimu Woyera. Ntchito yake ndikutionetsera Atate ndi Mwana, osati umwini wake, ichi nchifukwa chake lye sakutchuka kwambiri m'zolembera za Mau a Mzimu Wachinenero.

"Okhulupirira asachitenge ngati cha nzeru posatengako mbali pa zomwe zikuchitika chifukwa chakuti sakumvetsetsa mpfundo zina ndi zina za zing'ono zing'ono mofanana ndi momwe anzao ena akuzidziwira. Ngati iwo akugwirizana ndi anzaowo ndi kumvetsetsana pa ziphunzitso zofunikira kwambiri, asataye nthawi kukangana ndi kulekana ndi anzaowo pa zinthu zomwe sakuzimvetsetsa bwino ndi zopindulitsa pang'ono. Kukakamira pa mafunso osapindulitsa, a zinthu zomwe sizikukhuza chipulumutso cha munthu, kumangopitiriza kusokoneza maganizo ndi kuwachotsa ku choonadi ndi ku ziphunzitso zofunikira kwambiri pa chipulumutso. Okhulupirira asamalitse ndi kulingirira mozama za zochitika komanso ziphunzitso zomwe kawiri kawiri sakuzidziwa, kapena sakuzimvetsetsa kuti ziri choonadi ndi kuti zofunika ku chipulumutso chao kuti azidziwe…

"Kusemphana pa ziphunzitso kukamachitika pakati pathu, kumapatsa mpata anthu achikunja kutinena, 'Zidzatitengera nthawi yaitali kuti tikukhulupirireni pokhapokhapo muyambe mwayanjana nokhanokha molingana ndi momwe chimafotokozera choonadi. Anthu osakhulupirira Mulungu amatengerapo mwai wa magawano ndiponso makangano a pakati pa akhristu….'

"Anthu ena amafuna kumachita zinthu mosiyana ndi anzao nthawi zonse,



amakondwera akamabweretsa komanso kulandira ziphunzitso za chilendo ndi zodabwitsa ena, ndipo samasamala monga anayenera kuchitira za kufunikira kwa kulimbikitsa umodzi wa m'chikhulupiriro mu chimango cha chikondi... Tiyenera ife kumakupempha kuunika kochokera kwa Mulungu, komanso, nthawi yokhayokhayo tiyenera kusamalitsa momwe timalandirira bvumbulutso liri lonse lomwe lingadze m'dzina la kuunika kwatsopano. Tiyenera kukhala tcheru kuti, mwina podzinamiza tokha kuti tikufunafuna choonadi chatsopanocho, Satana angakhotetse maganizo athu kuwachotsa pa Khrsistu ndi choonadi chofunikira cha nthawi ino. Ndaonetsedwa kuti ndi cholinga cha mdaniyo kuti atsogolere ndi kusokaneza maganizo kuti akhazikike pa zinthu zomwe ndi zosafunika kapena zosapindulitsa, zinthu zomwe mkati mwake mulibe mabvumbulutso kapena zomwe ndi zosafunikira kwenikweni ku chipulumutso chathu. Chisokonekero chimatheka kudzera m'ziphunzitso za tsopanao zomwe zimatchedwa "choonadi chatsopano," chikhalirecho kufufuzitsa mkati mwa ichi, kuunika kwatsopanoko kumangokhala kukhotetsa zinthu kuposa momwe zinali poyamba, ndi kusokoneza maganizo a anthu ena omwe cholakalaka chao chinali kufunitsitsa umodzi wa chiyeretso cha m'chikhulupiriro....

"Chikhalidwe cha Mzimu Woyera chiri chinsinsi chomwe sichinabvumbulutsidwe poyera, ndipo inu simungathe kuchifotokoza ichi kwa anthu ena chifukwa Ambuye sanachionetsere ichi kwatunthu kwa inu."

[Kodi chimodzi cha zinthu zosafunika pa chipulumutso chingakhale chiyani?] "Chikhalidwe cha Mzimu Woyera ndi chinsinsi chomwe sichinabvumbulutsidwe kotheratu, ndipo nkosatheka kuti inu muchifotokoze momveka kwa anthu ena chifukwa Mulungu sanachibvumbulutsire ichi kwa inu. Mungathe kusonkhanitsa Malemba ambimbiri pamodzi ndikuyesetsa kuikapo maganizo anu olakwika pa awa ndi cholinga chakuti muchimvetsetse chinsinsichi, koma simudzafika pa yankho lokhoza.... Ndi kosafunika kwa inu kuyesetsa kudziwa komanso kutanthauzira chomwe Mzimu Woyera ali.... Pali zinsinsi zina zambiri zomwe ngakhale Ine sindingayesere ndi pang'ono pomwe kufuna kuzimvetsetsa kapena kuzifotokoza; ndi zakuya kwambiri kwa ine ndiponso kwa inu. Zikafika pamenepa kungokhala chete ndi chinthu chokhacho cha mtengo wapatali chomwe tingachichite...

"Malingaliro anu sakukhutitsidwa, choncho... pakutero samalitsani kuti mungalowe mkulakwa kumene ambiri akuchita kale, poganiza kuti mwapeza kuunika kwatsopano, chikhalirecho kuli njira ya tsopano yolowerera mkusayeruzika.... Mungathe kutenga mpfundo zina ndi zina za m'Malembo, kapena kumafufuza m'Bukhu Lopatulika motsogozedwa ndi maganizo anu olakwika, mungathe kudzisonkhanitsira ndime zankhaninkhani ndi kudzinamiza nokha kuti zikutanthauza ichi kapena icho, ndikuitana anzanu kuti atsimikizire maganizo anuwo ngati ndi olondora.... Pamenepa pamakhala choopsya, chifukwa pakutero mumapotoza anthu ambiri kuchoka pa choonadi cha nthawi ino.... Choncho, mbale wanga, ndi zoonadi kuti mtima umalakalaka utamvetsetsa, koma samalitsa ungabweretse chokhumudwitsa pochitenga ngati choonadi chatsopano." (14 MR 175-180).

"Pamenepa pamakhala choopsya chifukwa pakutero mumapotoza anthu ambiri kuchoka pa choonadi cha nthawi ino...."

Ndikukhulupirira kuti malangizo awa akhuza mbali zonse za chiphunzitso cha "kuunika kwatsopano" zomwe tichite nazo m'zolembera ziri m'kabukuka.

## Gawo C: - Umyaya wa Yesu

Ndi umboni wanji womwe tiri nao wotitsimikizira kuti Yesu alibe chiyambi ndipo analipo chilengedwe chisanakhale?

Pa Yohane 1:1-4 tikuwerenga kuti Yesu sanali "kwa Mulungu" kokha, Iye "Ndiye Mulungu." Iye sanali Mulungu chabe, koma analinso Mlengi wa zinthu zonse. Moyo uli wonse unachokera mwa Iye, koma Iye sanalandira moyo kuchokera kwa wina ali yense.

Pa Yohane 8:58 Yesu anati dzina lakuti "INE NDINE" ndi lake. Eksodo 3:14 akutifotokozera kuti dzina losankhika la Mulungu ndi "INE NDINE." Dzina la Mulungu linapatsidwa kwa Mose'li likutsimikizira za umyaya wachikhalire wa Mulungu, womwe Iye anati ndi wakewake... Iye anadzifotokoza kuti amadzikhalira moyo Mwini Yekha... amene maturukidwe ake ndi a kale lomwe, kuyambira nthawi zosayamba." (DA 469-470).

"Ngakhale masamba a mbiri yoyera, pomwe palembedwa machitidwe a Mulungu ndi anthu ake osankhidwa zalembedwa, pali maumboni okwanira a umyaya wa "INE NDINE" Wamkurukuruyo. Kulumikizana konse kwa kumwamba ndi mtundu wakugwa wa anthu kunakhala kukuchitika kudzera mwa Khristu.... Khristu ndi Alefa ndi Omega, Woyamba ndi Wotsiriza." (GAG 43). Chiri chonse chomwe timachiwerenga chokhuza Mulungu m'Chipangano Chakale, tikuwerenga za Khristu. Pa Yesaya 40:28 Mulungu ali "Mulungu wachikhalire," Mlengi wa malekezero a dziko lapansi." Mwa Khristu muli moyo, wachikhalire, wosabwereka, wosalandira." (DA 530). Khristu ali wachikhalire, mwini-moyo wa Iye yekha Mwana wa Mulungu... Iye akutitsimikizira ife kuti sipanakhalepo nthawi imene Iye analekanitsidwa m'chiyanjano ndi Mulungu wamyaya.... Ali wamyaya, Mwana wodzikhalira moyo wachikhalire." (Ev 615). Zisanakhale zonse, Khristu anali ali mmodzi ndi Atate. (BC 1115). Khristu anali chikhalire Mulungu, m'njira iri yonse. Iye anali ndi Mulungu kuyambira nthawi zosayamba." (RH April 5, 1906).

PP 63-64 likutifotokozera ife kuti ndi yekhayo amene ali mmodzi ndi Mulungu amene angathe kutetezera; ndi Mlengi yekha yemwe angapulumutse munthu. Ngati Khristu analandira moyo kuchokera kwa Atate nthawi ina yake m'mbuyomu; ngati moyo wake unali wobwereka kapena kulandira kuchokera kwa Atate; ngati Iye anadalira pa Atate za kukhala kwake; ngati Atate anangomsankha Iye kukhala mmodzi wa Umulungu, ndiye kuti Khristu sanali wodzikhalira moyo mwini yekha; Iye sanali Mulungu m'mjira iri yonse; Sali wamyaya; ndipo Iye sakanatha kupereka nsembe yachitetezero kwa anthu ochimwa ndi kupulumutsa mtundu wa anthu.

Mau akuti, "wobadwa yekha" ndi kumasulira kolakwika. Ahebri 11:17 akutifotokozera kuti Isake anali "mwana wake wayekha" wa Abrahamu. Momveka bwino mauwa akutanthauza wobadwa monga mwa lonjezano, wosafana-ndi-wina-wapayekha, wapaderadera. Machitidwe 13:33 akutiuza kuti Khristu, "anaukitsidwa" kwa akufa.

Ndi zochititsa chidwi kuti Mariya wa ku Agreda, mmodzi wa a sistere a chi-Katolika wokhala ndi masomphenya m'zaka za m'ma 1600 anafotokoza kuti Mau [Khristu] anabadwa mibadwomibadwo yasawerengeka kuchokera kwa Atate. M'mau ena ndiko kuti Khristu anabadwa ku nthawi zosayamba. (The Venerable Mary of Agreda). Izi zikutsimikiza kuti ganizo lakuti Khristu ali ndi chiyambi ndipo anapatsidwa moyo ndi Atate ndi la posachedwapa m'chi-Katolika.

## Gawo D: - Chikhalidwe ndi Zochita Za Atatu'wo

Iyi ndi njira ya momwe nkhani ya Utatu ingathe kumvetsedwera bwino pofuna kuthetsa makangano za chiphunzitsochi. Chikhalidwe cha Utatu wa Umulungu ndi chiphunzitso chosatchuka m'Malemba. Paliponse pamene chiphunzitsochi chalankhulidwa, chimangoonetsa mphamvu zitatu zofanana m'zonse, zoyambira ku nthawi ya myaya, iri yonse ndi cholinga komanso malingaliro osati nkumvetsetsedwa ndi olengedwa onse.

Cholinga chachikuru cha Malemba ndicho kufotokoza ntchito za Umulungu. Ichi chimatheka potsatira mphamvu iri yonse ya Utatu molingana ndi udindo wake kuyambira pa Atate mpaka kwa Mwana mpaka kwa Mzimu Woyera. Umu ndimo Umulungu umafunira olengedwa onse aumvetsetsere. Atate ali mwini ulamuliro wonse; Mwana ali nkhoswe yooneka ndi maso kwa olengedwa onse; Mzimu Woyera ali nkhoswe yosaoneka ya Mulungu kwa olengedwa onse.

Ziwalo za Umulungu ndi zolingana m'chikhalidwe, ndi maulemu ao, koma ndi zosafanana m'ntchito ndi maudindo ao pofuna kufikira olengedwa onse... Khristu akukhuzidwa ndi kumuonetsera Atate. Amatenga udindo wakukhala wachiwiri. Mzimu Woyera nthcito yake ndi kuonetsera onse Atate ndi Mwana. Iye samaoneka ndi maso.

Atate anafika powafotokozera angelo za kusiyana kwa Khristu ndi Lusifara, ngakhale awiriwa anali ndi ntchito zofanana. Ngati Umulungu sunamvetsetsedwe kumwamba, ndi chapafupi kuona chifukwa chimene ife tikulepherera kuumvetsetseranso.

Ntchito ya Khristu ndiyo kuonetsera Atate nthawi zonse. Iye amatenga udindo wakukhala wachiwiri. Mzimu Woyera ntchito yake ndi kuonetsera Atate ndi Mwana. Kawiri kawiri samaoneka ndi maso.

Ziwalo za Umulungu ndi zolingana m'chikhalidwe ndi maulemu ao, koma zosiyana m'ntchito ndi maudindo ao pofuna kufikira olengedwa onse.

## Gawo E: - Mbiri ya a Adventist

Umulungu wasankha kudzibvumbulutsa wokha pang'ono ndi pang'ono kwa anthu. Koma ichi sichinthu chokhacho chofunikira cha zina zonse ku chipulumutso cha mtundu wa anthu.

M'Chipangano Chakale, Khristu anaonetsedwa monga Mau a Mulungu, Mwana wa Mulungu. Mzimu Woyera anaonetsedwa monga Nkhoswe, Mtetezi. Chitsimikizo chinali pa Atatuwo omwe ali mwa Mulungu mmodzi, kuyambira pamwamba kutsika pansi pa udindo ndi ntchito kuchokera pa Atate kufika pa Mwana ndi pa Mzimu Woyera.

A Adventist oyambirira anakhuzidwa ndi ziphunzitso za Chihema ndi masiku 2300, Bukhu Lopatulika, za Miyambo, Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri; iwo sanawerenge ndi kukhuzidwa kwambiri ndi za bvumbulutso lokhuza Utatu.

M'ma 1800 chiphunzitso cha utatu wachikunja chinasakaniza za m'Baibulo, nzeru za umunthu, ndi mpfundo za m'misonkhano ya mpingo m'kati mwake. Ichi chinapangitsa mabungwe a Mgwirizano wa Akhristu, ndi la Amipanduko, kuutenga Utatu kuti unali chiphunzitso cha chi-Katolika ndi chachikunja. Yosefe Bates ndi Yakobo White anali ziwalo za Mgwirizano wa Akhristu. Chifukwa chakuti panthawiyo chiphunzitsochi chimati Atate ndi Mwana ndi olingana, chinakanidwa ndi atsogoleri

athu oyambirira.

Mulungu nayenso analora zinthu zikhale chomwecho mpaka m'ma 1890, pamene mbadwo wotsiriza unakhazikitsidwa.

Ellen White anali ku Australia pamene W. W. Prescott anafika kumeneko. Iye anayamba kulalikira Uthenga Wabwino mwatsopano pokhazikika pa chiphunzitso chakulungamitsidwa mwa chikhulupiriro m'chikhalidwe cha Mulungu (Uthenga wa 1888). Iye anatenga nthawi yaitali akugwira ntchito ndi Ellen White, nafikanso pofuna kudziwa za momwe a Adventist oyambirira anaphunzitsira za umulungu wa Khristu ndi Umulungu wa Utatu. A.G.Daniells anagwirizananso ndi chiphunzitso cha Prescott'cho. Pa nthawi yokhayokhayo Ellen White anali nkulemba Desire of Ages momwe anasiyananso kutheratu ndi a atsogoleri oyambirirawo za umyaya wa Khristu.

M. L. Andreason m'zaka zao zoyambirira zakukhala m'Adventist sanamvetsetse. Pambuyo pake iye anaturukira kuti atsogoleri ena amakaika ngati zolembera za Ellen White zinali "zakezake, zobwerekera, kapena zongopatsidwa." M' 1902 iye ananyamuka ulendo wapadera kupita ku California kukadzifufuzira yekha za zolemberazo, ndipo anapeza kuti zinali zolembedwa ndi dzanja la Ellen White ndithu. Chifukwa cha choonadi ndi chiphunzitso chomveka bwino za Umulungu chomwe chinali m'zolemberazo, chiphunzitso cha chi-Adventist za Utatu chinasinthidwanso kuchoka pa cha atsogoleri oyambirira [pioneers].

Nanga izi zinachitikiranji mochedwa kwambiri mu mbiri ya chi-Adventist? Mulungu anaika ndondomeko yoyenera m'kaperekedwe ka choonadi chake ku mpingo watsopanowu poyamba ndi zofunikira kwambiri kaye. Iye anapereka ntchito yakusindikiza ndi kufalitsa mau ake m'ma 1840, chilinganizo cha mpingo m'ma 1850, uthenga wa za thanzi m'ma 1860 kudzanso kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro m'ma 1880. Iye anagawagawa choonadi chatsopanochi pofuna kusunga umodzi wa mpingo wakewu. Anayamba ndi chizindikiritso cha za khalidwe la Mulungu chomwe chinali chinthu chofunikira kwambiri kuposa kuzindikira chilengedwe chake..

Pano adzanso anthu ena omwe akulimbikitsa zoti tibwerere ku chiphunzitso cha atsogoleri oyambirirawo chokana Utatu. Chochititsa mantha za kubwererako ndi cholinga cha anthu omwe akulimbikitsa zakubwererako. Kodi Ellen White analembadi zonse zimene zafalitsidwa m'dzina lake? Ngati tingapeze china chake m'zolembera zake chotsutsana ndi chiphunzitso chimene iye anachibvomereza kale, ndibwino tisachigwiritse ntchito choterocho. Chingathe kukhala chochokera m'zolembera za iwo ongofuna kutipotoza. Cholinga chao ndikungofuna kusokoneza zolembera zakezo kuti zioneke ngati zolakwika. Izi ziri ntchito za mipingo yachisokonezo ya Babulo. Wina wake anathirirapo ndemanga za zolembera za Ellen White pakunena, "Ellen G. White anauziridwa ndi Mulungu m'zolembera zake zonse, ngati sichoncho ndiye kuti mwina ndi iyeyo analakwitsa ngati asakhale adani a choonadi. Pachifukwa ichi ziri kwa munthu ali yense payekha kusankha kubvomereza zabwino za ziphunzitso zolondorazo kapena maganizo otsutsawo. Apatu zikutanthauza kuti ngakhale a Adventist osakhazikikawo ali ndi ufulu wakusakha ulamuliro wa Mulungu kapena wa munthu.

## Malangizo Otsiriza

Satana sasamala konse za momwe iye amasokeretsera anthu a Mulungu, kaya m'zadziko, kaya pakufunda muuzimu, kapena kudzera m'chinthu cha chilendo chomwe chingakope chidwi cha anthu ndi kuwachotsa mu mpingo wotsala wa Mulungu. Pali yankho limodzi lokha logonjetsera zonsezi m'Baibulo lomwe ndi: kumvera malamulo a Mulungu ndi kukhala ndi chikhulupiriro cha Yesu. Kapenanso kuti kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro. Kuchita ichi si kopepuka kapena kophweka monga kufufuza maina m'mabuku a mpingo, Utatu, maulosi, kapena zikondwerero za chi-Hebri. Kukhala mbali ya anthu 144,000 kudalira pa kudziperaka ndi mtima wonse, kugonjetsa tchimo, ndi kuyenda ndi Mulungu monga anachitira Enoke. Kukhala mu 144,000 kudalira pakukhala ndi khalidwe ngati la Mulungu kuposa kukhala ndi chidziwitso cha za Iye kokha. Mulungu ali wokonzeka kutiphunzitsa pomwe tikulephera. Choncho tiyang'anitsitse bwino umo tiyendera kuti tisapatutsidwe ndi ziphunzitso za "kuwala" kwatsopano, zomwe si zatsopanonso ndiponso siziri kuunika konse.

Dennis Priebe anagwira ntchito ya ubusa zaka 20, ya uphunzitsi zaka 11, ndi zaka 20 yonka aphunzitsa anthu mau a Mulungu m'Amazing Facts. Iye ndi mkazi wake Kay ali ndi mwana mmodzi wa mwamuna, Mateyu. Cholakalaka cha Dennis chachikuru ndicho kukonzetsera anthu za chikhulupiriro chake cha kubwera kwa posachedwa kwa Yesu ku dziko lapansi.

## CHPHUNZITSO CHA SABATA LA MWEZI [LUNAR]

Chenjerani ndi chiphunzitso cha Sabata la mwezi. Ngati ndi koyamba kwa inu kumva za kusunga Sabata loona la Mulungu, nkutheka kuti simunamvepo za "masabata a Mwezi." Koma pangakhalitse, mupezana nao anthu omwe amasunga ndi kuphunzitsa sabata la mwezi'li. Monga momwe Sabata la miyambo la Chikhristu [Sunday] lasokonezera za kusunga Sabata pa tsiku [Saturday] limene Mulungu analipatula, chomwechonso Sabata la Mwezi. Zolembera izi zalembedwa ndi cholinga cholimbikitsa mpingo wa Khristu kusunga Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri monga mwa Malemba ndi kufotokoza mwachindunji chifukwa chimene kuukira Mulungu ndi kusalisunga Sabata loonali kukutchedwera chikunja.

Mosakondera ndi Mosabisapo Kanthu

Monga ndinachitira pakuwerenga ndi kufufuza za "Sabata" la miyambo la "Sunday," pakufufuzanso za Sabata la Mwezi ndinayesetsa kuti ndisakondere ndi pang'ono pomwe, choncho sindinasamale konse ngati kutero kungandipangitse kusinthapo chiri chonse za chikhulupiriro changa. Ndi komwe nkomwe ndine munthu wa ntchito za malonda, amene ndiribe nazo ntchito za chiphunzitso cha Sabata la Mwezi ngakhale chikadakhala kuti ndi choona. Ndiribenso bvuto liri lonse ngati kungakhale kofunika kuti ndisinthe ndi kumapumula pa tsiku lina liri lonse la pa mulungu. Ndiribe mpingo womwe woti ungandifunse chomwe ndi kuchita, sindiri m'bungwe lopangidwa ndi munthu liri lonse. Ndiri ndi ufulu wakuwerenga ndi kuphunzira choonadi ndi kuchigwiritsa ntchito pa moyo wanga popanda chondiletsa.

Ndakhala ndi kuchita misonkhano ya mseri pa nkhaniyi pafupifupi kwa zaka 4 momwe ndalandiramo ndemanga zosachepera 5500 kuchokera kwa anthu ogwirizana ndi kukweza komanso osagwirizana ndi chiphunzitso cha Sabata la Mwezi'li. Sindikulemba monga munthu yemwe sakudziwa chomwe akuchita koma kwa nthawi yaitali ndakhala ndikulingirira mwakuya, kupemphera, ndi kuganiza mozama za nkhaniyi. Koma kufikira lero sindinapeze umboni uli wonse wotsimikizira za kuti Sabata la Mwezi ndi chiphunzitso chobvomerezeka ndi Bukhu Lopatulika. Koma, chotsutsana ndi Bukhu'lo.

## Umboni ndi Chiyani?

Ndapeza kuti pali zinthu zingapo m'maganizo a anthu zomwe amazitenga kukhala "umboni." Kwa anthu ena umboni ndi kulandira chitsimikizo cha pang'ono ngakhale chikhale chopanda maziko okhazikika m'Bukhu Lopatulika, pomwe kwa ena umboni uli chitsimikizo chokhazikika pa maziko okweza chiphunzitso ndiponso chikhulupiriro cha m'choonadi. Choncho chofunika kwa ife chidzikhala kukhazikika pa umboni weniweni ndi wokweza chikhulupiriro chathu m'choonadi osati pa matanthauzidwe a umunthu. Malingana ndi m'mene ndaonera ine, umboni womwe ukugwiritsidwa ntchito "kutsimikizira" za chiphunizitso cha Sabata la Mwezi umadalira pa munthu amene ali m'chiphunzitsochi ndipo anangokhulupirira kuti kuli Sabata la Mwezi, nafotokoza za chiphunzitso chakecho m'njira imene angathere kuti chioneke ngati chobvomerezeka.

Ndapeza kuti kuti wina akhulupirire mu chiphunzitso cha Sabata la Mwezi, afunika kukhazikika pa muyeso wa umboni wokhala (m'matanthauzidwe autambwali ) osati pa "umboni" weniweni wochokera m'Baibulo. Ichi nchifukwa chake, zolembera zonse zokhuza Sabata la Mwezi zangodzadza ndi mau monga, "umboni wotsiriza." Koma kuti munthu achiyeze chinthu chotchedwa "umboni wotsirizacho" amapeza kuti chonenedwa umbonicho si umboni konse ai. Tisamalitse ife kuti ngati munthu angatifikire pogwiritsa ntchito mau monga "umboni wotsiriza," tidzifunse ngati zomwe akupereka monga umbonizo ziri "umbonidi." Ndi chapafupi kwambiri kutengeka chifukwa chakagwiritsidwe ntchito ka mau, choncho nkofunikira ifenso tidzikhala ndi chidziwitso chokwanira chotha kulekanitsa ngati choperekedwacho ndi zotsimikizira zake chiridi "umboni" weniweni.

Tsono ponena za chikatikati chenicheni cha chiphunzitso cha Sabata la Mwezi'chi, tidzifunse "ngati chikugwirizana ndi choonadi cha m'Malemba," kapena ndi chongopeka, chongoganizira, ndi chochita kufunika wina kusankhapo pakati pa "zongoganizira zingapo" osati pa mpfundo zenizeni.

## Kodi Sabata la Mwezi [Lunar] ndi Chiyani?

Sabata la Mwezi silimabvomereza za mulungu wa masiku 7 m'malo mwake limagwiritsa ntchito kuoneka kwa mwezi motsutsana ndi Malemba. Alipo malemba atatu omwe amafotokoza nthawi yomwe mwezi watsopano umaoneka komanso kuthera. Tsono m'malo mosunga Sabata pa tsiku la 7 la mulungu uliwonse, wa masiku 7 mosasokoneza, anthu osunga Sabata la Mwezi'wa amayamba kuwerengera mulungu wa masiku 7 pafupi penipeni pa kuonekera kwa mwezi watsopano. Kawerengedwe ka mweziko kamatsatira malingana ndi tsiku limene mweziwo waonekera osati kawerengedwe ka 30-31 monga timachitira tonsefe.

Nzoonadi, masiku a zikondwerero za Mulungu amawerengedwa pogwiritsa ntchito masiku akuoneka kwa miyezi ina. Kuyambira pamene mwezi waoneka, Paskha limachitika pa tsiku la 14 la mwezi woyamba wa chaka chiri chonse. Koma anthu osunga Sabata la Mwezi amakhulupirira kuti Sabata lao limachitika m'masiku akutiakuti a mwezi uli wonse. Iwo amasankha kusunga Sabata laowo pa masiku a 8th, 15th, 22nd, ndi 29th a mwezi uli wonse ukangooneka. Owerengeka amasunga Sabatalo pa masiku a 7th, 14th, 21st, and 28th a mwezi uli wonse womwe waoneka koma pofuna kumvetsetsa bwino za chiphunzitsochi ife tisankha kufotokoza za awo omwe amasunga Sabatalo pa masiku a 8th, 15th, 22nd ndi 29th. M'munsimu ndi chitsanzo chakuti timvetsetse bwino:

Chifukwa chakuti Sabata la Mwezi silimabvomereza za mulungu wa masiku asanu ndi awiri tikugwiritsa ntchito lerowu, Sabata la Mwezi limatha kukhala pa tsiku liri lonse la pa mulungu. Limadalira kotheratu pa masiku omwe waonekera mwezi. Bvuto lalikuru kwambiri limene anthu osunga Sabata la Mwezi amapezana nalo ndi lakuti pamakhala masiku ena oonjezera pa mwezi uli wonse chomwe chimawalepheretsa kusunga Sabata m'masiku asanu ndi awiri.

Mwezi umayamba ndi ndikutsiriza

ulendo wake pozungulira mosaphonyetsa (mwezi watsopano, gawo lachinai loyamba, mwezi watunthu, gawo lachinai lotsiriza, kukonzekera kuonekanso) pafupifupi masiku 29.5. Popeza nkosatheka kuligawa dziko kukhala theka, zikuthanthauza kuti kuti mwezi uoneke zimautengera masiku 29, pamene miyezi ina imafika mpaka masiku 30.

Tsono zikatero anthu osunga Sabata la Mweziwa amachita chiyani ndi masiku a 1st ndi 30th a mwezi uli wonse? Apa ndi pomwe ambiri amayamba kusiyana. Pamene onse amawatcha masikuwa "Masiku a mwezi watsopano" ena amawasunga monga Masabata oonjezera kutalika kwa tsiku la 29th. Ili ndi bvuto lalikuru ndithu ichi nchifukwa chake pali Malemba ena onena za anthu amene anapitiriza zomangamanga (Eksodo 40) ndi za maulendo (Ezra 7:9) pa tsiku la mwezi watsopano. Komanso, palibe pamene ife tikulamulidwa kuti tidzipumula patsiku looneka mwezi uli wonse kupatula tsiku looneka mwezi wa 7th. Tsiku looneka mwezi wa 7th limakhala la Chikondwerero cha Malipenga. Uwu ndi mwezi umene mwina Bukhu Lopatulika likuufotokoza pa Amosi 8:5 pamene ena a Ayuda sanaloredwa kugulitsa zokolora zao patsiku loyamba la mwezi.

Anthu ena osunga Sabata la Mwezili amangosiya kugwira ntchito za malonda kapena zolembedwa m'masiku amenewa koma amakhala ndi ufulu kuchita ntchito za mtundu wina uli wonse monga kutchetcha udzu, kulima kumunda, kukumba maenje, kumanga nyumba, kuyenda maulendo, ndi kuchita zina zonse za pa nyumba. Ichi chikutanthauza kuti iwo alibe tsiku lenileni lakupuma pa masiku asanu ndi awiri. Amayenera kuyembekezera mpaka masiku asanu ndi anai kuti apumule. Mwachitsanzo, ngati iwo angasunge Sabata pa tsiku la 29th la mwezi, ndi oloredwa kugwira ntchito zosiyanasiyana pa tsiku la 30th la mwezi umenewo ndiponso pa masiku a 1st, 2nd, 3rd, 4th, 5th, 6th, ndi 7th a mwezi wotsatira. Ichi chikutanthauza kuti munthu angathe kugwira ntchito masiku 8 osati 6 omwe Mulungu analamulira, ndikupumula pa la 9th, m'malo mwa la 7th lomwe Mulungu analamulira.

Njira iri yonse anthuwo angatsatire, lamulo la Mulungu lakugwira ntchito masiku asanu ndi limodzi ndi kupumula pa lachisanu ndi chiwiri limaswedwa kumapeto a mwezi uli wonse.

"Malemba a Nyengo Zoikika [Moeddim]" Kodi Akuchitira Umboni Masabata a Mwezi?

Maziko a chiphunzitso cha Sabata la Mwezi akhazikika pa Malemba atatu. Malemba amenewa ndiwo okhulupirira onse a Sabata la Mwezi akhala akuwagwiritsa ntchito m'zolembera zao zopezeka pa intaneti komanso zolembera ndi zowerenga zao zina zoyetsetsa kutchinjiriza chiphunzitsochi. M'modzi wa anthuwo akufotokoza kuti malembawo ndiwo akupanga "mpfundo za mphamvu kwambiri" zotchinjiriza chiphunzitso chao, ndipo anzake akubvomerezana naye.

Tsono popeza malembawo akutengedwa kukhala maziko amphamvu a chiphunzitsochi, tiyeni tiwawerenge ndi kuona ngati alidi ndi mpfundo zoyenera. Lemba loyamba likupezeka m'bukhu la Genesis:

Genesis 1:14 "Ndipo Mulungu anati, Pakhale zounikira pa thambo lakumwamba, zakulekanitsa usana ndi usiku; zikhale zizindikiro ndi nyengo, ndi masiku, ndi zaka;"

Wokhulupirira Sabata la Mwezi aliyense amafotokoza kuti mwezi, pokhala chimodzi cha zounikira mumlengalenga, unapangidwa ukhale chizindikiro cha "nyengo." Liu "nyengo" m'lemba ili limatchedwanso "Moedim" m'chi-Hebri lomwe palibe angatsutse kuti limatanthauza "nyengo zoikika."

Bukhu la Strong likutanthauzira liu'li motere:

4150 mow'ed moade' kapena moled {mo-ade'}; kapena (chachikazi) moweadah (2 Mbiri 8:13) {moaw-daw'} kuchokera 3259; choikidwiratu, kotheratu, mwachitsanzo nthawi kapena nyengo; makamaka, chikondwerero; kuimira chaka; kumasulira kwina, msonkhano (monga woikika ndi cholinga chapadera); mwachindunji msonkhano ngati wa mpingo; mopatsira, malo a msonkhano; ndiponso chizindikiritso ( choikika nthawi za mtsogolo): - chizindikilo, nthawi zoikika, malo a, opatulika) msonkhano chiguru, ( choikika, mwapadera), phwando, (loikika, pomwepo) nyengo, chotsimikizika, sunagoge, (yokonzedwa) nthawi (yoikika).

Pano tiyeni tiwerenge lemba lachiwiri, lomwe ndi chiyambi cha nthawi zoikika za Mulungu kuchokera m'Levitiko 23:

Levitiko 23:1-3: "Ndipo Yehova ananena ndi Mose ndi kuti, Nena ndi ana a Israyeli nuti nao, 'Nyengo <4150> za Yehova, zimene muzilalikira zikhale masonkhano opatulika, ndizo nyengo zanga <4150>. 3 'Masiku asanu ndi limodzi azigwira ntchito; koma lachisanu ndi chiwiri ndilo Sabata lakupumula, msonkhano wopatulika; musamagwira ntchito konse; ndilo Sabata la Yehova m'nyumba zanu zonse.'"

Mau "nyengo zoikika" a m'ndime 2 akutanthauzidwanso "Moedim" m'chi-Hebri. Onaninso kuti Sabata la pa mulungu laikidwanso m'ndandanda wa "nyengo zoikika." Ili ndi lemba lofunikira kwambiri kwa munthu wokhulupirira Sabata la Mwezi. Kwa iwo, likuwatsimikizira kuti mwezi uyenera kuikidwa pa zikonzetsero za Sabata la masiku asanu ndi awiri. Tsono popeza Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri laikidwa monga limodzi la "nyengo zoikika" pamodzi ndi zikondwerero zina zonse monga za Paskha ndi Chikondwerero cha Milungu m'lemba ili patapita nthawi, ndiponso Genesis 1:14 likufotokzа kuti mwezi uli chizindikilo cha "nyengo zoikika," malingaliro a anthu osunga Sabata la Mwezi ndi akuti mwezi nawonso uzigwiritsidwa ntchito pakuchita nazo zilinganizo za Sabata la masiku asanu ndi awiri.

Pano tiyeni tipite kulemba lachitatu ndi lotsiriza lomwe okhulupirira Sabata la Mwezi amaligwiritsanso ntchito monga "maziko" a chiphunzitso chaochi:

Masalmo 104:19 "Anaika mwezi nyengo zake, dzuwa lidziwa polowera pake."

Pano tapezananso ndi liu la chi-Hebri lija "moedim" m'ndime iyi, lotanthauzidwa "nyengo." Kwa okhulupirira Sabata la Mwezi, lembali likuthetsa makangano onse akuti mwezi usamagwiritsidwe ntchito pazikonzetsero za Sabata la masiku asanu ndi awiri, lomwe lirinso mkati mwa "nyengo zoikika."

Ngati wosazama m'chidziwitso zomwe zalembedwa pamwambapa'zi, zingakhale ngati zoona:

1) Kuti mwezi ndi "nyengo yoikika."

2) Kuti Sabata la nthawi zonse likutchedwa "nyengo yoikika" m'Malemba.

3) Kuti pokhala nyengo yoikika mwezi udzigwiritsidwa ntchito pa zikonzetsero za Sabata la pa mulungu.

Ngakhale zinthu ziri choncho, mpfundo zalembedwa pamwambazi sizochokera m'choonadi. Nkofunikira kwambiri kuti ife tikhazikitse chidziwitso chathu pa malangizo a Mulungu, osakhala pa "mau omveka ngati anzeru ndi ongosangalatsa" ochokera pongowerenga Malemba owerengeka chabe nkumadzinamiza kuti tachipeza choonadi.

Mau a Mulungu akuti mpfundo yaikuru SIYAKUTI mwezi uli chimodzi cha "nyengo zoikika." Koma kuti uli chimodzi cha zizindikilo zoonetsera "nyengo zoikika" ZONSE. Nkofunika kwambiri kumvetsetsa za kusiyana kwa mpfundo ziwirizi.

Ngati muli zitsanzo m'Malemba zomwe zikutitsimikizira kuti mwezi suukugwiritsidwa pakawerengedwe ka "nyengo zoikika" monga chizindikilo ndiye kuti mtsutso wa osunga Sabata la Mwezi ndi wopanda pake. Chifukwa? Chifukwa ngati Malemba akutsimikiza akuti mwezi uli chizindikilo cha "nyengo zoikikazo" zikutsimikizira kuti mweziwo ndi wosafunikira kapena suukukhuzidwa m'kakonzekedwe ka Sabata la pa mulungu.

## Pano tiyeni timvenso izi:

Woweruza 20:38 "Koma kunali chizindikilo <4150> choikika pakati pa amuna a Israyeli ndi olalirawo, ndiko chakuti afukitse mtambo wa utsi kumudzi."

M'lemba liri pamwamba'li, liu "chizindikilo" likutanthauza "chisonyezo choikika." "Chizindikilo" ndi chichepetso m'chiwerengero cha liu "zizindikilo." Liu'li likuchokera ku bukhu lotanthauzila mau m'chiwerengero la Strong. Mosakaika konse, popeza chizindikilo choikika chinali kufukiza mtambo wa utsi kuti ukwere kuchokera mu mzinda, tingathe kunena kuti ndi zoonekeratu kuti mwezi sunagwiritsidwe ntchito mu "chisonyezo" ichi. Chodziwika bwino ndi chakuti sitingathe kugwiritsa ntchito mwezi kuyatsira moto.

Pano liu, chizindikilo latanthauzidwa kuti "nthawi yoikika:"

Numeri 28:2-4 "Uza ana a Israyeli, nuti nao, Muzisamalira kubwera nacho kwa Ine chopereka changa, chakudya changa cha nsembe zanga za moto, cha pfungo lokoma, pa nyengo yake yoikika. <4150>' 3 "Ndipo nena nao, Nsembe ya moto imene muzibwera nayo kwa Yehova ndiyi: ana a nkhosa awiri a chaka chimodzi opanda chirema, tsiku ndi tsiku, nsembe yamoto yosalekeza. Mwana wa nkhosa mmodziyo umpereke m'mawa, ndi mwana wa nkhosa winayo umpereke madzulo."

Malemba awa akufotokoza za nsembe ya tsiku ndi tsiku m'kachisi kapena nyumba yokumaniramo. Pamakhala nkhosa ziwiri zomwe zimaperekedwa tsiku liri lonse, imodzi m'mawa ndi ina madzulo. Mulungu akuti, "Muzisamalitsa kubwera kupereka nsembe zanu kwa Ine mu nyengo yoikika <4150>. "Nyengo yoikika" kapena kuti "nthawi" ikutanthauza m'mawa ndi madzulo. Mwezi sukukhuzidwa za kawerengedwe ka m'mawa kapena madzulo, chikhalirecho izi nazonso zikutchedwa "nyengo zoikika." Ichi ndi chitsimikizo cha poyera kuti zina za "nyengo zoikika" za mulungu sizifuna chizindikilo cha mwezi konse.

Ndi zoona ndithu kuti Mulungu anaika mwezi kukhala chizindikilo cha "nyengo zoikika," koma si nyengo zoikika ZONSE za Mulungu zomwe zinafuna mwezi monga momwe amaphunzitsira anthu osunga Sabata la Mwezi. Choncho,zonena zao ZONSE zakuti "nyengo zoikika" zonse za Yehova zimafunika mwezi (chotero Sabata nalonso liyenera kukhuzidwa ndi mweziwo) ndi bodza lenileni.

Pofuna kutsimikizira mpfundoyi, tiyeni tiwerengenso Masalmo 104:19:

Masalmo 104:18-19 "Mapiri atali ndiwo ayenera zinkhoma, pamatanthwe mpothawirapo mbira. Anaika mwezi nyengo zake, dzuwa lidziwa polowera pake."

Ngati titati titsatire chiphunzitso cha anthu osunga Sabata la Mwezi, ndi chodziwikiratu kuti iwo amaonjezerapo maganizo ao pa mau a Mulungu pakunena kuti Mulungu "anaika mwezi pa nyengo zoikika zake ZONSE, choncho nyengo zoikika ZONSE zifunika mwezi m'zochita zao."

Pofuna kutsutsa chiphunzitso chabodzachi, tiyeni tibwerərenso ku Masalmo 104:19. Tiyeni tilingirire kanthawi kochepa za ndime imene tangowerengayi, yomwe ili ndi kalembedwe ka mau mofana ndi a yoyamba ija. Iyo ikuti, "Mapiri atali ndiwo ayenera zinkhoma." Kwa munthu wa Sabata la Mwezi kuti amvetsetse, tiyeni tinene chonchi:

Ngati: Mulungu "anaika mwezi kukhala chizindikilo cha 'nyengo zoikika' ZONSE ndiye kuti 'nyengo zoikika' ZONSE ziyenera kugwiritsa ntchito mwezi."

TSONO (pogwiritsa ntchito nzeru ngati yomweyo): Mulungu anapanganso "mapiri ndiwo zikhalemo zinkhoma ZONSE ndiye kuti zinkhoma ZONSE ziyenera kugwiritsa ntchito mapiri atari.

Ichitu, ndi chiphunzitso chosamveka koma chongoonetsa kupusa kokakamira zinthu zopanda nazo umboni ponena kuti

'nyengo zoikika' ZONSE zifuna mwezi m'zochitika zao.

Chimene tikuwerenga m'Masalmo 104 ndi ndakaturo za chi-Hebri, osati mpfundo zopanda maumboni,ndi mau odziyenereza. Mwinanso, wina angathe kupitiriza kuwerenga mpaka ndime 20 pomwe angamvenso mau akuti, Pamenepo zituruka zirombo ZONSE za m'thengo kunka zikuyendayenda pali ponse kamodzi usiku uli wonse.

Mwachidule, kunena kuti "nyengo zoikika" zonse za Mulungu zifuna mwezi m'zochita zao ndi kunama dzuwa likuswa mtengo. Tanthauzo la mau "nyengo zoikika" m'chi-Hebri ndi lotambalala kwambiri kuposa momwe anthu osunga Sabata la Mwezi amalifotokozera, ndipo ngati wina angayesetse kuti amvetsetse bwino za katanthauzidwe kao za Masalmo 104:19, zingakhale zomvetsa chisoni kufikira pakuti mwana angathe kuseka.

Tiyenera kusamalitsa za ziphunzitso ngati izi. Munthu angathe kungotenga lemba ndi kulitanthauzira mosiyana ndi cholinga chake pongolitanthauzila mwapamwamba pamwamba pofuna kukweza zolinga za chikhulupiriro chake. Chifukwa cha ichi, nkofunika kumamvetsetsa matanthauzo a mau a chi-Hebri, Tifufuze mosatopa za chomwe ndi cholinga cha mau'wo powayerekeza ndi mutu umene akukhuzidwa nao m'Malemba. Tikatere, tanthauzo lenileni la mau'wo lidzakhala poyera.

Tsono funso ndi lakuti, "Ngati malemba atatuwa ndiwo 'akupanga maziko olimba pomwe pakhazikikapo chiphunzitso cha kusunga Sabata la Mwezi, koma m'matanthauzidwe ake mulibe mpfundo zogwira mtima chomwechi, kodi zimenezi zikutionetsera chiyani za mpfundo zofooka za anthu osunga Sabata la Mweziwa?"

Popanda umboni uli wonse wochokera m'Malemba, munthu nkumatiuza kuti mwezi uziikidwamo mu zikonzetsero za Sabata la pa mulungu, onena nakhala anthu osunga Sabata a Mweziwo, osati malemba, si zoona.

## Masabata oikika kodi akunena za Sabata la Mwezi?

Mpfundo yachiwiri ya "mphamvu kwambiri za Sabata la mwezi" imati chokhacho choti Malemba ena akuonetsa kuti Sabata la Mulungu, limatha kuchitika pa tsiku limene Sabata la mwezi limakhala, ndi umboni wokwanira kuti Sabata la mwezinso ndi loona. Sindikuchiona chifukwa chomwe chimaipanga iyi kukhala mpfundo ya mphamvu kwambiri. Chifukwa sikawiri kawiri kuti Masabata osiyanawa amatha kuchitikira pamodzi. Ndikamodzi patapita nthawi yaitali chifukwa masabata a mweziwo amadalira pa kuzungulira kwa mwezi, komwe nthawi zina kumatha kuchitika kawiri pa chaka. Chifukwa chakuti liri lonse la masabatawa linatchulidwa m'Bukhu Lopatulika isakhale nkhani imeneyo.

Kuti chiphunzitso cha Sabata la Mwezi chibvomerezeke, anthu ayenera kukhala ndi umboni wakuti Sabatalo linachitikapo pa tsiku lakuti lakuti motsatizana m'miyezi iwiri kapena yochurukirapo m'zaka zakuti m'mbuyomu. Ichi nchosatheka pochiyerekeza ndi Sabata la pa mulungu. Chomvetsa chisoni za osunga Sabata la mweziwa ndi chakuti, ngakhale ayesetsa, akadali kutali ndi chitsimikizo chokwanira cha chiphunzitso chaocho. Ngati akutsutsabe polimbikira kuti ali nacho chitsimikizo, msachedwe ndilembereni.

Malingana ndi m'mene ndafufuzira ine, pali malo amodzi kapena awiri okha m'Malemba omwe wina angathe kukaikira kuti tsiku la Sabata la Mulungu linachitikapo pa tsiku lakuti la mwezi wakuti.

Lemba loyamba ndi Eksodo 16:1 lomwe likufotokoza za ulendo wa a Israyeli wolowa m'Chipululu cha Sini, pa tsiku la 15th la mwezi wa 2nd kuchokera pamene anaturuka m'dziko la Aigupto.

Eksodo 16:1 "Ndipo anachoka ku Elimu, ndi khamu lonse la ana a Israyeli linalowa m'chipululu cha Sini, tsiku lakhumi ndi chisanu la mwezi wachiwiri ataturuka m'dziko la Aigupto."

Pa tsiku lotsatira lomwe linali la (16 la mweziwo), Mulungu anayamba kuwatumizira iwo manna kuchokera kumwamba ndi kuwauza iwo kuti adziola miyezo iwiri pa tsiku lachisanu ndi chimodzi la pa mulungu lomwe linali la 21st la mweziwo:

Eksodo 16:22-23 "Ndipo kunali tsiku lachisanu ndi chimodzi, anaona mkate, naonjezapo linzake, maomeri awiri pa munthu mmodzi; ndipo akazembe a khamulo anadza nauza Mose. Ndipo ananena nao, Ichi ndi chomwe Yehova analankhula, Mawa ndiko kupuma, Sabata lopatulika la Yehova; chimene muziotcha, otchani, chimene muziphika phikani; ndi chotsala chikukhalireni chosungika kufikira m'mawa."

Pongoganizira kuti m' Eksodo 16 mwina munali masiku ena omwe sakutchulidwa, tsiku likunenedwa'li, linali la Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri lomwe linati likhale pa tsiku la 22nd la mweziwo , koma ili sichitsimikizo chokwanira kuti ife tingachilandire chiphunzitso cha Sabata la Mwezi. Monga ndanenera poyamba, izi zingathe kuchitika nthawi zina kawiri pa chaka.

Kunena mwatchutchutchu, ndime izi zikutsutsaniranatu ndi chiphunzitso cha Sabata la Mwezi. Mulungu anapereka manna kwa masiku asanu ndi limodzi nasiya osapereka mkatewu pa la Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri.

Eksodo 16:24-30 "Ndipo anausunga kufikira m'mawa, monga adalamulira Mose; koma sunanunkha, ndipo sunagwa mphutsi. Ndipo Mose anati, Muudye lero; pakuti lero ndilo Sabata la Yehova; simuupeza lero pabwalo. Muziola uwu masiku asanu ndi limodzi; koma tsiku lachisanu ndi chiwiri ndilo la Sabata, pamenepo padzakhala palibe. Ndipo kunali tsiku la Sabata, kuti anthu ena anaturuka kukaola, koma



sanaupeza. Ndipo Yehova anati kwa Mose, Mukana kusunga zouza zanga ndi malamulo anga kufikira liti? Taonani, popeza Yehova anakupatsani Sabata, chifukwa chake tsiku lachisanu ndi chimodzi alikupatsa inu mkate wofikira masiku awiri; khalani yense m'malo mwake, munthu asaturuke m'malo mwake tsiku lachisanu ndi chiwiri. Ndipo anthu anapumula tsiku lachisanu ndi chiwiri."

Tamvani chomwe Malembawa anena, "Mukana kusunga zouza zanga ndi malamulo anga kufikira liti? Taonani, popeza Yehova anakupatsani Sabata, chifukwa chake tsiku lachisanu ndi chimodzi alikupatsa inu mkate wofikira masiku awiri." Mulungu amawaphunzitsa iwo za tsiku la Sabata kuti ndi liti powapatsa iwo mkate wa masiku awiri pa tsiku lachisanu ndi chimodzi. Anapatsidwa manna mpaka tsiku la 6th ndipo pa la 7th la pa mulungu sanayenera kukaola uwu popeza linali la Sabata.

Ndi chiphunzitso cha Sabata la Mwezi, zoola mkatezi zinali zobvutirapo chifukwa zinayenera kuchitika ku mapeto a mwezi. Kodi Mulungu anapatsapo mkatewu m'miyezo itatu kapena inai kuti a Israyeli athe kusunga masiku a 29th, 30th ndi 1st la mwezi wotsatira? Kapena, kodi iye anagwetsa magawo awiri a manna pa tsiku la 29th la mwezi ndi kuwalora iwo kukaolanso manna pa tsiku la 30th ndi la 1st la mwezi wotsatira omwe anali (masiku a mwezi watsopano)?

Machitidwe a mtundu uwu ali wonse anali otsutsana ndi chiphunzitso chomwe Mulungu amachipereka m'Eksodo 16. Zinafunika Mulungu kupereka magawo anai a manna pa tsiku la 28th kuti mkatewo ukwanire masiku a 28th, 29th, 30th, ndi la 1st, (chifukwa ngati sakanatero anthu akananyamuka kukafunafuna manna!), kapena Iye anayenera kuwapatsa manna wokwanira masiku 7-8 mogwirizana ndi tsiku la 29th lakuoneka kwa mwezi (lomwe likutsutsana ndi chiphunzitso chakuti "masiku asanu ndi limodzi anaola mkate.")

Lemba lachiwiri la m'Malemba lomwe lingakhale ngati likunena za Sabata kuti linakhala tsiku limodzi ndi Sabata la Mwezi ndi lija lonena za mulungu uja Yesu anapachikidwa pa mtanda. Tsiku lapambuyo pakupachikidwa kwakelo zikuoneka kuti linatchedwa la Sabata.

Yohane 19:30-31 "Pamene Yesu tsono adalandira vinyo wosasayo anati, Kwatha; ndipo anawerama mutu, napereka mzimu. Pomwepo Ayuda, popeza panali tsiku lokonzekera, kuti mitembo ingakhale pamtanda tsiku la Sabata, pakuti tsiku lomwelo la Sabata linali lalikuru, anapempha Pilato kuti miyendo yao ithyoledwe, ndipo achotsedwe."

Tonse tikudziwa kuti Yesu anaphedwa pa tsiku la Paskha, lomwe linali la 14th la mwezi woyamba. Ngati timakhulupirira kuti Sabata latchulidwa pamwamba'li ndi la tsiku lachisanu ndi chiwiri la pa mulungu, ndiye kuti linali pa tsiku la 15th la mwezi woyambawo lomwe linali la Sabata.

Chomwe ndinganene ndi chakuti njira imene osunga Sabata la Mwezi aitsata pokhazikitsa chiphunzitso chao ndi ya pansi kwambiri, makamaka pokhala yokhuzana ndi kasungidwe ka lamulo lofunikira kwambiri lachinai! Kusamalira momwe timalankhulira, kuphunzitsira kapena kulembera mau athu ngati kuti ali "choonadi" ndi chinthu chofunikira kwambiri. Ngati munthu akulankhula kapena kulemba mpfundo, ndi bwino kupereka umboni wa mauwo. Ngakhale osunga Sabata la Mwezi akuti ali ndi "mpfundo za mphamvu kwambiri" koma mulibe mphamvu iriyonse mu izi.

## Malemba omwe akufotokoza za Sabata Loona

Bvuto lalikuru limene Sabata la Mwezi likupezana nalo ndi la kusowa kwa umboni wa chiphunzitsochi kuchokera m'Malemba. Zikadakhala bwino ngati pakadapezeka ngakhale Malemba awiri okha ochitira umboni kapena kutsutsana za Sabata la Mwezi'lo ndi Sabata loona omwe akadachititsa owawerenga kuyesetsa kupeza chifukwa chomwe akutsutsanirana. Koma pakunena za Sabata loona la pa mulungu palibe lemba liri lonse lotsutsa koma kuchitira umboni.

Sindikukhulupirira ngati pangapezeke wowerenga za lamulo la Sabata m'Levitiko 23, kapena m'Eksodo 20 kapena za chilengedwe, yemwe angapeze lemba lochitira umboni chiphunzitso cha "Sabata la Mwezi." Palibe lamulo liri lonse pali ponse m'Malemba lomwe limati:

"Pa tsiku looneka mwezi wina uli wonse, masiku asanu ndi limodzi mukhale mutatsiriza ntchito yanu yonse, ndipo tsiku lachisanu ndi chiwiri ndi la Ambuye Mulungu wanu. Kapena kuti mugwire ndi kumaliza ntchito yanu kwa milungu inai. Kenaka kutengera ndi pamene ungaonekere mwezi watsopano, musagwire ntchito zanu za malonda, kapena ntchito iri yonse yolipidwa kwa masiku 1 kapena 2. Kenaka mudzayambenso mulungu wina momwe kwa 'masiku asanu ndi limodzi mudzagwira

ndi kumariza ntchito yanu, ndipo lachisanu ndi chiwiri lidzakhala Sabata lakupumula, lopatulika."

Ndi zachidziwikire, Mulungu sanalankhulepo mau otere, koma chikhalirecho ili ndi lamulo lomwe osunga Sabata la Mwezi amalisunga ndi kulitsatira. Choncho liri lamulo osati lochokera kwa wina aliyense koma lopangidwa ndi anthu chifukwa silikupezeka pali ponse m'Malemba.

## Tiyeni tikumbukire kuti Mulungu anati:

Deuteronomo 12:32 "Chiri chonse ndikuuzani, muchisamalire kuchichita; musamaonjezako, kapena kuchepsako."

Kusasamalira kwa malangizo oterewa , kwadzetsa chipambano cha chiphunzitso chotsogolera kuchionongeko cha Sabata la Mwezi. Langizo ili likutionetsa kuti nthawi zambiri ife timalakwa pomaganiza kuti Mulungu amationa ngati ndife ozindikila, ndipo tidzapitirira kukhala otere, choncho sitisowa kutsutsidwa pa zomwe timachita.

Koma… Ngati Mulungu akuyembekezera munthu kugwira ndi kumaliza ntchito yake masiku asanu ndi limodzi kenaka nkusunga Sabata pa tsiku lachisanu ndi chiwiri osati moduladula koma mwa ndondomeko yolukana bwino, chikhale chopepuka kubvomereza kuti Iye ayenera tsono kumatilangiza za momwe tigwirire ntchito zathu m'masiku asanu ndi limodzi ndi kupumula pa la chisanu ndi chiwiri – pasakhalenso chiphunzitso china kuposa chimenechi.

## Ndipo izi ndi zomwe Mulungu anazilankhuladi:

Eksodo 20:9-10 "Masiku asanu ndi limodzi uzigwira, ndi kumariza ntchito zako zonse; koma tsiku lachisanu ndi chiwir ndilo Sabata la Yehova Mulungu wako."

Eksodo 23:12a "Uzichita ntchito yako masiku asanu ndi limodzi, koma tsiku lachisanu ndi chiwiri uzipumula."

Eksodo 31:17 "Ndicho chizindikilo chosatha pakati pa Ine ndi ana a Israyeli; pakuti Yehova analenga zam'mwamba ndi dziko lapansi masiku asanu ndi limodzi, napumula tsiku la chisanu ndi chiwiri, naonanso mphamvu."

Eksodo 34:21 "Masiku asanu ndi limodzi uzigwira ntchito, koma lachisanu ndi chiwiri uzipumula."

Eksodo 35:2 "Masiku asanu ndi limodzi azigwira ntchito, koma tsiku lachisanu ndi chiwiri muliyese lopatulika, Sabata lakupuma la Yehova."

Deuteronomo 5:13-14 "Masiku asanu ndi limodzi uzigwiritsa ntchito, ndi kuchita ntchito zako zonse; koma tsiku lachisanu ndi chiwiri ndilo Sabata la Yehova Mulungu wako."

Ngati tingamvere ndi kutsatira zonse zimene Malemba akunena, popanda kuonjezera kapena kuchotsapo zina ziri zonse mwa umunthu wathu, tidzazindikira kuti Sabata limayenera kuchitika mosadukanadukana, koma monga amayendera masiku a pa mulungu. Palibenso katanthauzidwe kena ka mau awa. Masiku asanu ndi limodzi uzigwira ndi kumaliza ntchito zako zonse ndi kupumula tsiku la chisanu ndi chiwri.

Tikafuna ife kumvetsetsa momwe kayendedwe ka masiku a pa mulungu kaliri, tibwerere kuchiyambi ku chilengdwe tiwerengenso za Sabata lomwe Mulungu analikhazikitsa.

Monga tikudziwira, Genesis 1 akufotokoza mwakuya za masiku asanu ndi limodzi omwe Mulungu anawagwiriramo ntchito polenga miyamba ndi dziko lapansi. Liri lonse la masiku amenewa linapangidwa ndi "madzulo ndi m'mawa [usiku ndi usana]. Mulungu anati madzulo ali onse ndi m'mawa wake zipange liri lonse la masiku a pa mulungu.

Pamene tsiku lachisanu ndi chiwiri linalengdwa m'Genesis 2, Mulungu akuti anapumula m'limenelo kuchokera ku ntchito yake yakulenga, naliyeretsa ndi kulidatitsa.

Genesis 2:1-3 "Ndipo zinatha kupangidwa zakumwamba ndi dziko lapansi ndi khamu lao lonse. Tsiku lachisanu ndi chiwiri Mulungu anamariza ntchito yonse anaipanga; ndipo anapuma tsiku lachisanu ndi chiwiri ku ntchito yake yonse. Mulungu ndipo anadalitsa tsiku lachisanu ndi chiwiri, naliyeretsa limenelo: chifukwa limenelo adapuma ku ntchito yake yonse imene Mulungu anailenga ndi kupanga."

## Pambuyo panthawi, popereka Malamulo Khumi, Mulungu anati:

Eksodo 20:8-11 "Uzikumbukira tsiku la Sabata, likhale lopatulika. Masiku asanu ndi limodzi uzigwira, ndi kumaliza ntchito zako zonse; koma tsiku lachisanu ndi chiwiri ndilo Sabata la Yehova Mulungu wako; usagwire ntchito iri yonse, kapena iwe wekha, kapena mwana wako wamwamuna, kapena mwanawako wamkazi, kapena wantchito wako wamwamuna, kapena wantchito wako wamkazi, kapena nyama zako, kapena mlendo amene ali m'mudzi mwako; chifukwa masiku asanu ndi limodzi Yehova adamariza zakumwamba ndi zapansi, ndi nyanja ndi zinthu zonse ziri m'menemo, napumula tsiku lachisanu ndi chiwiri; chifukwa chake Yehova anadalitsa tsiku la Sabata likhale kuti lopatulika."

Tsono, tiyeni titchere khutu ndi kumvetsetsa chomwe Mulungu akulankhula. Iye anadalitsa ndi kuyeretsa tsiku limodzi. Iye akulitchula ili "la Sabata" nalitchanso "la chi 7th."

## Talingirirani pa ichi mozama:

Chokhacho chakuti Mulungu anadalitsa ndi kuyeretsa tsiku loikika… zikutsimikizira za chikhazikitso cha tsikuli ku nthawi zonse. Ngati chikhazikitso (choikikacho) chitasokonezedwa chifukwa cha kusintha sintha masiku, ndiye kuti tsiku loikika mwapaderalo (la chi 7th) silingazindikirikenso!

Mulungu akadafuna kuyeretsa ndi kudalitsa masiku ena angapo a pa mwezi monga a chi 8th, 15th, 22nd, ndi 29th , akadanena motsimikiza kuti wadalitsa mwapadera masiku akuti akuti a mwezi. M'mau ena kudalitsa ndi kupatulidwako kukadachitika pa masiku angapo akuoneka kwa mwezi, osati pa tsiku limodzi la chi 7th la pa mulungu. Chinanso ndi chakuti, chokhacho chakuti pali tsiku limodzi lomwe Iye analitcha la Sabata, zikutsimikizira kuti munthu sangasokoneze za chilengedwe cha masiku a pa mulungu.

Tikafuna kutsimikizitsa mpfundoyi kuposera apa, tiyeni tibwerere kuchiyambi ndikutengera chitsanzo chathu kuchokera pa Adamu.

Mulungu anali atangolenga miyamba ndi dziko lapansi m'masiku asanu ndi limodzi Sabata linali litagoyeretsedwa ndi kukhazikitsidwa. Chinthu chiri chonse chinali changwiro ndi chabwino ndithu.

Chinachitika? Tsiku lotsatira linali lakuti kugwira ntchito ya m'munda kukufika pa mapeto ndipo lamulo la Mulungu lifunika likwanitsidwe. Tikanakhala Adamu, tikanachita chiyani poona madzulo ndi m'mawa asanu ndi amodzi atapita? Chodziwika bwino ndichakuti tikanapumula pa tsiku lachisanu ndi chiwiri, tsiku lopatulidwa mwapadera lomwe Mulungu analamulira kuti lizisungidwa loyera.

Kenaka? Afikanso madzulo ndi m'mawa ena oonjezera tikanachita chiyaninso? Mosakaika tikananyamuka ndi kugwiranso ntchito m'madzulo ndi m'mawa oonjezerawo ndipo monga tinachitira poyamba tikanapumulanso pa tsiku lachisanu ndi chiwiri. Kayendedwe mozungulira ka masiku a pa mulungu monga ali lero, kanayambira nthawi yomwe Mulungu anapumula pa tsiku lachisanu ndi chiwiri loyambalo nalamulira munthu kuchita chimodzimodzi. Ichi ndi chinthu chosachita kufuna kufunsa kuti wina achimvetsetse.

Taganizirani ngati Mulungu akanakhazikitsa Sabata la Mwezi kuyambira pa chilengedwe. Kodi pambuyo pa milungu 3 kuchokera pomwe panachitika kusunga kwa mulungu wa masiku-7 woyambirira ndi pakutha kwa madzulo ndi m'mawa oonjezera, kusunga kwa tsiku lopatulidwa mwapadera lomwe Mulungu analitcha la Sabata, kukanalondozekabe? Sizikanatheka kupumulabe pa tsiku lopatulidwa ndi kuyeretsedwa mwapaderali.

Ndiye? Apa ndi pomwe ngakhale anthu osunga Sabata la kuoneka kwa miyezi amasiyananso okhaokha . Ena amati, akanakhala Adamu akadapumula pa tsiku lachisanu ndi chitatu, kapena lachisanu ndi chinai ngati mwezi ungakhale usanaonekebe. Chifukwa chiyani chisokonekero chotere? Zonsezi ndi chifukwa chotsutsana ndi zomwe Mulungu anakhazikitsa pa chilengedwe. Kungotero kokhako ndi njira yosokonezera kusunga kwa "Sabata" la tsiku loyeretsedwa mwapadera, la chisanu ndi chiwiri. Kubvomereza chikhazikitso cha kawerengedwe kosokonekera ka masiku kotero ndi njira imodzi yosokonezeranso kasungidwe koyenera ka Sabata la tsiku lapadera lokhalo lomwe Mulungu analiyeretsa – tsiku la chi-7th!

Ena a anthu osunga Sabata la masiku akuoneka kwa mweziwa amati akadakhala Adamu akadangodziletsa kuchita ntchito za malonda ndiponso/kapena zolipidwa ndalama pa tsiku la chisanu ndi chitatu ndi la chisanu ndi chinai. Koma mu nthawi ya Adamu panalibe munthu aliyense amene amagula kapena kugulitsa, ndiponso panalibe aliyense yemwe akanamlipira Adamu pa ntchito yomwe amaichita. Apa anthuwa akungotanthauza kuti ngakhale mu tsiku la mpumulo, Sabata, Adamu akanapitirizabe ntchito yake m'munda wa Edeni pa tsiku lotsatira la pa mulunguli la 7 mpaka la 8, kenaka nkupumula pa la chisanu ndi chinai. Koma chokhacho chakuti Adamu akanapitiriza masiku ake ogwirira ntchito m'mundamo mpaka la 7 kapena la 8 zikutsutsana ndi chikhazikitso chomwe Mulungu anachiika m'Genesis. Kudali kosatheka Adamu kulisiya tsiku la chisanu ndi chiwiri kudutsa chikhalirecho ali ndi chidziwitso chokwanira za kasungidwe koyenera ka Sabata.

Choonadi ndi chakuti, Mulungu sanapumule masiku awiri kapena kwa masiku atatu. Iye sanalamulire mpumulo wa theka wa tsiku limodzi kapena masiku awiri m'la Sabata la 4th la mwezi. Lamulo lotero ndi longopangidwa ndi munthu. Mulungu anayeretsa mwapadera tsiku limodzi, ndipo ndi limodzi lomwelo. Iye anagwira ntchito masiku asanu ndi limodzi napumula pa tsiku lachisanu ndi chiwiri. Ndi ndondomeko yake yomweyi imene ife tiyenera kuitsatira pakunena za kasungidwe ka Sabata loyera, monga Iye anatilamulira:

Eksodo 20:11 "chifukwa masiku asanu ndi limodzi Yehova damariza zakumwamba ndi zapansi, nyanja ndi zinthu zonse ziri m'menemo, napumula tsiku lachisanu ndi chiwiri; chifukwa chake Yehova anadalitsa tsiku la Sabata kuti likhale lopatulika."

Lemba likuti "Yehova anadalitsa tsiku lachisanu ndi chiwiri ndi kuliyeretsa." Tamvani silikunena kuti "Mulungu anadalitsa tsiku lachisanu ndi chiwiri, nthawi ina nadalitsa ndi kuyeretsanso lachisanu ndi chitatu kapena lachisanu ndi chinai, kutengera pomwe waonekera mwezi watsopano ai.

Pali tsiku limodzi lokha lomwe Mulungu analiyeretsa, ili ndi lachisanu ndi chiwiri la pa mulungu. Palibe chiri chonse chonena za tsiku la chisanu ndi chitatu kapena la chisanu ndi chinai la pa mulungu. Ngati pangakhalepo masiku oterowo, ndiye kuti chikhazikitsidwe chonse cha pa chilengedwe ndi chosokonekera. Ndipo Sabata siliyenera kuchitika m'tsiku limodzi, koma kuyambira pa limodzi, awiri kapenanso atatu – kutero komwe kungakhale kuthetseratu kwa chikhazikitso cha chiyero cha tsiku limodzilo.

Tsono pakubvomereza za chisokonezo achibweretsachi, ena a anthu osunga Sabata la masiku akuoneka kwa mwezi'wa ayamba kuwatcha masiku otsala a kumapeto kwa mwezi kuti ndi "masiku opanda ntchito." Ndi mau awa

iwo akutanthauza kuti, masiku amenewo si masiku konse. Sakuwerengedwa, ndipo kulibe awa. Ife timati alankhulenji; ndi pake iwo kulankhula choncho.

Kudzera m'zolembedwa za m'Genesis 1 tikudziwa bwino lomwe kuti tsiku likupangidwa ndi madzulo ndi m'mawa. Ndipo masiku onse akumapeto kwa miyezi yomwe Mulungu anailenga liri lonse liri ndi madzulo ndi m'mawa, izi ziri choncho ngakhale wina ayesetse kuchikana choonadi ichi. "Madzulo ndi m'mawa" zokwanira masiku awiri kapena atatu zikadutsa zimapanga "masiku basi." Choncho nkosatheka ife kubvibviniza mitu yathu mu mchenga ndi kunamizira ngati masiku'wo kulibe chifukwa chakuti munthu wina akufuna kupitiriza kumakhulupirira zomwe moyo wake wasankha kusokeretsedwa nazo.

Choonadi chake ndi chakuti, ganizo lakuti mulungu ungapitirire mpaka masiku 8 kapena 9 ndi la chilendo m'Malemba. Ndipo kunena mwachindunji, uku ndi kutsutsana ndi Malembawo kotheratu. M'chi-Hebri, mau zisanu ndi ziwiri ndi liu lomwe limatanthauza "mulungu" onse akuchokera ku verebu la chi-Hebri lomwe likutanthauza chiwerengero "zisanu ndi ziwiri."

## A BELL ATSUTSA ZA MASIKU A ZIKONDWERERO

Ndinakopedwa kuyamba kukhulupirira za masiku a zikondwerero ndi a Judy Justice m'chaka cha 1988. Chidali chinthu chokondweretsa ndi chochititsa chidwi kwambiri. Ndinaganiza kuti ichi chinali chiyambi chakuti ndizindikira zinthu zambiri ndipo ndinali wokonzeka kuyamba kusunga zikondwererozo.

Koyambirira kweni kweni panalibe kutchulapo za m'chitidwe uli wonse wa chi-Yuda wokhuzana ndi kasungidwe ka zikondwererozi. Sindinauzidwe za kabvalidwe kophimba kumutu, kuliza nyanga ya nkhosa, kapena kugwiritsa ntchito maina akuti akuti a Yesu ndiponso Mulungu Atate. Ndikuganiza kuti zikanakhala choncho, ndikanaziona zonse kukhala za chilendo ndipo ndikanakana kulowa mu mchitidwewu wosokeretsawu pachiyambi pomwepo.

Mosanama ndinakhutitsidwa ndi kumva kukoma mu mtima mwanga komanso kunyadira kuti ndinazindikira chinthu china chatsopano chomwe ndinali wokonzeka kuchigawana ndi anthu ena. Koma pamene ndinayesera kulankhulapo koyamba za kusunga masiku a zikondwererowo, ndikukumbukira kuti mau anga sanalandiridwe monga ndimayembekezera. Mnzanga amene anatsagana nane ku misonkhano yomwe anachititsa a Judy Justice, nakopekanso kuyamba kusunga zikondwererozo, tinakhumudwira limodzi za chiphunzitsochi chifukwa sitinayembekezere kuona momwe zinthu zinalimo. Chifukwa poyamba polowa tinkaona ngati kuti anthu omwe sanalandire ndi kukhulupirira chiphunzitsochi anali achikunja ndi osatembenuka.

Anthu ambiri, akamaphunzitsidwa chiphunzitso chachilendo pa moyo wao wa chikhristu, ndipo akatsimikiza mtima kuchilandira, amadana ndi omwe samagwirizana ndi chiphunzitsicho m'malo mowafunsa chifukwa chimene samagwirizanira nacho. Iwo amakondana ndi munthu wowaphunzitsayo ndiponso onse omwe akubvomerezana nao. Kwa ma-Adventist, ichi sichachilendo, ambiri akhala akumva za anthu amene akuphunzitsidwa za Sabata kwa nthawi yoyamba kuti ngati sakufuna kukhulupirira Sabatalo amadana ndi wowaphunzitsa ndi ena onse akulisunga ndi kupita kwa abusa a mipingo yao omwe amadziwilatu kuti akawauza kuti Sabatalo kulibe chifukwa malamulo onse a Mulungu anathera pa mtanda. Ma-Adventist ena anayamba achitapo zoterozo. Koma chofunika kuchidziwa ndi chakuti, ndi bwino, munthu akapezana ndi chiphunzitso chachilendo asadane ndi womphunzitsa. Kwa mbusa wake kapena mkhristu yemwe ndi wokhazikika m'chidziwitso ndi mu uzimu wa mu mpingo wake apite ndi kuwafunsa ngati chomwe akuphunzitsidwacho chiri choona kapena ai. Umu ndi momwe ine ndinachitiranso, sindinapite kwa aliyense amene ndinadziwa kuti akatsutsana ndi chiphunzitso cha zikondwererochi. Choonadi, ngakhale chiponderezedwe chimafukuka nkukhalabe poyera.

Pamene tinasunga tsiku la chikondwerero chathu choyamba, sitinamvetsetse chomwe tinayenera kuchichita. Tinaganiza kuti tidzikhala tikukomana kagulu kakang'ono ka okhawo amene tinakondweretsedwa kapena achidwi ndi ofuna kuphunzira phunziro la chilendo kuchokera m'Bukhu Lopatulika ndi m"Mau a Mzimu Wachinenero. Tinkaziwa bwino lomwe kuti kunali kosafunika kuti tizipereka nsembe za nyama zophera. Mbali imeneyi inachitika kale. Ndikakumbukira bwino tinangosunga masiku azikondwerero ziwiri kenaka aliyense anayamba kutangwanika kenaka mnzanga ndinalowa naye limodzi uja anadwala kansa namwalira. Ndinakhala ndekha nkumasunga masiku a zikondwererowo pakhomo panga. Kenaka ndinasiya chifukwa chotangwanika ndi za m'banja langa lomwe linali kukula. Koma m'maganizo mwanga ndinakhala ndikuganizirabe ndi kudzifunsa ngati kunali kofunikira kapena ai, kupitiriza kusunga masiku a zikondwerero'wa.

Pambuyo pa pafupifupi zaka 3 kapena 4 ndinasintha malo okhala pochoka ku California Wakumwera kukakhala ku Oregon, koma ndinapitirira kukaikirabe ngati kunali koyenera kupitiriza kumasunga zikondwererozo. Ndinkatsutsika m'moyo mwanga ndikamawerenga kuchokera m'Mau a Mzimu Wachinenero ndi Bukhu Lopatulika kuti sikunali kofunikira kutero. Pa nthawiyi sindinali ndi chilakolako chofuna kuzindikira zinthu zatsopano zokha. Koma ndinafunitsitsa ndi mtima wanga wonse kuzindikira choonadi chomwe chinditsogolere kukondweretsa Mulungu. Ndinachita chimene anthu ena anakhala akunena kuti anachitapo. Ndinapemphera kuti Mulungu andithandize. Ndinapemphera pemphero ili mwachinsinsi mu mtima mwanga, kuti Satana asazindikire yankho la pemphero langalo. Ndinampempha Mulungu kuti alore kuti ndidzadwale pa tsiku la chikondwerero, kuti ndisadzapite ku ntchito. Koma sizinatheke. Pambuyo pake munthu wina amene anandiuza kuti Mulungu anayankha pemphero lake, anandifotokozera kuti Mulungu sanayankhe pemphero langa chifukwa linali lotdzetsa kupweteka pa moyo wanga. Komatu Mulungu yemweyo anayankhatu pemphero la Ellen White lakuti adzidwala nthawi iri yonse yomwe iye anayamba kudzikweza.

Ndinapempheranso pambuyo pa loyambalo. Mulungu sanayankhebe. Kenaka ndinatsimikizika mtima kuti zokhuza chiphunzitso Mulungu samayankha mapemphero a umunthu. Chonse chomwe tipempha Iye chidzikhala ndi maziko a m'Bukhu Lopatulika. Koma anthu ochuruka amachita monga ndinachitira ine'mu – akafuna kuti Mulungu awachitire kanthu koti kawalepheretse kupita ku ntchito zolembedwa ndi cholinga chakuti asunge masiku a zikondwerero. Zikatero amapatsidwa tchuti pa tsiku lachikondwerero'lo. Mosakaika konse, Satana amachizindikira ichi ndipo ndi iye amayankha.

Pano tsono ndifotokoze zina za zinthu zomwe ndinaziphunzira ndi zinandizindikiritsa kuti masiku a zikondwerero alibe ntchito mu nthawi yathu ino. Ndinayamba ndi kukaikira zonena za anthu ena osunga zikondwererozo. Iwo amafotokoza kuti zikondwerero zikadagwirabe ntchito kuyambira pomwe zinakhazikitsidwa pachilengdwe, chifukwa Genesis limagwiritsa ntchito liu "mo'ed" pa Genesis 1:14, pamene likufotokoza kuti pakhale zounikira pa thambo zikhale zizindikilo za "nyengo." Iwo amafotokozanso kuti malonjezano apadera amene Mulungu anapangana kwa Abrahamu anakhazikika pa masiku a zikondwerero, chifukwa panagwiritsidwanso liu "mo'ed". Kuchokera apa ndinayamba kuzindikira kuti zambiri zomwe akunenazo zinali zongopeka. Palibe pena pali ponse pomwe panenedwa za masiku a zikondwerero m'mapangano omwe Mulungu anapangana ndi Abrahamu.

Monga lafotokozedwa kale, liu "mo'ed" limatanthauzanso, zimene Bukhu Lopatulika la King James Version limati (nyengo). Ngakhale liu'li likutanthauza masiku a zikondwerero m'Genesis 1:14, sizoona kuti zikondwerero za zinsembezo zinayamba pachiyambi pachilengdwe. Mu ndime yomweyi, zizindikilo monga mwezi zinkagwiritsidwa mtchito younikira m'thambo lakumwamba. Kunali kosatheka kuti zikondwerero ndi masiku akezi zigwiritsidwe ntchito kuyambira pa chilengwedwe chifukwa kunalibe uchimo kupatula pambuyo pa kulowa uchimo m'dziko lapansi pomwe zinayamba kugwiritsidwa ntchito monga anamkungwi olozera ochimwa ku nsembe ya chipulumutso. Uchimo usanalowe m'dziko, Mulungu analankhula mwachindunji ndi munthu mosafunanso zinsembe ndi masiku azikondwerero. Zakuti Abrahamu anasungapo masiku a zikondwerero mulibe umboni m'Malemba ngakhale m'Mau a Mzimu Wachinenero. Ndi zongopeka.

Pomwe nthawi inakhala ikupita ndipo ndinakhala ndikuwerenga Malemba, ndinaturukira mpfundo zina zazing'onozing'ono ndi zofunikira zomwe zinanditsimikizira kuti zikondwerero za zinsembe sizofunikanso kusungidwa. Nditawerenga m'bukhu la Yohane, ndinapeza kuti kambiri iye anazitcha izi "zikondwerero za Ayuda." Ichi chinanditsimikizira kuti, ngati zikondwererozi zikanakhala zofunika kusungidwabe, iye akanangozitcha "zikondwerero" osaonjezera kuti za Chiyuda.

Ndinawerenganso mau omwe Paulo analankhula, akuti, "Pakuti nthawi zonse mukadya mkate uwu ndi kumwera chikho, mulalikira imfa ya Ambuye kufikira akadza Iye." 1 Akorinto 11:26. Iye sanati "Mukadya mkate uwu ndi kumwera chikho pa Tsiku la Paskha chaka chiri chonse." Zikufotokozedwanso bwino kuti Paulo sanatchule za dzina la tsiku lakutilakuti kuti ndi lomwe anthu adzichita chilinganizo cha mgonero. Ellen White nayenso akufotokoza momveka bwino za utumiki wa mgonero womwe unalowa m'malo mwa utumiki wa Chikondwerero cha Paskha: "Pamene Iye anali pa Paskha ndi ophunzira ake, anakhazikitsa m'malo mwa Paskhalo utumiki womwe uli chikumbutso cha nsembe yake yaikuru. Uku kunali kuchotseratu kwa myaya kwa Chikondwerero cha Paskha ku mtundu wonse wa Ayuda. Utumiki wa mgonero womwe Khristu anaukhazikitsa unakhala wakuti usungidwe ndi otsatira Ake m'maiko onse ndiponso kumibadwo yonse." Counsels for the church, 298.

Mnzanga wina yemwe akusungabe zikondwerero za zinsembe anandiuza kuti ife tiyenera kulumikizidwa ku mpesa, womwe ndi mtundu wa Israyeli. Koma ine ndinaganiza kuti kudzilumikiza ku mtundu womwe wakanidwa ndi Mulungu ndiko kuchita chigololo cha uzimu. Bukhu Lopatulika likufotokoza za kufunikira kwa munthu kulumikizidwa ndi Mulungu m' Aroma 11, ndipo Paulo akutsimikizira za a Israyeli okhala otero ku thupi kuti adzilumikize ku Mpesa Woona, Yesu Khristu.

Mu ulaliki wa Emiliano Richards, akufotokoza kuti sitikufunikanso ife kupereka nsembe ya nkhosa, chifukwa Khristu ndiye Nkhosa ya Mulungu; sitikufunanso mkuru wa nsembe wa dziko lapansi chifukwa Khristu ndiye Mkuruwansembe wathu; ndipo sitifunanso kachisi wa pansi pano chifukwa Khristu ndiye Mtumiki wa Kachisi Wakumwamba. Mlalikiyu anafunsa funso lakuti, "Ngati

Khristu ali chikwaniritso cha zikondwerero za zinsembe, ife tisowanso kuzichita izi, kodi ichi sichingatitsimikizire kuti Iye anakwaniritsa izi ndipo ife sitifunikanso kuzisunga, monga sichitsimikizo chokwanira chotizindikiritsa kuti Iye anakwaniritsa zikondwerero ndi masiku zimachitikamo zomwe zinali m'thunzi wa zinthu zinali nkudzazo kuimira Khristu Mwini, choncho sitiyeneranso kukhala mu izi?"

Richards akufotokoza momwe Khristu wakaniritsira chiri chonse cha zikondwereozo:

Paskha: Chinali chikumbutso cha nthawi imene a Israyeli anaturutsidwa mu ukapolo wa Aigupto. Nkhosa ya mphongo inaperekedwa nsembe. Yesu Mwanawankhosa wa Mulungu anakwaniritsa chikondwererochi potipulumutsa mtundu wonse wa anthu kuchokera mu ukapolo wa uchimo. Yohane 1:29 – "M'mawa mwake anaona Yesu alikudza kwa iye, nanena, Onani Mwanawankhosa wa Mulungu amene achotsa tchimo lake la dziko lapansi!" Yesu anafa pa Paskha ndendende nthawi yomwe imaperekedwera nsembe yachikondwerero cha Paskha, kukwaniritsa cholinga cha nsembe yomwe ichi chimaimira. "Pamenepo anamtenga Yesu kuchokera kwa Kayafa kupita ku Pretorio; koma munali mamawa; ndipo iwo sanalowa ku Pretorio, kuti angadetsedwe, koma kuti akadye Paskha." Nsembe ya madzulo imachitika ora la chisanu ndi chinai, ndendende nthawi yomwe Yesu anafera. "Ndipo ora lake pamenepo linali ngati lachisanu ndi chimodzi. Ndipo panali mdima pa dziko lonse kufikira ora lachisanu ndi chinai, ndipo dzuwa linada, Ndipo nsaru yotchinga ya m'Kachisi inang'ambika pakati. Ndipo pamene Yesu anapfuula ndi mau akuru, anati, Atate, m'manja mwanu ndipereka mzimu wanga. Ndipo pakutero anapereka mzimu wake."

"Yesu anaima pakatikati pa machitidwe a mitundu iwiri ndi mautumiki ao akuruakuru awiri. Iye, Mwanawankhosa wa Mulungu wopanda banga la uchimo, anali atafika pafupi penipeni podzipereka yekha nsembe ya machimo. Kuti pakutero athetse zinsembe zazikondwerero ndi zophera zomwe kwa zaka zikwi zinai zinalozera imfa yake. Ndipo pamene Iye anali pa chakudya cha Paskha ndi ophunzira ake, anakhazikitsa m'malo mwa Paskhalo, utumiki womwe uli chikumbutso cha nsembe yake yaikuru. Utumiki wa zinsembe wa Ayuda, unathetsedwa kwa myaya. Ndipo utumiki [wa mgonero] umene Khristu anaukhazikitsa kuchitidwa ndi omtsatira ake m'maiko onse kumibadwo yonse." Desire of Ages, 652.

Mkate Wopanda Chotupitsa: Chotupitsa chimapangitsa mkate kufufuma. Ngati mu mkate mulibe chotupitsa, sumafufuma. Chikondwerero cha mkate wopanda chotupitsa chinachitika patsiku lotsatira limene Khristu anapachikidwa, lomwe linali la Sabata chaka chija. Yesu anakwaniritsa chomwe chikondwererochi chimaimira, posauka Iye kwa akufa pa tsiku lotsatira la kupachikidwa kwakelo.

Zipatso Zoyamba Kucha: Levitiko 23:9-11 "Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, Nena ndi ana a Israyeli, nuti nao, Mutakalowa m'dziko limene ndikupatsani, ndi kucheka [kukolora] dzinthu zake, pamenepo muzidza nao mtolo wa zipatso zoyamba za masika anu kwa wansembe; ndipo iye aweyule mtolowo pamaso pa Yehova, ulandirikire inu, tsiku lotsata sabata wansembe aweyule." Nsembe yoweyulidwa yoperekadwayo imakhala ya zokolora zoyamba kucha yomwe imachitika. Imaimira kuona mtima, kapena kuti mbali ya dipo, loonetsa kuti kholora lonse likhala lochuruka.

Poyamba pamene a Israyeli analowa m'Dziko la Lonjezano, sanalilandire dziko lonse lomwe Mulungu anawalonjeza. Komabe anayenera kuthokoza, chifukwa mbali analandirayo inali dipo limene Mulungu awapatse, ngati atakhulupirika.

Yesu ali mphatso yeniyeni ya chipulumutso cha anthu yolonjezedwa ndi Mulungu. "Koma tsopano Khristu waukitsidwa kwa akufa, chipatso choundukula cha iwo akugona. Pakuti monga imfa inadza mwa munthu, kuuka kwa akufa kunadzanso mwa munthu. Pakuti monga mwa Adamu onse anamwalira, choteronso mwa Khristu onse akhalitsidwa ndi moyo. Koma yense m'dongosolo lake la iye yekha, chipatso choundukula Khristu; pomwepo iwo a Khristu, pakubwera kwake."

Chifukwa chakuti Khristu anagonjetsa tchimo nailaka mphamvu ya manda, adzatero anthu ake. Mateyu 27:50-53 akutifotokozera kuti panali zipatso zoundikura zochuruka pakuuka Khristu. "Ndipo Yesu, pamene anapfuula ndi mau akuru, anapereka mzimu wake. Ndipo onani, chinsaru chotchinga cha m'Kachisi chinang'ambika pakati, kuchokera kumwamba kufikira pansi; ndipo dziko linagwedezeka, ndi miyala inang'ambika; ndi manda anatseguka, ndi mitembo yambiri ya anthu oyera ntima, akugona kale, inauka; ndipo anaturuka m'manda mwao pambuyo pa kuuka kwake, nalowa m'mzinda woyera, naonekera kwa anthu ambiri."

Aefeso 4:8 akufotokoza chomwe chinachitika kwa anthu omwe anaukitsidwa kwa akufawo: "Chifukwa chake anena, M'mene anakwera kumwamba, anamanga ndende undende, naninkha zaufulu kwa anthu." Khristu anatenga anthu anaukitsidwawo nanka nao kumwamba.

Iwo anali zipatso zoyamba kucha za mdzukilo wake. Mulungu analandira awa, monga adzateronso ndi olungama onse.

Pentekoste: "Kukwera kwa Khristu kumwamba kunali chizindikilo chowatsimikizira ophunzira ake kuti adzalandira madalitso omwe Iye anawalonjeza. Chifukwa cha ichi ophunzirawo anayenbekezera kwa kanthawi asanayambe ntchito yao. Pamene Yesu anapyola miyamba nalowa pa zipata zakumwamba, anakwezedwa Iye pampando wachifumu wake nalemekezedwa ndi angelo. Chilinganizochi chitangotha, Iye anatumiza Mzimu Woyera yemwe anatsikira pa ophunzira ake ndi mkokomo ngati wa mphepo yaikuru, pomwepo Khristu anapatsidwanso ulemu waukuru umene anali nao pachiyambi ndi Atate ku nthawi zosayamba. Kuperekedwa kwa Mzimu Woyera kunali uthenga wochokera kumwamba wofotokoza za kwanitsidwa kwa kukwezedwa pampando kwa Mpulumutsi.

"Monga mwa lonjezano lake, Iye anatumiza Mzimu Woyera kwa ophunzira ake kuchokera kumwamba kukhala chizindikilo chowatsimikizira ophunzirawo kuti tsopano kuonjera pakukhala Mkuruwansembe ndi Mfumu, wapatsidwanso mphamvu zonse za kumwamba ndi za dziko lapansi, ndi kutinso anali Wodzozedwa wa anthu ake." Machitidwe Atumwi, 38-39.

Khristu atangobvekedwa Ukuruwansembe pomwepo Mzimu Woyera anatumizidwa. Pakutero chikondwerero cha Pentekoste chinakwanitsidwa.

Ndi zochititsa chidwi kuti mkate wopanda chotupitsa umaperekedwa pa Pentecoste (werengani Levitiko 23:15-17). Uwu umaimira Khristu wodzozedwayo ali wosachimwa. Monga analipo yemwe anadzozedwapo ali wochimwa, yemwenso anaimiridwa ndi mkate wa chotupitsa? Tiyeni tiwerenge Eksodo 40:9-15. Aroni anadzozedwa ali m'thupi la uchimo kuimira Khristu; nanga ana ake amuna andzozedwa, kuimiranso ndani? Mu Masalmo 133, Aroni anadzozedwa ndi mafuta ochuruka kotero kuti anatsikira mpaka pa zobvala zake kapena kuti thupi lake lonse. Mutu ukadzozedwa thupi limadzozedwanso. Khristu anadzozedwa, monga tinenenso kuti thupi lake lonse linadzozedwa? Ichitu chikuimira kuti Mzimu Woyera anaperekedwa kwa olungama [anthu] ochuruka omwe akumenyanabe nkhondo m'thupi la uchimoli. Monga kumasulira kotereku kukuchitiridwa umboni ndi Malemba? Monga anali ana a Aroni, panakhalaponso ansembe ena, monga lero palinso ansembe ena kuonjezera pa Yesu? 1 Petro 2:9 akuyankha: "Koma inu ndinu mbadwa yosankhika, ansembe achifumu, mtundu woyera mtima, anthu a mwini wake, kotero kuti mukalalikire zoposazo za Iye amene anakuitananі muturuke mumdima mulowe kuunika kwake kodabwitsa." Komanso Chbvumbulutso 1:6 ndi 5:10 akutifotokozera kuti Khristu watiyesa ife mafumu ndi ansembe a Mulungu ndi Atate wake.

Malipenga: Chikondwerero cha Malipenga chimaimira masiku khumi a nkhawa patsogolo pa Tsiku la Chitetezero. Malipenga amaimbidwa kuchenjeza za china chake chinali nkudza. Malipengawa amakumbutsa kuti machimo onse abvomerezedwe ndi kulapidwa. Chikondwererochi chinakwanitsidwa makamaka patsogolo pa October 22, 1844. Palibenso nthawi yomwe linaperekedwa chenjezo lamphamvu kuposa la nthawiyi.

Tsiku La Chitetezero: Pa tsiku la khumi la mwezi wachisanu ndi chiwiri wa 1844 (October 22, 1844), ntchito yeniyeni yachitetezero inayambika. Pano tiri m'nthawi ya chiweruzo chakufufuza mitima.

Misasa: Chikondwerero cha Misasa ndi pangano lomwe likukwanitsidwa kotheratu m'dipo lomwe Yesu akulichita kwa olungama omwenso ali zipatso zoundukura. Ichi chidzapherezera kotheratu pakubwera kwake kwachiwiri. Ayuda anauzidwa kukhala m'misasa masiku asanu ndi awiri, mbusa Richards akufotokoza kuti izi zikuimira masiku asanu ndi awiri omwe olungama adzakhale akuyenda ulendo wao wochokera pansi pano kupita kumwamba. Malingana ndi Levitiko 23, ndi ana enieni obadwa mwa a Israyeli omwe analamulidwa kusonkhana pamodzi ku Yerusalemu. Pakubwera kwa Yesu, ndi gulu limodzi la olungama okha lomwe lidzatengedwe kulowa kumwamba.

Ellen White wangotchulapo kawiri kokha za chikondwerero cha misasa m'zolembera zake. M'zolemberazo iye akutilimbikitsa ife kuchita madyerero a Misasa nthawi zonse, chifukwa pakutero timakwaniritsa cholinga cha chikondwererochi. Iye sakunena kuti tizichisunga koma kuti tidzichita "chikondwererochi."

Mbusa Richards akufotokoza kuti zatchulidwa zikondwerero zisanu ndi ziwiri m'Levitiko 23. Chiwerengero "zisanu ndi ziwiri" ndi cha umphumphu wa machitidwe a chiyero a Mzimu Woyera. Choncho zikondwererozi pa zokha, osaphatikizapo Sabata la tsiku la chisanu ndi chiwiri, zikukwaniritsa mwamachitidwe a chilungamo cha Umulungu. Sabata la pa mulungu siliri mbali ya zikondwerero zazinsembezi ngakhale latchulidwa limodzi nazo.

Zolembera zina zomwe zinandithandiza ine kumvetsetsa za zinsembe za Chiyuda kuti sizinali zokhalitsa, zinati, "Ansembe omwe anatumikira m'kachisi' anataya masomphenya posamvetsetsa chomwe chinali cholinga cha utumiki womwe ankauchita. Iwo Sanamvetsetse iwo za chomwe utumiki wa zinsembe anauchitawo umaimira. Popereka nsembe zophera amangochita ngati mwa masewero a zisudzo. Mautumiki omwe Mulungu anawakhazikitsa kukhala chopulumutsira anthu, anasandutsidwa owapangitsa khungu ndi kulimbitsa mitima ya otumikirawo kukhala ngati mwala. Mulungu sakanathanso kupulumutsa munthu pogwiritsa ntchito mautumiki oterewa. Choncho mchitidwe wotere wonsewo unayenera uchotsedwe ndi kutaidwa." Desire of Ages, 36.

Tsiku lina ndinkawerenga Agalatiya 4:9-11: "Koma tsopano, podziwa Mulungu inu, koma makamaka podziwika ndi Mulungu, mubwereranso bwanji kutsata miyambo yofoka ndi yaumphawi, imene mufuna kubwerezanso kuichitira ukapolo? Musunga masiku, ndi miyezi, ndi nyengo ndi zaka. Ndiopera inu, kuti kapena ndadzibvutitsa ndi

inu chabe." Poyambirira pomwe nditafunsa tanthauzo la mau awa, aphunzitsi a zikondwerero anati akutanthauza za zizindikilo za njira yozungulira [zodiac] momwe mumayendamo zakumwamba komanso za kakhalidwe ka za kumwambazo [astrology].

Komabe, pano ndikutha kulumikiza ndi pena pake m'mutu womwewu: "Ndiuzeni, inu akufuna kukhala omvera lamulo, kodi simukumva chilamulo? Pakuti palembedwa, kuti Abrahamu anali nao ana amuna awiri, mmodzi wobadwa mwa mdzakazi, ndi mmodzi wobadwa mwa mfulu. Komatu uyo wa mdzakazi anabadwa monga mwa thupi; koma iye wa mfuluyo, anabadwa monga mwa lonjezano. Izo ndizo zophiphiritsa; pakuti akaziwa ali mapangano awiri, mmodzi wa ku phiri la Sinai, akubalira ukapolo, ndiye Hagara. Koma Hagara ndiye phiri la Sinai, m'Arabiya, nafanana ndi Yerusalemu wa tsopano; pakuti ali muukapolo pamodzi ndi ana ake. Koma Yerusalemu wa kumwamba uli waufulu, ndiwo amai wathu. Pakuti kwalembedwa, Kondwera, chumba iwe wosabala; yimba nthungululu, nupfuule iwe wosamva kuwawa kwa kubala; pakuti ana ake a iye ali mbeta achuruka koposa ana a iye ali naye mwamuna. Koma ife, abale monga Isake, tiri ana a lonjezano. Komatu monga pompaja iye wobadwa monga mwa thupi anazunza wobadwa monga mwa Mzimu, momwemonso tsopano."

Kwa ine mau'wa akumveka kuti Paulo amanena za kufunika kwa kusiyanitsa kwa kusunga zikondwerero za zinsembe ndi malamulo a Mulungu. Sakunena za chikhalidwe cha zinthu zakumwamba [astrology]. Pamene ndinawerenganso mau awa olembedwa ndi Ellen White, anatsimikizira za tanthauzo linali m'maganizo mwanga'lo, ndipo ndinakondwera: " Mu mpingo uli wonse muli Ayuda mwa chibadwa. Kudzera mwa okhulupirira ngati amenewa aphunzitsi a Chiyuda anapezerapo mwai wolowera ndi kukhazikitsa ziphunzitso zao m'mipingo. Nkosatheka, pogwiritsa ntchito ziphunzitso za m'Malemba, Ayudawo kugonjetsa ziphunzitso za Paulo; koma iwo anagwiritsa ntchito machenjerero a chikunja kugonjetsa chikoka ndiponso mphamvu yake. Anamuipitsa iye pakunena kuti sanali wophunzira wa Yesu, ndipo sanalandira ulamuliro uli wonse kuchokera kwa Iye; chifukwa cha chimenechi , iwo anamnamizira iye kuti akuphunzitsa ziphunzitso zotsutsana mwachindunji ndi zomwe anaphunzitsa Petro, Yakobo, ndi atumwi ena onse. Umu ndimo atumiki a chipembedzo cha Chiyuda anachitira pofuna kuwalekanitsa akhristu ochuruka ndi mphunzitsi wao wa uthenga wabwinoyo. Atatha kumuipitsa motero, iwo anawapatutsa otsatira a mtumwiyo kuwabwezera ku miyambo yakusunga zikondwerero za zinsembe za chilamulo zomwe ndi zosafunikiranso pa chipulumutso. Chikhulipiriro cha Yesu ndi kusunga malamulo khumi, zinanenedwa zosafunikira. Magawano, chikunja ndi kuchita zofuna za thupi kunakula kwambiri pakati pa okhulupirira a ku Galatiya." LP, 188.

Zolembera zina za Mau a Mzimu Wachinenero zomwe zinandithandiza kumvetsetsa kwambiri za kusafunika kwa zikondwerero za zinsembe m'nthawi yathu ino zinali Life Sketches of Paul [Moyo wa Paulo], 121-122: "Magulu otumidwa ndi aphunzitsi a Chiyuda anauka, kunka akusokeretsa okhulupirira omwe analowa Chikhristu powauza kuti azisunganso chilamulo cha zinsembe pochita mdulidwe. Iwo anaphunzitsa kuti Israyeli wolephera wakale uja anali chikhalirebe mtundu wokwezedwa ndi ana a Abrahamu, ndipo akulandirabe malonjezano omwe anaperekedwa kwa iye. Ndi mtima wao wonse anaganiza kuti kuphatikiza ziphunzitso za Chiyuda ndi za Chikhristu pamodzi, inali njira yachipambano yowachotsera akhristuwo m'chikhulupiriro angochilandiracho kuti alowe ndi kuonjezera chiwerengero cha ziwalo za Chiyudazo kukhala chachikuru.

Magulu otumudwa ndi Ayudawo anaonetsa mbali yao, yotsutsana ndi ya Paulo, ponka akuuza anthu kuti polandira anthu achikunja ndi osadulidwa mu mpingo, mtumwiyu amachititsa kuti Ayuda asachilandire chiphunzitso cha Chikhristu poopa kudetsedwa ndi achikunja osadulidwawo. Umu ndimo iwo anayesetsera kukutchinjirizira kutsutsana kwao ndi chiphunzitso cha mtendere chomwe chinaphunzitsidwa ndi atumiki otumidwa ndi Mulungu. "Iwo anakana kubvomereza kuti ntchito yakupulumutsa ya Khristu inakhuza anthu onse a dziko lapansi. Ananka akulalikira kuti Khristuyo anali Mpulumutsi wa Ahebri [Ayuda] okha.; choncho onse osakhala Ahebri adziyamba alandira mdulidwe asanabvomerezedwe kutengako mbali mu mpingo wa Khristu.

Utachitika msonkhano wa ku Yerusalemu ndi kuperekapo maganizo ake, ambiri a Ayuda sanagwirizane nazo, koma ngakhale zinali choncho, kuyambira pamenepo Ayudawo sanatsutsanenso ndi mtumwiyo mopitiriza monga anachitira pachiyambi. Pa nkhani ya mdulidweyi, msonkhano wa ku Yerusalemu'wo unagamula kuti onse omwe analowa Chikhristu kuchokera ku mtundu wa Chiyuda apitirize kuchita monga chilamulo cha Mose chinanenera ngati atafuna kutero, pamene otembenuka onse amitundu asakakamizidwe kuchita mdulidwe. Koma mbali yotsutsayo inatengerapo mwai wa chigamulochi, nipitiriza kulekanitsa iwo osunga chilamulo ndi osachisunga, ndi kuopseza osachisungawo kuti pakutero anadzilekanitsa ndi Mulungu.

Kodi ndi zinthu ziti m'chilamulo cha zinsembe, zomwe Ayuda anafunitsitsa zitamachitika? Sizinali nsembe zophera, chifukwa izi zinalekeka pa imfa ya Khristu. Monga iwo anangofuna kukweza mdulidwe wokhawo? Mdulidwe unali chimodzi cha zinthu zambiri zomwe anafunitsitsa zidzichitidwa. Mkumvera kwanga, ndiponso kuchokera m'maumboni ena, zikuoneka kuti iwo anafunitsitsanso kuti ngakhale masiku azikondwerero azisungidwa.

Chimene ndachipeza mkufufuza kwanga ndi chakuti anthu ambiri omwe amasunga masiku azikondwerero amalemekeza ndi kukweza masikuwo kwambiri ndi kunyozera chidzudzulo ndi malangizo ena a Mau a Mzimu Wachinenero. Ambiri amabvala mikanda, ndolo ndi zoletsedwa zina. Amadyanso nyama – maka maka m'masiku a zikondwererozo kweni kweni cha Paskha. M'malo mophunzitsa za Sabata loona moikapo mtima, monga amachitira a Adventist, anthu ambiri omwe amasunga zikondwererozi, ngati si onse, zapezeka kuti amalilowetsa pansi ndi kulipondereza Sabata, nkumakweza ndi kusamala kwambiri masabata a zikondwerero.

Zapekanso kuti pali gulu lina lomwe limachitanso ngakhale masewera a mitundu mitundu kuphatikiza a mpira pa tsiku lotsekera zikondwererozo. Iwo alibe chidziwitso ngakhale pang'ono za momwe Sabata limayenera kusungidwira. Amachita chiri chonse chimene chawafikira kapenanso angachifikire, ndipo samatha kudziletsa kapena kulingirirapo kuti ndi zinthu ziti ayenera kapena sayenera kuzichita pa Sabata.

Kalelo kuliza kwa lipenga inali njira yoitanira mtundu wonse ku mapemphero. Koma lero lino osunga zikondwererowa amatha kungoomba lipenga ngakhale atakhalapo anthu khumi okha pa gulu lao. Zinthu sizinayenera kukhala choncho. Ngati anthu ali m'makomo mwao, kumakhala kobvuta kumva lipenga loombedwalo. Chikanakhala chabwino kumangogwiritsa ntchito mafoni monga njira imodzi yoitanirana ku msonkhano. Anthuwa amathanso kuliza malipenga a nyanga za nkhosa mwamwambo ngakhale anthu onse atasonkhana kale pa malo amodzi. Kale kuomba lipenga kunali njira yoitanira anthu omwe anali patali patali kuti abwere pamodzi. Maombedwe a lipengawo amakhala osiyanasiyana m'zikondwerero zosiyanasiyana molingana ndi cholinga cha chikondwerero chiri chonse pa chokha; panopa cholinga cha chikondwerero chiri chonse chinakwanitsidwa kale. Koma patsala kuliza kumodzi kwa lipenga. Uku sikudzachitidwa ndi munthunso koma ndi mngelo kapena Khristu ndipo kudzakhala kuitana akufa kuti auke kuchokera m'manda pa lipenga lotsiriza.

Pali chinthu chotsiriza chomwe ndafuna kuti ndichinene. Akazi ambiri omwe ali m'chipembedzo chosunga zikondwerero amakonda kuphimba kumutu. Kwa inu amene mumakhulupirira m'Mau a Mzimu Wachinenero, mverani langizo ili za mchitidwewu. Ellen White anapatsidwa uthenga wa momwe amai athu ayenera kubvalira. Uthengawu ukudziwika ndi mau akuti "kabvalidwe koyenera." Ngakhale kabvalidweka sikamasamalidwa, koma



m'menemo ndimomwe akazi anayenera kubvalira. Kabvalidwe kabwinoko sikakuphatikiza kuphimba ku mutu. Tisalole ife kabvalidwe kodziyenereza kophimba kumutu. Ichi ndi china cha zifukwa zimene Mulungu anatipatsira ife mneneri ku nthawi yakumapeto ino, kuti atichenjeze. Mulungu amadziwa zakuipa kwa kabvalidwe kodziyenerezaka.

Tipemphere kuti tikhale ophunzira olimbika a Mau a Mulungu ndi kugwiritsa ntchito Mau a Mzimu Wachinenero kukhala muuni wotitsogolera kumvetsetsa Malemba. Tisayang'ane kwa munthu kuti tipeze chidziwitso komanso monga chitsanzo chathu. Tipemphere Mulungu atithandize. Wolemba Jeff Bell

Nditangotsiriza kulemba za masiku a zikondwerero, pambuyo pa miyezi yowerengeka mtima wanga unayambanso kulingalira za chinthu china chatsopano. Ichi chinandidzera nditangowerenga pa mutu wina wa m'bukhu la Early Writings wotchedwa "Kumapeto Kwa Masiku 2300." Ndinaturukira kuti masiku onse a zikondwerero za zinsembe za Chiyuda, kupatula Tsiku Lachitetezero, amakhuza utumiki wa bwalo lakunja la Malo Opatulika.

Tsono popeza tikuzindikira kuti panopa tinayenera kumtsatira Yesu m'Malo Opatulikitsa, m'chikhulupiriro chathu, kukakamira pa mautmiki a Malo Opatulika [pa kudziyenereza kwathu] ndi chinthu chosapindulitsa. Malinga ndi mutu womwe ndatchula wa m'Early Writings, ngati ife sitingalowe mwa chikhulupiriro ndi kukhala ndi Yesu m'Malo Opatulikitsa, tizindikire kuti mapemphero athu onse omwe timapemphera amayankhidwa ndi Satana. Kodi chingakhale cha nzeru kuti momwe tiri m'nthawi ya ora la Tsiku la Chitetezero'yi tisakhale naye Yesu m'Malo Opatulikitsa m'chikhulupiriro chathu, ndiponso tisalumikizane naye koma nkumatsutsa kuti mapemphero athu sakuyankhidwa ndi Satana? Ambiri timadzinamiza choncho. Ndiri ndi chiyembekezo kuti tiyesetsa kukhala ndi Yesu m'Malo Opatulikitsa, ndipo ichi chidalira pakuti munthu ali yense payekha akhale wosamalitsitsa.

## ZIKONDWERERO ZA PACHAKA ZA ZINSEMBE SIZOFUNIKA KWA ANTHU OKHALA NDI

## CHIKHULUPIRIRO MWA YESU

Chifupikitso cha kabukhu kolembedwa ndi R. Lee – 2009.

Tchimo losabisa, lochitidwa moonetsera linachotseratu chikhulupiriro cha Uthenga Wabwino mu m'mipingo yaku Galatiya. Khristu, maziko oona, ananyozedwa poyera chifukwa cha miyambo yopanda tanthauzo ya zinsembe za Chiyuda. Mtumwi Paulo anaona kuti kuti mipingoyo ipulumutsidwe kuchoopsa inalimocho, papezeke njira zoyenera zitsatidwe…." {LP 190}.

"Za zikondwererozi, Khristu analamulira ophunzira ake kuti asasamale ndi kulemetsedwa ndi miyambo ya Chiyuda yakaleyo yomwe inakhazikika m'zinsembe zophera ndi masiku omwe zimachitikiramo. Izi sizinali zofunikira; chifukwa zinali m'thunzi wa zinthu zinali nkudza kutanthauza kuti zimaimira Iye, amene anali mphamvu ndi maziko a zinsembe zonse za Chiyuda zomwe zinalozera za Iye amene ali nsembe yokhayo yaikuru ndi yoposa yoperekedwa chifukwa cha machimo a dziko lapansi." {RH, June 14, 1898 par. 15}.

Zobvuta Zomwe Osunga Zikondwerero za Chiyuda Amapezana Nazo

Ndikofunika kufotokoza momveka bwino kuti malingana ndi momwe walembera mtumwi Paulo pa Agalatiya 3:6-10 ndi 5:1-4…, munthu asangochita monga akufunira ngati akufuna kusunga malamulo a chilamulo cha zinsembe cha Mose, achite onse ndi zonse osasiyako ena ndi zina zomwe iye akuziona kuti ndi zobvuta ndi zosatheka kuzitsatira monga zikufunikira. Chofunika ndi chakuti ngati munthu akufuna kubwereradi m'mbuyo ndi kuyambanso kusunga chilamulo chotopetsachi monga zimachitikira kalekalelo, iye atero ndi MALAMULO ONSEWO motsatira ndi mwandondomeko osasiyapo kanthu monga zinalembedwera m'chilamulo cha Mose. Kumvetsetsa bwino bwino zomwe chiphunzitso cha Chipangano Chatsopanochi chikufotokoza kukupereka kubetchera kwakukuru kwa anthu onse omwe akuti akupitirizabe kusunga zikondwerero za zinsembe za Chiyuda, zomwe zafotokozedwa momveka m'munsimu.

Eksodo 12:21-25: - "Pamenepo Mose anaitana akuru onse a Israyeli, nanena nao, Pitani, dzitengereni ana a nkhosa monga mwa mabanja anu, nimuphere Paskha. Ndipo muzitenga mpukutu wa hisope, ndi kuubviika m'mwazi uli m'mbale, ndi kupaka mwazi uli m'mbalemo pa mphuthu ya pamwamba ndi pambali; koma inu, asaturuke munthu pakhomo pa nyumba yake kufikira m'mwawa. Pakuti Yehova adzapita pakatipo kukantha Aigupto; koma pamene adzaona mwaziwo pa mphuthu pamwamba ndi za pambali, Yehova adzapitirira pakhomopo, osalola woononga alowe m'nyumba zanu kukukanthani. Ndipo muzisunga chinthu ichi chikhale lemba la kwa inu, ndi kwa ana anu ku nthawi zonse. Ndipo kudzakhala, pamene mulowa m'dziko limene Yehova adzakupatsani, monga analankhula, muzisunga kutumikira kumeneku."

Eksodo 23:16: - "Ndi madyerero a masika, zipatso zoyamba za ntchito zako, zimene udazibzala m'munda; ndi madyerero akututa, pa chaka, pamene ututa ntchito zako za m'munda."

Kufotokoza zina zosankhidwa kuchokwera Ku Umboni wa Yesu

S.T. July 29, 1886: - "Zikondwerero zonse za m'chilamulo cha zinsembe za Chiyuda zinali ulosi, ulosi wa zinsinsi mu ndondomeko ya nthano ya chipulumutso. Mautumiki ndi zikondwerero za chilamulo cha zinsembezo zinaperekedwa ndi Khristu mwini, amene… anali mtsogoleri ndi mkuru wa makamu a Israyeli; ndipo chilamulochi chinali choyenera kuchitidwa mosamalitsa, chifukwa ichonso ndi choyera. Ngakhale pambuyo pakuti sichinayenera kusungidwanso, Paulo anafotokoza chomwe ichi chimaimira ndi kukwanitsidwamo kwa Ayuda, naonetsera gawo lomwe chimachita mu ndondomeko ya chipulumutso ndiponso kulumikizana kwake ndi Khristu; mtumwi wopambanayu anachitcha ichi chilamulo cholemekezeka, mogwirizana ndi umulungu wa Iye amene anachipereka. Ichi chomwe chidali choti chidzachotsedwa chinali cholemekezeka, koma sichinali lamulo la Mulungu loyendetsera banja lake la za Kumwamba ndi dziko lapansi; pakuti loyendetsera boma lakelo liri la ku nthawi zonse, monga kumwamba kuli kwa myaya chomwechonso malamulo a Mulungu adzakhalitsa kosatha."

R. & H., February 22, 1881: - Yohana anakhala moyo naona uthenga wabwino wa Khristu utalalikidwa m'fupi ndi m'tari,,…. Koma anadzazidwa ndi chisoni pamene anaona ziphunzitso zosokeretsa zikulowa mu mpingo. Ena a anthu amene anamlandira Khristu, analalikira kuti chikondi cha Khristuyo chinawapulumutsa kotero kunali kosafunikanso kwa iwo kumvera ndi kusunga malamulo a Mulungu. Kumbali ina enanso analimbikitsa za kusunga malamulo onse a Mulungu powaphatikiza awa ndi miyambo ndi malamulo a zinsembe za Chiyuda, chifukwa amati mbali ziwirizi pamodzi ndi zokwanira pa chipulumutso, ngakhale popanda mwazi wa Khristu. Iwo anaphunzitsa kuti Khristu anali chabe munthu wabwino, monga anali atumwi, pakutero iwo anakana umulungu wake. Yohane anachiona choopsa chomwe mpingo unalimochi, nalakalaka kuti ziwalo zake zisalandire ziphunzitso zotere, ndipo iye anatsutsana ndi izi molimba mtima."

## MASEWERA A UZIMU: GWERO LA KUGALUKIRA MULUNGU KWAKUKURU ALANDIRIDWA M'CHI-ADVENTIST.

Mbiri ya dziko lapansi yadzala ndi nkhani za ziwembu. Taganizirani za kuphedwa kwa Kaisara Julius kunaloseredwako pa Danieli 11:17-19. Taganizirani za chiwembu cha Bolshevik, cha Lenin pakulanda ufumu wa Tsar wa ku Russia. Takumbukirani za tsiku la Guy Fawes ndi upandu wa ma-Jesuiti wolimbana ndi dziko la Britain kuti aliononge pokhala ilo kuchimake cha Mpanduko (Protestantism). Taganizirani za chiwembu cha bungwe la illuminati [chipembedzo cha Satana] pansi pa Adam Weishaupt komanso nkhanza za ma-Jesuiti zofuna kulanda ulamuliro wa dziko lapansi. Taganizirani za kulumbira konama kwa mabishopu. Taganizirani za malumbiro oopsa a ma-Jesuiti. Taganizirani za lumbiro la ma-Jesuiti lofunitsitsa kuonongeratu a Mpanduko. Mu Mbiri ya dziko lapansi muli maupandu ambiri otchuka ndi ochita kukonzedwa mwa dala.

### Upandu wa Aroma Wolimbana ndi Maufulu athu

Bukhu la Mkangano Waukuru [Great Controversy] likuika poyera chiwembu cha Aroma cholimbana ndikuononga maufulu athu. Ma-Jesuiti atsekereza zofufuzafufuza pakati anthu ochuruka m'pfuko lathu lonse pogwiritsa ntchito "matatanthauzidwe onama za chomwe upandu uli." Ichi ndicho George W Bush anachichitanso pambuyo pa 9-11 pakutsekereza kufufuza kuli konse poopa kuti zingadziwike kuti boma linatengako mbali pa chiwembu cha 9-11'cho. M'malo mwake anthu anangouzidwa kukhulupirira zinthu za bodza m'dzina lakuti adzikhala ogonjera ndi kumvera ulamuliro wa boma, womwe uli maziko enieni akukhazikitsidwa kwa m'chitidwe wa kayendetsedwe ka zinthu wa chi-Roma m'America. Mu "Malangizo Oganiza monga Uchitira Mpingo [Rules for Thinking With the Church]" tikuwerenga kuti ma-Jesuiti amaphunzitsidwa kuti ngati mpingo ukunena kuti kuyera kuli mdima, iwo abvomereze ndi kukhulupirira. Ndipo ichi ndi chitsanzo chenicheni chomwe chimaperekedwa. Munthu asamabvutike ndi zofufuzafufuza, koma azingobvomereza zomwe wauzidwa ndi ambuye ake ma-Jesuiti, ngakhale zoterozo zikhale zonama.

Ngati pali chinthu chimodzi chofunikira kwambiri kuti chiphunzitsidwe kuchokera mu Uthenga Wabwino wa m'Chipangano Chatsopano, komanso m'Chipangano Chakale, ndi chakuti mpingo woona wa Yesu Khristu ukhazikika pa maziko Khristu mwini, pa Khristu yekha osati pa wina, komanso kuti mpingo uli wonse ngakhale ukhale kuti wakhazikitsidwa pa maziko Khristu ungathe kusokonezedwa ndi machenjerero a Satana, ngakhale mpingowo mwa iwo wokha ungamadzinamize kuti ukuchita zolondora ndi kuchita monga mwa Malemba. Ungathe kulephera kumzindikira Ambuye wake ngakhale kudana naye Iye amene ali Mpulumutsi ndi Mfumu ya Mafumu wake, ndiponso kudana ndi omtsatira ake ngakhale kumumpha Ambuye wakeyo pamodzi ndi omtsatira ake olungama.

Ndi umboni ku mphamvu ya Satana ndi ku luso lake lakunka akulanda mipingo yokhazikika ; ndiponso umboni ku chifoko cha chikhalidwe cha umunthu chakugonjera ku machenjerero ake, kuti Satana anachita chipambano pakulanda Mpingo wokhazikika wa Chiyuda, kotero kuti pamene Khristu anadza m'thupi, nakhala Mulungu m'chifanizo cha umunthu "pomanga hema wake" pakati pathu, Mpingo, umene poyamba unakhazikitsidwa ndi Khristu mwini, unamyesa Iye mdani, nuyesera kambirimbiri kumupha Iye , unataya kunja maina a omtsatira ake, nuchita chipambano kumapeto kwake pogwirizana ndi mphamvu-za ulamuliro wa dziko za-Aroma kumupha Khristu mwankhanza ndi mopanda chisoni pa mtanda wokhala ndi udani waukuru pa Gologota.

Ndi umboni wakunthawi zonse wa uthenga wabwino wosatha kuti mpingo wa Khristu wakhazikika pa maziko Khristuyo, ndi wozikika pa Iye kuyambira pa chiyambi, koma podzikhulupirira ndi kudzinamiza kuti ukutsatira Malemba mosamalitsa, chikhalirecho uli woukira anthu olungama, monga unachitira mpingo wa Aroma-Katolika, womwenso pofunitsitsa kudzikundikira mphamvu ndi ulamuliro zomwe zinayenera gulu lodziwika ndi dzina lakuti "ana a Mulungu" unazunza polimbana komanso kupha anthu ochurukitsa otsatira ndi ophunzira eni eni a Khristu, nuchitanso nkhondo yolimbana ndi Khristu mwini kuonjezera pa yomwe unachita pa olungama ake.

### Choonadi cha Mabuku Anai a Uthenga Wabwino

Ichi ndi choonadi cha zomwe zinalembedwa m'mabuku anai a Uthenga Wabwino, ndipo kuchikana ichi kuli chimodzimodzi kuukana Uthenga Wabwino Wosatha wa Yesu Khristu, pozindikira kuti ichi ndi Choonadi Choyamba, Chiphunzitso Chofunikira chopezeka m'mabuku Anai a Uthenga Wabwino maka bukhu la Uthenga wa Yohane. Si mabuku anai okha omwe akuchitira umboni choonadi cha uthenga wabwino wosatha ndi wodabwitsawu, komanso Machitidwe ndi Chipangano Chatsopano chonse, akufotokoza za kuzunzidwa kwa otsatira a Yesu, komwe kunachitidwa ndi Mpingo wokhazikikawo, komanso makalata olembedwa ndi atumwi m'Chipangano Chatsopano omwe ndi odzala ndi za nkhondo yosalekeza yomwe Mpingo Wokhazikikawo unaichita polimbana ndi Paulo ndiponso mpingo unali kungoyamba kumenewo.

Padutsa zaka khumi, ndipo pfuko lathu likukumbukira 9-11, iyi ndi nthawinso yomwe Adventist Review ikuchipeza chobvuta kukana mwatchutchutchu kuti ikukweza chikunja polimbikitsa kuphatikiza Mau a Mzimu Wachinenero ndi zolembera za ziphunzitso za Miyambo ya Umunthu m'zolemba zake; iyo imati palibe chochititsa mantha kutero. Adventist Review ya Satisfying the Longing of Your Soul [Kukwanitsa Cholakalaka Cha Moyo Wanu] yomwe ikufotokoza za Roman Lectio Divina [Umulungu wa Aroma] ndi Breath Prayers [Mapemphero Ogwira Mtima] ndiponso kulimbikitsa za mabuku osayenera a chipembedzo cha chi-Hindu ndi machitidwe

ake, ikufalitsidwa mofulumira kwambiri kuchokera m'ma ABC ndipo sichedwa kutha chifukwa ziwalo za Mpingo zimaifunitsitsa ngati agalu okhaula ndi ludzu lalikuru.

### Mpingo Ukanitsitsa za Chiwembu cha Ma-Jesuiti

Dzulodzulo'li ndinapezana ndi munthu wina amene ndi banja lake anasamuka kukakhala m'mapiri zaka zowerengeka zapitazo. Tinalankhulana kwa kanthawi ndithu. Anandifotokozera kuti wakhala akumenya nkhondo yotsutsa chiphunzitso cha Uzimu Wochitidwa monga mwa miyambo ndi machitidwe a umunthu [Spiritual Formation] mu mpingo wake, ndipo iye sakukaika kuti mbusa wake ndi m'Jesuiti. Iye anafotokoza kuti mbusayo anamfunsa funso lokaikitsa lakuti, "Ukuganiza kuti ma-Jesuiti aulowerera mpingo wathu? "Zosatheka kuwerenga kachikwi chimodzi!" Iye anapitiriza kufotokoza kuti awa ndi mau amene mbusayo analankhula "Zosatheka kuwerenga kachikwi chimodzi!"

Mpingo Uyesetsa Kubisa za Uzimu wa Miyambo

Sizobisa, kunena mwatchutchutchu, kuti anthu sakuphunzitsidwa kukhulupirira mau a choonadi, chomwe chalembedwa momveka bwino ndi mosaphiphiritsa m'maumboni ochuruka, koma mpingo wa Adventist wasankha kuziziritsa chikumbumtima ndi kutsogolera malingaliro a anthu kugonjera ulamuliro wa ma-Jesuiti kudzera m'ziphunzitso za Uzimu Wokhazikika pa Miyambo ya Umunthu. Ndi mchitidwe womwewo wopondereza chikumbumtima, wa ma-Jesuiti kudzera mu chiphunzitso cha Uzimu Wochitidwa mwa Miyambowu, womwe ukuchitika pofuna kukhazikitsa Fano la Kayendetsedwe ka Zinthu la Aroma. Kuzimitsiratu chikumbumtima cha kutsatira "malamulo ndi kaganizidwe kabwino mu mpingo" ndi cholinga cheni cheni cha chiphunzitso cha ma-Jesuiti cha Uzimu Wokhazikika pa Miyambo ya Umunthu. Pano mchitidwewu ukukakamizidwa mwa mphamvu.

M'Adventist Review [August 11, 2011 yotchedwa ["Formed In Christ" [Kulengedwa mwa Khristu]," akachenjede atatu ophunzitsa pa sukulu ya ubusa ndipo amaphunzitsa phunziro la Uzimu Wokhazikika pa Miyambo [Spiritual Formation], akukana kuti iwo samaphunzitsa " chiphunzitso chosokeretsachi." Pokanapo akuti anthu omwe akuwanamizirawo akutero pongofuna kumkweza Ellen White ndi kutsutsana ndi bungwe la Uzimu Wokhazikika pa Miyambo ya Umunthu.

### Iye Amene Ali ndi Luntha[Nzeru] Amvetsetse

Bukhu la maphunziro a nkhondo la ma-Jesuiti – The Art of War, lolembedwa ndi Sun, Art Militaire Des of War, ou Receuceil D'Anciens Traites Sur La Guerre, lomasulidwa m'zilankhulo za maiko akumadzulo , kuphatikiza m'chi-French, lolembedwa ndi M'Jesuiti Yosefe-Marie Amiot, yemwe anali wofufuzafufuza wa za m'mlengalenga wa Mfumu ya China, m'1772, chaka chimodzi kusanachitike kuponderezedwa kwa Ma-Jesuit m'1773, linachitira ndemanga yochititsa chidwi iyi yochokera kwa Bwana Sun: "Choncho maganizo okhazikitsa gulu la asirikali liyenera kukhala lopanda tanthauzo. Pamene palibe cholinga, zinthu za chinsinsi sizingakhale za tanthauzo, zofufuzafufuza sizingakhalenso chinthu cha chipambano." – Sun Tzu, The Art of War: Complete Texts and Commentaries, tr. Thomasi Claery, Boston: Shambhala, 2003, p. 116.

Mobwerezabwereza, nkhondo yafika poti ikukanika ndi kuopseza nzeru ndi njira zamseri za mdani poziika zolingirira zake poyera , atumiki ake akuchita mobisalira , mosadzionetsera chikhalireccho akupitiriza kumenya nkhondo mwakachetechete. Iwo akupanga gulu la nkhondo ndi kuliphunzitsira ku Andrews, pa mtima penipeni pophunzitsira atumiki a Mulungu a Mpingo wa SDA, kuti agonjetse kuchokera mkati. Akukondwera ndi chipambano cha pansipansi chao, ponka akuika zizindikilo zao pa zilinganizo zao zolembedwa Uzimu Wokhazikika pa Miyambo ya Umunthu. Atsogoleri a Uzimu wa Miyambo ya Umunthu, akumapereka zitsanzo za Uzimu wa Miyambo Woyenera, kukhala ngati njira imodzi yosekera ndi kunyozera umbuli ndi kupusa kwa iwo amene akuwalanda nyale yao, nadzitamandira za chipambano chao – iwo sakuwaletsa olandidwawo kuchita zinthu monga akufunira, koma akumangosokoneza cholinga chao. Olandawo akumachita zizindikilo zokweza cholinga chao.

Chifukwa chiyani Dybhahl anapita ku Benedictine Monastery mwachinsinsi ndi kukakhalako mwezi umodzi kapena iwiri?

Adventist Review sikufotokoza chomwe John Dybdahl, mtsogoleri wotchuka m'mpingo wathu komanso wa chilinganizo cha Uzimu Wokhazikitsidwa mwa Miyambo ya Umunthu ku sukulu ya ukachenjede ndiponso wa phunziro la tsopano la Ukachenjede wa Utumiki anakachita ku Benedictine Monestary. Mtsogoleri wa phunziro la Uzimu Wokhazikika pa Miyambo'yu, anapita mwachinsinsi ku Benedictine Monastery nakhalako mwezi umodzi kapena iwiri, anachita ichi atangobwera kuchokera ku Thailand komwe anakagwira ntchito ya mpingo. Ine [mlembi wa zolemberazi] ndinazindikira za ulendowo chifukwa amalume anga, apongozi a Dybdahl, anadiuza kuti a Dybdahl apita ku Benectine Monastery kwa mwezi umodzi kapena iwiri, koma palibe amene akudziwa chomwe mkuruyu amachitako. Ngati zinthu zikukhala chonchi, tinene kuti ndi maulendo angati aku ma-Monastery a chi-Roma omwe atsogoleri chi-Adventist amawachita mwakabisira?

Kachenjede Larry Geraty wa phunziro la za Ufulu ku sukulu ya ubusa, anaonedwa kambiri akuyenda momasuka ndi ansembe awiri achi-Katolika ali m'zovala zao za unsembe akudutsa pa bwalo la sukulu ya Andrews, awiriwo akuyenda mbalimbali iye pakati, pali nso kusinthana zilinganizo pakati pa sukulu za Ukachenjede za Andrews ndi Notre Dame [lomasulirdwa, Our Lady] ya chi-Katolika. Zinthu ziri chotero ma-Jesuiti ali mphindi 45 zokha kuchokera pa Andrews. Utumiki wa Achinyamata umatumiza abusa achinyamata ophunzira pa sukulupo kukatengako mbali m'zochitikachitika ku Notre Dame.

Chifukwa chiyani Mpingo wa Adventist umatumiza "Atsogoleri a Uzimu" ake ku Shalem Institute, yokhuzidwayo ndi Bungwe la Benedictine ndi chi-Buddha?

Review siikufotokoza chifukwa chimene "Atsogoleri a Uzimu" a kalasi latsopano pa Andrews amatumizidwira ku Shalem Institute komwe amaphunzitsidwa ndi a sistere, ansembe ndi akatswiri a za bongo. Wansembe Richard Rohr wa chi-Franciscan – Buddhist New Age [Satanic] ndi mmodzi wa aphunzitsi otchuka a Shalem, ndipo bukhu lotchedwa Masewero a Uzimu la Ignatius Loyola ndi limodzi la mabuku omwe amaphuzitsira ku Shalem. Shalem imalumikizananso ndi bungwe "Lozama Malingaliro [The Contemplative Socitety]" ndi lopatsa "luntha la nthawi ya zaka 1500 la "Benedikito Kutengera Kaganizidwe Kozama [Benedictine contemplative heritage]," – la Shalem Institute ya Uzimu Wokhazikika pa Miyambo ya Umunthu [Spiritual Formation].

Monga anthu akukuona kusokoneza komwe Review ikukuchita kuchionongeko cha moyo wao. Pali nkhondo yaikurutu yomwe ikuchitika; Mpingo wa Adventist ukuchita chinyengo chobisalira chomwenso chikuchitika ndi gulu la zofufuzafufuza lomwe ndi losadalirikanso, ndipo choonadi za chinsinsi chao chikunka chikukhalirakhalira poyera.

Chotontholetsa mtima ndi uthenga wamadandaulo pa interneti: "Uthenga wodandaula pa internet kuchokera kwa ziwalo zokhuzidwa za mpingo wa Adventist ukupempha mtsogoleri wa mpingowu Ted N. C. Wilson kuti athetse phunziro la Uzimu Wokhazikika pa Miyambo ya Umunthu ku Sukulu ya Ukachenjede ya Andrews. http//www.petitiononline.com/omegasda/." – contemplative Spiritual Formation in the Adventist church.

Monga ma-Adventist amaganizo abwino, koma opanda chiyembekezo'wa akuganiza kuti kuchotsedwa kwa phunziro'li kungathetse chisokonekero chomwe chikuchitikachi? Kwa zaka khumi, Uzimu Wokhazikika pa Miyambo'wu wakhala ukufalikira mosabisa ngati mliri ku zigawo zonse za mautumiki a mpingo wa Adventist: m'sukulu za ukachenjede, m'zipatala, makoleji, masekondale, m'mipingo, m'makomo, ndi m'mabanja. Mchitidwewu wafalikira pali ponse, m'chiri chonse, mothandizidwa ndi Atsgoleri a za Uzimu ophunzitsa ku sukulu ya Ukachenjede ya Shalem, ndipo tsopano ukuphunzitsidwa kwa ana m'sukulu zosiyanasiyana kuphatikiza za ukachenjede za mpingo wa Adventist komwe anawonso amautengera.

Nkhondo ya Satana yolimbana ndi mbeu yotsala ya mkazi yangotsala pang'ono kufika pachimake. Chikhalidwe cha anthu chamizidwa, kusokonezedwa ndi kulamulidwa ndi Masewero a za Uzimu a ma-Jesuiti. Chiphunzitso cha Ignatius'chi chalandiridwa ponseponse kuphatikiza m'zigawo 13 za utumiki wa Mpingo wa SDA pa dziko lonse. Mautumiki onse a Mpingowu anaulandira, - monga zingakhale zoona kuganiza kuti kuuthetsa mchitidwe wakugwawu m'chigawo chimodzi kungakhale kuuthetsa m'zigawo zonse – popanda kuti ungabulikire kuchokera ku mbali zina – zingatheke kukuthetsa kufalikira kwake kwa ngati madzi osefukia pa dzikoku, mchitidwe womwe mizu yake yazikika pansi, ndipo nthambi zake zafalikira pali ponse, ndipo moyo wake ukuchokera ku mpweya wa Fano lachirombo – womwe pano ukosokoneza mipingo ndiponso kufoketsa ndi kuthetsa maulamuliro a dziko, ndi kukhazikitsa Fano la Ulamuliro wa Upapa - makamaka wa U-Jesuiti m'malo mwao? Ndikhulupirireni, maina omwe ali pa mndandanda wa ma-Adventist omwe akuti phunziro la Uzimu Wokhazikika pa Miyambo'li lichotsedwe ku sukulu ya ukachenjede ya Andrews akutsatidwa ndi kufufuzidwa ndi magulu a ma-Jesuiti ndiponso CIA/ma-Knight a ku Malta ndi atumiki a GC. Zinthu ziri choncho, bukhu la Miyambo likuchenjeza: "Wochenjera aona zoipa nabisala; koma achibwana angopitirira, nalipitsidwa." Miyambo 22:3. Nkhondoyi yafika patali kwambiri, posati nkupafikira wamba. Munthu sumadandaula ku ofesi imene m'mbuyomu inali pansi pa Folkenberg (amene anali ndi maziko a chi-Roma) Vicariatus Urbis [kutanthauza Nthumwi yaku Mzindawo] iye analipilidwa ndalama za chi-America zookwanira myanda 8 [US$ 8,000,000] ndi GC kuti asaulule chinsinsi. Folkenberg anaopsyeza Danny Shelton wa Wailesi ya Kanema ya 3ABN ndi chilango cha imfa. Choncho mosakaika konse mndandanda wa maina a anthu omwe ali pa gulu lodandaula zakuti phunziro la uzimu wakugwali lichotsedwe posachedwapa akhala akutsatidwa ndi ma-Jesuiti, malamulo owapatsa mphamvu akangokhazikitsidwa ndipo yense wotsutsana ndi ambuye wa ma-Jesuiti'wo adzachitidwa zoopsa monga zomwe gulu'li linachitira ena onse amene anatsutsana nalo m'mbuyomu. Ngati munalemba nao dzina lanu, zindikirani kuti munalitumiza ku ofesi yomwe inathandizira kukhazikitsa Uzimu Wokhazikika pa Miyambo ku dziko lonse lapansi kudzera m'mautumiki onse a mpingo omwe anali pansi pa Ted Wilson yemwe anali wachiwiri kwa mtsogoleri wa mpingo pomwe izi zimachitika zaka 10 zapitazo. Sukulu ya Ukachenjede ya Walla Walla imafunsa onse ofuna kuyamba kuphunzira pa sukuluyo kulemba za Uzimu Wokhazikika pa Miyambo/ pomtenga prezidenti Yohane McVay, kukhala chitsanzo.

[Ndemanga zotsatirazi ndi za mlembi

wakabukuka: Zikuoneka kuti pali njira ziwiri za chitsitsimutso zomwe zikuchitika mu mpingo wa Adventist, ndiponso m'mabungwe athu a zamaphunziro: njira yoyamba ndi chitsitsimutso cheni cheni cha m'Bukhu Lopatulika ndipo yachiwiri ndi yosakaniza za m'Bukhu Lopatulika'lo ndi zikhulupiriro zachikalekale (zachikunja) zosokeretsa, zomwe ndi Machitidwe a Ziwanda, Chikatolika, Zipembedzo za Maiko Akum'mawa, Chi-Buddha, Chi-Zen, ndi zina. Ndi chitsitsimutso chachiwirichi chomwe chikudetsa nkhawa m'chi-Adventist monga bungwe lopembedza. Ellen White ananenerapo kambirimbiri za chitsitsimutso cha mbali ziwirichi, naitcha mbali yoyamba Alefa, yomwe onse obwera pambuyo pa Ellen Whiteyo analimbana nayo, pamene m'nthawi yathu ino tikulimbana ndi mbali yachiwiri yomwe iye anaitcha Omega. Ndinalandira foni kuchokera ku WW University komwe nkhondoyi yakula kwambiri. Pa msonkhano womwe unachitika pa Oct 15 zambiri zomwe zinalankhulidwa zinali zongopeka, ndi za mwano zongoonetsa kuti palibe chomwe ochita zosayenerawo akuopapo chifukwa akulimbikitsidwa ndi abusa. Mbusa wina analandira mafoni ndi ma-imelo ambirimbiri omfunsa za mazanamazana a mabuku osakhala a chi-Adventist koma a zipembedzo zachikunja ndi za ziwanda ndi mizimu yosokeretsa omwe anayalidwa pamodzi ndi mabuku a Mau a Mzimu Wachinenero kuti anthu adzigula. Kaya makolo a chi-Adventist adzamva bwanji akaturukira kuti ana ao akumaphunzitsidwa zachikunja m'masukulu athu, sindikudziwa.!

Pamene ndinali ku maphunziro a za ubusa, mbusa Torkelson, yemwe anali wachiwiri kwa prezidenti wa GC, anakonza zothana ndi amuna theka la anthu khumi ndi awiri omwe amafuna kumachita zinthu mosaopa Mulungu. Anangotsala pang'ono kukwaniritsa ganizo lakelo ku Msonkhano wa Uphungu wa sukulu ya Ukachenjede ya Andrews pamene Neal Wilson, atate wake wa Ted yemwe anali prezidenti wa GC, ndipo anali pa ulendo wa ku Russia, anamletsa Torkelson kuti asachite chiri chonse kufikira iye (Wilson'yo) atabwerako ku ulendo wakewo. Ndikutsimikiza kuti zomwe ndikunenazi ndi zoona chifukwa Torkelson anandifotokozera yekha za nkhaniyi pamene ndinali ku sukulu ya ubusa. Chotsatira chake chinali chakuti ganizo lonse la Torkelson linathetsedwa, ndipo anthu osokonezawo anasiyidwa. Chifukwa? Chifukwa prezidenti wa GC amene anaitanitsa maprezident m'zigawo omwe ndi "akenani," ake analonjeza polumbira pa mlandu wa ku Merikay Mcleod kuti Mpingo wa Adventist wasiya kulalikira modzudzula upapa pa zoipa zomwe zalembedwa m'mbiri ya dziko kuti upapawo unazichita. Abale anga, imeneyi ndi GC yomwe inalandira nthumwi ya upapa kukhala nao pa mdipiti wa Msonkhano waukuru wa GC womwe kunadzanso nthumwi zochokera ku dziko lonse kudzakhalapo.

## Mantha ndi Oopsya

Kusalingirira mwa nzeru, ndi kusachitapo kanthu mofulumira pa nkhondo tirimoyi ndi chinthu choopsya. Tinapatsidwa mabuku a Danieli ndi Chibvumbulutso kudzanso Mkangano Waukuru [Great Controversy] kutithandiza. Ndibwino kumadziwa mbali yomwe atsogoleri ali pa nkhondo ya za chinyengoyi. Iwo amaganiza kuti ndi msonkhano wa GC wa mtundu wanji womwe ankauchita? Uwu unali msonkhano womwe unachitika pansi pa utsogoleri wa Neal Wilson, atate wa Ted, komwe mpingo unalembetsedwa monga bungwe la za malonda ndipo dzina lake linatengedwa kukhala lotetezedwa [trade marked] ndi lamulo pofuna kupeza njira yowaimbira milandu ndi kukhaulitsira anthu okhulupirira ndi a choonadi eni eni. Ndi GC yomwe inakhazikitsa Bungwe la IBMTE kuti likhazikitse Uzimu Wokhazikika pa Miyambo [Spiritual Formation], pa nthawi imene Ted Wilson anali wachiwiri wa prezidenti wa komiti ya IBMTE. Ndi GC yomwe inalora nthumwi yoimira upapa kukhala nao pa mdipiti wa msonkhano waukuruwu wa mpingo wa dziko lonsewu. Ndi GC imene inapereka chilango cha Umasoni [Usatana] cha imfa kwa Danny Shelton wa 3ABN [mobisalira]. Muyenera kumadziwa momwe ikuchitikira nkhondo tirimoyi kuti mosadziwa mungapezeke muli amodzi [Gestapo] ozunza anthu olungama mwadala kapena posadziwa.

Kwezani mapemphero anu kwa Khristu, Mtsogoleri Woona wa Mpingo, osati ku GC yomwe yakodwa m'msampha wopandukira Mulungu. Ndi pemphero komanso pembedzero mwa chikhulupiriro funafunani dzanja la Wosaonekayo. Pomwepo mudzapita chitsogolo ndi kuchita chipambano m'nkhondoyi, m'mamenyedwe a Ukadaulo ndi Upangiri wochokera kwa Khristu amene anagonjetsa kale nkhondo ngati yomweyi.

Dybdahl m'bukhu lake lotchedwa "Hunger" akutilangiza, "Yang'anitsani Wosaonekayo" ndipo "Mpumireni Pemphero."

M'bukhu Hunger [Njara], p. 62, pa mutu "Lectio Divina," lodedwa ndi mpingo wa Adventist, Jon Dybdahl akufotokoza za kapempheredwe ka a Katolika.

Pa tsamba 52 la Hunger, Dybdahl akufotokoza za pemphero. Akulemba moyamikira m'modzi wa anthu amene anayambitsa chipani cha Chi-Franciscan, Francis wa ku Assisi: "Francis wa ku Assisi anapemphera mosalekeza usiku wonse pongotchula dzina lomwelo mobwerezabwereza 'Yesu, Yesu wanga.'" – Hunger, p. 52. Mchitidwewu ndi womwe Akatolika amauzidwa kuuchita popemphera rosary. Ndi mchitidwe wodzitsitsimutsa munthu yekha. Zofotokoza za Dybdahl m'Bukhu lake Hunger, Zokopedwa kuchokera m'WRM yofalitsidwa m'October 2011.

## CHIPHUNZITSO CHOSOKERETSA CHA MITU 7

Jean Handwerk

M'Chibvumbulutso 12, 13, ndi 17 Mulungu watipatsa chizindikilo cha chirombo cha mitu isanu ndi iwiri ndi nyanga khumi. Chibvumbulutso 17 chikumasulira mituyo kuti: "Mitu isanu ndi iwiri ndiyo mapiri asanu ndi awiri… ali mafumu asanu ndi awiri…" Malemba akulankhula mwachimvekere kuti phiri limaimira ulamuliro/ufumu/pfuko. Za Yuda Mulungu anati, "… Iwe phiri langa la m'munda, ndidzapereka chuma chako ndi zosungidwa zako zikafunkhidwe…" (Yer 17:1-3), ndipo za Babulo anati, "… Taona ndidzamenyana ndi iwe, iwe phiri lakuononga…" Yer. 51:24-25. Tanthauzo la Malemba ndi lofunika kwambiri. Mitu isanu ndi iwiri/mafumu/mitundu ndi maulamuliro ndi anthu omwe amatsutsana ndi mau ndiponso chifuniro cha Mulungu m'mbiri yonse ya dziko. Ellen White akufotokoza za kuti "kuuka ndi kugwa kwa mafumu,maulamuliro ndi mitundu zafotokozedwa momveka bwino m'mabuku a Danieli ndi Chibvumbulutso…" FLB 345.

Mngelo anamuuza Yohane, "Asanu adagwa, imodzi iriko, yinayo siinadze; ndipo pamene ifika iyenera iyo kukhala kanthawi" patsogolo pa ya 8th yomwe ikhale kumapeto a mbiri ya mtundu wa anthu. Danieli 2, 7 ndi 8 akuwaonetsa mafuko/mafumu anai oyambirira, ndipo mbiri ikutsimikizira za mitu isanu yoyambirira inagwayo momveka bwino kuti inali Babulo, Amedi/Aperezi, Ahelene ndi Romu Wa chikunja, kudzanso nyanga yaing'ono yomwe ndi Romu wa Upapa. Mutu wa 6,th ndi "yinayo sinadze" koma ifika pakungotha kwa ndende ya mutu wa 5th. "…Ngati munthu alinga kundende, kundende adzamuka…Ndipo ndinaona chirombo china chirikuturuka…." Chibv. 13:10-11. M'Adventist aliyense azindikire kuti chirombo chachiwiri cha Chibvumbulutso 13 chikuimira America wa Mpanduko [chi-Protestant]. Zolembera zikumfotokoza America kuti ndiye mutu wa 6th, ndipo Malembo ndi Mau a Mzimu Wachinenero akufotokoza za ulamuliro kapena "ufumu" womwe ukukwaniritsa malo a mutu wa 7th. Akuonjezerapo za Uthenga wochititsa chidwi wonena za mutu wa 8th. kuti uli mu wa 7th.

Omasulira ambiri amati ufumu/mutu wa 6th ndi ulamuliro unakanitsitsa Mulungu [Atheism]. Koma ife titanthauzira mosiyana ndi awa chifukwa sitikukhulupirira kuti ndi zoona. Inde, ulamuliro wokanitsitsa Mulungu unachitikapo ndipo ubweranso nthawi ya kumapeto kuno, koma uwo sumodzi wa mitu isanu ndi iwiri, ndipo m'zolemberazi tifotokoza zifukwa zomwe tikuutanthauzira mutu wa 6th mosiyana ndi anzathuwo.


France Wokaniratu Mulungu Sunali Mutu

M'Mkangano Waukuru [Great Controversy] 268-9, Ellen White anati, "Chakhala chiri cholakalaka cha Aroma, kulipondereza Bukhu Lopatulika osafuna anthu alidziwe, iwo analitsekera Bukhu'li m'chalankhulo chosadziwika…. Ndipo ulamuliro wina…chirombo chochokera kupompho – chinaturukira ndi kuchita nkhondo yotsutsana mwachindunji ndi mau a Mulungu." Izi zinachitika kanthawi pang'ono patsogolo pa chaka cha 1798."

Ulamuliro uwo, pokhala "chirombo," unalinso pfuko: ndipo ndi France. Ellen White analemba, "Mwa mapfuko onse ofotokozedwa mu mbiri ya Bukhu Lopatulika, Aigupto ndi ufumu umene unamkana Mulungu moonetsera ndi kukanitsitsa kumvera malamulo ake… Dziko lomwe likuimiridwa ndi dzina Aigupto linalankhulanso mau achipongwe ofanana ndi omwe analankhula Aigupto nilimkananso Mulungu ndi malamulo ake pomuukira, wosamkhulupirira komanso podzikuza… ulosi uwu unakwaniritsidwa mu mbiri ya dziko la France." Uriah Smith anachitiranso umboni pofotokoza kuti France ndi pfuko lomwe linaloseredwa m'Danieli 11:37-40 – ndiponso kuti ndi pfuko lomwe likuneneredwanso m'Chibvumbulutso 11 kuti ndi chirombo choturuka mpompho." DR 301.

Pharaoh anafunsa, "Yehova, ndi ndani kuti nditchere khutu langa ku mau ake?" Potsirirapo ndemanga pa mau odzikuzawa, Mrs White analemba, "Uku ndiko kukanitsitsa Mulungu." Koma sikukanitsitsa Mulungu komwe kunaturuka ku pompho. Kukanitsitsa Mulungu ndi "mtima wakusamkhulupirira ndi kumchitira Iye mwano" monga kunachitidwa ndi Aigupto pachiyambi; kunali "kukanitsitsa ngakhale kumva kuti kuli Mulungu wa moyo." Mchitidwewu ndi wakalekale ndithu. (OHC, 278). Ku France unali "machitidwe atsopano wotsimikizira mphamvu ya Satana. Kuchitira mwano Mulungu sikunali chirombo choturuka ku pompho; koma pfuko la anthu lochita chipongwe ndilo linali chirombo choturuka ku pompho. Choncho, munthu angathe kunena kuti mutu wa 6th unali mchitidwe wokanitsitsa Mulungu, chifukwa onse awiri, Malembo ndi Ellen White akufotokoza kuti, "choncho chirombo choturuka ku pompho" chomwe chinachita nkhondo pa mboni ziwiri chinali pfuko la anthu.

Kunali kosatheka kuti France akhale mutu wa 6th kumapeto kwa m'ma 1700, chifukwa dzikolo silinali ulamuliro wa dziko lonse, ndipo ulamuliro wake unangokhala zaka 31/2. Komabe, mbiri ikufotokoza kuti pafupi pa mapeto a zaka 1260, a Hugueot a chi-French, a Puritan a chi-Ngelezi, ndi ambiri ena anathawa nkhondo ya chipembedzo kukafuna chitchinjirizo m'Dziko Latsopano, lomwe pambuyo pake linatchedwa United States of America. Pamene upapa womwe unali mutu wa 5th unalandira bala lake la kuimfa, chirombo china chatsopano chokhala ndi nyanga ngati za mwana wa nkhosa ndi kulankhula ngati chinjoka chinaturukira nichikhala mutu wa 6th.



Apatu zikupitirira kutsimikizira kuti mitu imaimira maulamuliro a dziko ophatikiza chipembedzo ndi ndale mkati mwao.

Chosachimvetsetsa ndi chakuti, ndi chiyani chinachititsa France kudana ndi mau a Mulungu, ndi kudzetsa Kuukira kwa Chi-French kwa 1787-1799 komwe kunakhetsetsa mwazi wambiri. Pambuyo pakutsekerezedwa kwa Kukonzanso kwa Mpanduko m'France, anthu a chitukuko a chi-Huguenot anathawa... Ma-Jesuiti analowa m'dziko lomwe zonse zinaonongeka, nalamulira mipingo, masukulu, ndende ndi ntchito za maulendo a panyanja mwa mphamvu ndi mwankhanza...[Koma] m'malo mowaona [Aroma] kuti ndiwo akanapangitsa anthu khungu ndi ziphunzitso zao, anthu anaona dziko la France kuti ndilo linawapanga anthu ake kukhala osagwirizanika ndi oukira. Anali machitidwe a chi-Roma omwe ananyozetsa mau a Mulungu kuti anapindulira ansembe wokha. Anthu anadana ndi ansembe kuti ndiwo anali kuwazunza, chifukwa mulungu yekhayo anthuwo anamdziwa anali mulungu wa Aroma. Ziphunzitso za Aromawo ndizo zinali chipembedzo chao. Iwo anakutenga kuipa kwa Aroma kuti kunachokera m'Bukhu Lopatulika chotero Afransa anadana ndi Bukhu Lopatulika." GC 281.

Mapfuko okana Mulungu akunyozabe chipembedzo kuti chiri "chiyembekezo chonama" chongotsekereza njira "zachisangalalo chenicheni" (Karl Marx). Za ndondomeko ya mitu, America wa Mpanduko anali atakomana kale ndi lamulo la Sunday la Blair m'1888, Vladimir Lenin asanatembenuze zolembera za Marx ndi kuzichita, chomwe chinayambitsa Kuukira kwa Bolshevik kwa 1917 m'Russia.

## Chomwe America Sangakhalire Mutu wa 7th

Chibvumbulutso 17 akufotokoza mpfundo imodzi youzindikirira mutu wa 7th: "Ndipo pamene ifika iyenera iyo kukhala kanthawi." Ufumu wa Babulo (605-539 BC) unakhala zaka 66; wa Amedi/Aperezi (539-331 BC), zaka 163; wa Romu Wachikunja (168 BC – 476, zaka 644; wa Romu wa Upapa (AD 508/538-1798), zaka 1290 kapena 1260. Wa America wa Mpanduko unayamba kubvomerezedwa ndi dziko la France kuti ndi pfuko m'chaka cha 1798. Choncho kuyambira 1798 mpaka lero ufumu wa America ukukwanitsa zaka zoonjezerapo 213 kuposera mitu iwiri ya isanu inakhalayo usanakhale uwu. Choncho ufumuwu sukukwaniritsa makhalidwe ouyenereza "kukhala wa kanthawi kochepa."

## Zizindikilo Ziwri Zofunikira

Maufumu oyambirira anai anauka ndi kugwa pogonjetsedwa ndi anzao m'njira ya nkhondo, koma atatu otsirizawa akuthera pakuchita migwirizano wina ndi unzake. Bala la kuimfa la mutu/ufumu wa 5th lidapola, mutu/ufumu wa 6th unagwira ntchito yopoletsa balalo, mutu/ufumu wa 7th ukukopedwa ndi kulumikizana ndi mitu ya 5th ndi 6th ndi kuthandizira pokhazikitsa mutu/ufumu wa 8th ndipo cholinga chao chakhala chiri chachipambano.

Chidziwikenso, kuti chiri chonse chomwe tikuchiwerenga chokhuza chirombo/mutu m'Chibvumbulutso 13 chidzapitirira kuchitika mpaka chimaliziro cha mbiri ya mtundu wa anthu. Chirombo/mutu, cholembedwa mwachidule pa ndime 3, chikuimira ulamuliro wa upapa wa Aroma, womwe unathetsedwapo koma, "bala lake la kuimfa lidapola; ndipo dziko lonse linazizwa potsata chirombocho. "Bala lidzapola pamene munthu wakusayeruzikayu adzapatsidwanso mphamvu." Chirombo/mutu cha Mpanduko, chomwe chafotokozedwa mwachidule pa ndime 12, chidzaumiriza "dziko ndi iwo akukhala momwemo kulambira chirombo choyamba, chimene bala lake la kuimfa lidapola." Uku kudzakhala kubwezeredwanso kwa mphamvu ndi ulamuliro wa Upapa pafupi penipeni pa mapeto a nthawi ya chitetezero ya mtundu wonse wa anthu, pomwe aliyense adzakhala atachita chisankho. Chirombo/mutu chachitatu [Fano la chirombo] cha Chibvumbulutso 13 chidzalamulira kufikira chimaliziro cha dziko, monga kufotokozedwere m'munsimu.

Mutu wa 6th: America wa Mpanduko

Chibvumbulutso 13 chikutipatsa chidziwitso chokwanira za chirombo chachiwiri, chomwe ndi mutu wa 6th wa Chibvumbulutso 17, chomwe chikulamulira mu nthawi tikukhalayi. Chirombochi chinakhala ulamuliro posachita nkhondo, ndipo nchifukwa chake chikufotokozedwa kuti "chinali nazo nyanga ziwiri ngati za mwana wa nkhosa." Pakugwa kwa mutu 5th, America wa Mpanduko wofotokozedwayo, "imodzi iriko" – anali atalandira ufulu wodzilamulira kuchokera kwa Angelezi. Malamulo oyendetsera dzikolo anabvomerezedwa m'chaka cha 1787.

Nyanga ziwiri zosaopsyazi zikuimira maziko awiri a ufulu wodzilamulira ndi a Mpanduko. "'Ndikunena kwa iwo akukhala padziko, kuti apange fano la chirombo.' Apa pakufotokozedwa za mtundu wa ulamuliro momwe mphamvu yakupanga malamulo (kuchita zilinganizo) ili kwa anthu, chinthu chomwe chikutsimikiza kotheratu kuti dziko la America wa Mgwirizano [United States] ndi pfuko lomwe likufotokozedwa ndi ulosi umenewu." GC 441-2.

Wina angathe kupusitsidwa ndi maonekedwe osaopsya a chirombo chikufotokozedwachi, koma osati ndi malankhuludwe ake angati a chinjoka monga chikuchitira lero. Poyambirira, mchitidwe wa ufulu wachipembedzo wa dziko la America unapereka chiyembekezo choonetsa ngati silidzalora machitidwe a upapa, koma mkupita kwa nthawi, "Ngakhale anadzionetsera ngati otsatira Mwanawankhosa wa Mulungu, anthu a dzikolo anadzazidwa ndi mzimu wa usatana. Iwo anadzitcha anthu abwino ndi odzichepetsa, chikhalirecho malamulo a dziko lao akulimbikitsa machitidwe a mzimu wa Satana, nauonetsera uwu m'zochita zao kuti akutsutsana kotheratu ndi zomwe iwo amadzifotokoza kuti ali... Anthu akakana kupondereza malamulo a Mulungu pansi pa mapazi ao, chinyengo cha Satana chimaikidwa pambalambanda." Mar 191. "Atsogoleri a bungwe lokweza Sunday....akubisa chinsinsi chenicheni cha zomwe zikuchitika, ndipo ambiri omwe akutsatira zochita za anthu osokeretsawa sakudziwa chomwe akuchitsatira ndi komwe chikuwatsogolera. Kudziphatika ku mchitidwewu kukukhala ngati chinthu chabwino komanso chachikhristu pamaso, koma pamene malamulo oukakamiza adzakhazikitsidwa udzaonekera kuti ndi wa chinjoka." Ellen White akufotokoza kuti "Mchitidwe wa Mpanduko ukuyendetsedwa ndi mphamvu yochokera ku pompho." Mar 187.

Kunalibe ufulu wa chipembedzo kwa anthu oyambirira, kenaka unaperekedwa m'Malamulo Oyambirira Oyendetsera dziko la America, nubetcheredwa m'1888 m'lamulo la Blair ndi "malamulo a mtambo," kenaka unabetcheredwanso ndi umodzi wa zipembedzo, zikhulupiriro-zosiyanasiyana, kuyendera maprezidenti kwa papa, komanso Khothi Lalikuru, ndi machitidwe ena – machitidwewa anatsogolera dziko la U.S. ku lamulo la Sunday. M'malo osiyanasiyana, Mau a Mzimu Wachinenero akufotokoza kuti dziko la Mgwirizano la Amerika ndi chirombo, ndipo uchirombo wa dziko'li umaonetsedwa m'machitachita ake a chipembedzo, monga, "bungwe la za Sunday," "Mpanduko," "mphamvu za chipembedzo," "mipingo," Amerika wa Mpanduko." M'machitidwe onsewa, chinjoka chakhala chikulankhula m'Amerika kwa nthawi yaitali. Ndipo posachedwapa chitero mobangula.

Chirombo chachikunja chofiira cha Chibvumbulutso 12 chinapatsa Romu wa upapa "mphamvu [ya usatana] yake, komanso mpando [wa usatana] wake, ndi ulamuliro waukuru," ndipo Amerika wa Mpanduko achita "ulamuliro wonse wa chirombo choyamba [Romu wa upapa] pamaso pake. Pakutero ulamuliro umodzi womwewo ugwira ntchito zake m'maulamuliro angapo.

America wa Mpanduko alambiritsa "dziko ndi iwo akukhala momwemo chirombo choyamba chimene bala lake la kuimfa lidapola" chomwenso chikuonetsera poyera chikoka cha Amerika wa Mpandukoyo ku dziko lonse ndi cholinga cholibweretsa dziko lapansi'lo kukutumikira ulamuliro wa chirombo wa chi-Roma unakhalawo kale ndipo wakhazikitsidwanso. Pakali pano, palibe nkhanza kapena kukakamiza kuli konse komwe kukuchitika. Monga pa Chibvumbulutso 12, chinjoka chofiira chachikuru "chinasokeretsa dziko lonse lapansi," osati mwankhanza chomwechonso pa Chibvumbulutso 13 America wa Mpanduko "akusokeretsa iwo akukhala padziko" kuti alambire (amvere) chirombo choyamba osati mwa nkhanza ndi mokakamiza. Koma motani? "Pogwiritsa ntchito zizindikilo zimene anachipatsa mphamvu yakuzichita pamaso pa chirombo." Bukhu la 3SM 408 likuti, Kwalembedwa m'Mau a Mulungu kuti mdaniyo adzagwiritsa ntchito atumiki ake omwe adzakhala atachoka m'chikhulupiriro cha choonadi, ndipo iwo adzachita zizindikilo, ngakhale kutsitsa moto uchokere m'mwamba nugwe padziko, pamaso pa anthu."

Zozizwa zochitika m'machenjerero a usatana zidzakhala njira yokhayo yowakakamizira ndi kuwasokeretsera anthu okhala padziko kuti "apange fano la chirombo, chimene chinali nalo bala la lupanga nichinakhalanso ndi moyo." Zozizwa za chinyengozi zidzapatsa mphamvu America wa Mpanduko kukhazikitsa malamulo olimbikitsa chipembedzo ndi kumvera ulamuliro wa upapa kuyambira pa pfuko, kenaka mgwirizano umodzi wa maiko ndiponso umodzi m'kapembedzedwe.

Chinyengochi chidzachita chipambano. Mabvuto a zachuma, ndale ndi kusintha kwa nyengo, kudzanso umbuli wa mau a Mulungu, zidzapangitsa anthu ankhaniankhani okhuzidwa ndi zowawazi kutembenuka ndi kubvomereza machitidwe a ziwandawa. Chotsatira chake chidzakhala kukhazikitsidwa kwa lamulo la Sunday; America wa Mpanduko adzanyoza ndi kukana malamulo ndi ukuru wa Mulungu. Chibvumbulutso 13:15 chikufotokoza momwe fano la chirombo lidzakhazikitsidwire: "Ndipo anachipatsa mphamvu yakupatsa fano la chirombo mpweya, kutinso fano la chirombo lilankhule, nilichite [lipangitse]...." Umu ndimo udzakhazikitsidwire ulamuliro wamphamvu wamgwirizano wa mpingo-ndale womwe udzazunze ndikuyesetsa kuonongeratu mpingo wotsala wa Mulungu.

A Mpanduko Oukira a America Wa Mgwirizano [United States] akhala akukhazikitsa mgwirizano wamphamvu wachikoka m'magawo onse atatu oyendetsera boma la dzikolo kuti



magawowo agwirizanenso ndi zolinga zao pa chipembedzo. Kumapeto kwenikweni, "pofuna kutchuka ndi kubvomerezeka ndi onse, aphungu a dziko'lo adzagonjera zofuna a Mpandukowo nakhazikitsitsa lamulo la Sunday..." Ichi chidzakhala chiyambi cha mapeto a "mkangano waukuru wotsiriza wa choonadi ndi uchimo." 5T 451.

### Mutu wa chi-7th

Kuti timvetsetse bwino za makhazikitsidwe a ulamuliro wa mutu wa chi-8th, tifunikira kudziwa ndi kumvetsetsa bwino za mutu wa chi-7th, womwe wafotokozedwa kuti "inayo siinadze; ndipo pamene ifika iyenera iyo kukhala kanthawi." Ndi ulamuliro uti, pfuko kapena ufumu uti womwe Malemba akunena za iwo, kuti udzalumikizana ndi zolinga za upapa (mutu) wa 5th ndiponso Mpanduko waukira (mutu) wa chi-6th, womwe udzaichita "ntchito yonyansitsayi" yolunzanitsa mchitidwe wa zipembedzo zosiyana zwirizi? Ulamulirowu watchulidwanso pa Chibvumbulutso 13, ndi kufotokozedwa pa Chibvumbulutso 17-19. Koma magwero ake akupezeka pa Chibvumbulutso 16:13. Apa tikuwerenga za mgwirizano wopangidwa ndi magawo atatu wopandukira, " Mgwirizano wa utatu" womwe wakhala ukugwira ntchito yokhazikitsa ulamuliro wa chi-8th womwe ndi wotsirizira wa dziko.

"Ndipo ndinaona moturuka m'kamwa mwa chinjoka, ndi m'kamwa mwa chirombo, ndi m'kamwa mwa mneneri wonyenga." Magawo onse atatuwa akulamulidwa ndi ziwanda. GC 588 likuwafotokoza magawo atatu ogwirizanawa ndi pochiika cholinga cha mgwirizano wao poyera: "A Mpanduko aku United States adzakhala patsogolo pa onse kutansa manja ao ndi kugwirana ndi dzanja la mizimu ya ziwanda; ndipo awiriwa adzatansa manja ao ku pompho kugwirana ndi mphamvu ya upapa wa Aroma; ndipo pansi pa chikoka ndi chikakamizo cha mgwirizano wa utatu wao, dziko lino lidzayenda m'machitidwe monga unachitapo ulamuliro wa upapa wa Aroma wopondererza ufulu wa chipembedzo wa anthu."

Chipembedzo cha Satana chakhazikika m'Chikatolika, ndi m'Mpanduko Woukirawo. Bodza lake lakuti mzimu umakhala myaya, ndiponso lakuti akufa amakhalabe ndi moyo m'manda mwao, lamanga nthenje m'mabungwe a chipembedzo awiriwa. Mvetsetsani kuti apatu chipembedzo cha Satana chikutchulidwa pa chokha osaphatikizidwa ndi ziwirizo, komanso molekanitsidwa ndi mgwirizano wa Chiyuda-Chikhristu.

M'zolembera zotsatirazi, timvabe za mgwirizano wa utatu wafotokozedwapo pamwambawu: "Alonda oima pa malinga a Ziyoni asaphatikizane nao... ndi mgwirizano wonyoza, wa upapa ndi a Mpatuko oukira, wokweza miyambo koposa Malemba, nzeru za umunthu koposa mabvumbulutso a choonadi, luntha la umunthu kuposa chikoka ndi mphamvu za Umulungu." RH March 24, 1896. Awa ndi anthu onyoza osapembedza Mulungu m'choonadi, koma monga mwamachitidwe a onse otsatira upapa ndi a Mpanduko akugwa. Omwe kwa iwo, kupembedza Mulungu ndikupatsa ulemu zolengedwa, munthu, maganizidwe a mizimu – ngati kuti Mulungu kulibe konse. Kwa iwo chipembedzo ndi kukhulupirira mizimu ya akufa ndi ya ziwanda, chikunja, kupenduza, chipembedzo cha Satana, ndikutsimikizitsa kuti kulibe Mulungu komanso kupembedza mafano.

Chipembedzo cha mizimu chalunzanitsa "anthu okana Mulungu," Akatolika ndi a Mpanduko osalungama kupanga umodzi wa utatu." "Pakuti ali mizimu ya ziwanda zakuchita zizindikilo; zimene zituruka kumka kwa mafumu a dziko lonse kuwasonkhanitsira ku nkhondo ya tsiku lalikuru la Mulungu Wampahamvuyonse." "Mizimu ya ziwanda" zakuchita-zozizwa, ikaturuka "kumka kwa mafumu" imagwira ntchito "kuwasonkhanitsira" iwo kumabvuto a za ndale ndi a za chuma cha dziko. Cholinga? Kugwiritsa ntchito mafumuwo ndiponso chikoka ndi zonse ali nazo pakukhazikitsa ufumu wa chi-8th, wa mgwirizano wa chipembedzo-ndi-ndale womwe ukhale wa dziko lonse, wopangidwa ndi chipembedzo-chimodzi chophatikizana ndi boma-limodzi, ndipo ukutchedwa boma-chipembedzo la pamalo ponse. Ulamuliro wa chipembedzo pawokha sungachite kanthu, umafuna mphamvu ina kuchokera kunja youthandizira kukwaniritsa cholinga chake, ichi nchifukwa chake pakhazikitsidwa mphamvu yokopera "mafumu" alowe mumgwirizanowo pogwiritsa ntchito chinyengo cha zozizwa.

Mau a Mulungu akufotokoza za maulamuliro opsinjidwa ndi mabvuto a zachuma ndi za ndale, m'mau akuti nyanga/mafumu khumi. Iwo akudziwikanso kuti ali m'kati mwa mutu/chinjoka wa chi-7th. "...Mafumu ndi olamulira ndi ziwanga adzadzisankhira okha mzimu wakukana Khristu, ndipo mu umodzi wao adzadziwikanso ndi dzina la chinjoka chomwe chikunka chikuchita nkhondo ndi oyera mtima..." (MT 38.) "...Anthu osalungama adzadzipereka kukukhulupirira mabodza, machenjerero ndi chinyengo chachikuru, chowatsogolera kuchionongeko. Anthuwa adzadzibveka ndi chobvala chakuunika, kuti akanyenge ngati nkotheka osankhidwa omwe." (PM 389) "'Ndipo chinjoka chinakwiya ndi mkazi, nichichoka kunka kuchita nkhondo ndi otsala a mbeu yake, amene asunga malamulo a Mulungu, nakhala nao umboni wa Yesu.' Posachedwapa tikhala tikuona mau awa akukwanitsidwa kotheratu pamene mipingo ya Mpanduko idzachita mgwirizano ndi dziko lapansi komanso ndi ulamuliro wa upapa womwe udzalimbana ndi onse akusunga malamulo." 5T 449. Nyanga/mafumu khumi "alandira ulamuliro ngati mafumu, ora limodzi pamodzi ndi chirombo" ndipo "adzachita nkhondo pa Mwanawankhosa." "Ndipo ndinaona chirombocho, ndi mafumu a dziko, ndi magulu a nkhondo ao, osonkhanidwa kuchita nkhondo pa Iye wakukwera pa kavalo ndi gulu la nkhondo lake." Kupatula kagulu kakang'ono ka "osankhidwa omwe," koma dziko lonse lapansi pa nthawiyi lidzakhala pamgwirizano wotsutsana ndi boma la Mulungu ndi anthu ake. Mkati mwa zochitika izi ufumu wa chi-8th udzakhazikitsidwa.

Koma mutu/ nyanga khumi wa chi-7th "iyenera iyo kukhala kanthawi kochepa [kokha]" Zochitika za kumapeto kuno zikhala zothamanga kwambiri, ndipo pamene "Mwanawankhosa adzawalaka," adzazindikira iwo amene amalimbana Naye. Pomwepo "adzadana ndi mkazi wachigololoyo..."

### Chifukwa Ninji Nyanga Khumi ndi Zosaphatikizana

Nyanga khumi za chirombo cha mitu isanu ndi iwiri zikuimira ufumu wa chi-7th, koma zikuonetsedwa ngati nyanga, osati mutu umodzi. Ichi ndi chifukwa chakuti nyangazi si ufumu umodzi kapena chirombo chimodzi koma maulamuliro angapo okhala pa mgwirizano. Ufumu uli wonse pa wokha, ulibe mphamvu yokhala ulamuliro wa dziko lonse. Chibvumbulutso 17 chikukufotokoza za kupangidwa kwa mgwirizano wa maulamulirowa kuti uli "ufumu" umodzi woimiridwa ndi mutu wa chi-7th. Kukhala kwao a "mtima umodzi," kukufotokozedwa kuti "apereka mphamvu ndi ulamuliro wao kwa chirombo" kutanthauza mgwirizano wochitira zinthu limodzi mosatsutsana, chinthu chomwe chikupanga tanthauzo la ulosiwu kumveka bwino.

Nyanga khumi zikukumbutsa kugawidwa m'maufumu khumi kwa ufumu Wakumadzulo wa Aroma. Izi zikuonetsa kuti dziko lapansi ligawidwanso m'migwirizano ya "m'zigawo" zokhala ndi mafuko angapo mkati mwake omwe adzapereka mphamvu ndi maulamuliro ao pansi pa mtsogoleri wamgwirizano umodzi. Chenicheni chichitike sichinadziwike bwinobwino panopa, koma mgwirizano wa Maiko aku Ulaya [European Union], womwe unayamba ngati wonyozeka wa zamalonda chabe pakati pamaiko okhuzidwa, ukhale chitsanzo chathu. Pano mafuko onse amumgwirizano'wo apereka maulamuliro ao ku bungwe la Mgwirizano wa Maikowo [ European Commission]. Ndi chopepuka kuyendetsa/kulamulira mabungwe a migwirizano ya mafuko kudzera m'bungwe limodzi kusiyana ndi kuyendetsa/kulamulira mafuko iliri lonse palokhapalokha. Yosefe Stalin anati, "Tiligawe dziko lapansi m'zigawo ngati njira imodzi yokonzekera boma limodzi la dziko lonse. Tikatero anthu adzasiya kumvera maulamuliro a m'maiko ao ndikuzolowera maulamuliro am'zigawo, ngakhale sichapafupi kuti adzamvere ulamuliro umodzi wa dziko lonse. Koma, pang'ono ndi pang'ono maulamuliro a m'zigawowo adzalumikizidwa m'ulamuliro umodzi wamphamvu ndi wokakamiza." (Maxism and the National Question).

M'dziko la Mgwirizano la Amerika, bwalo la milandu la dziko lonse lokhazikitsidwa pansi pa NAFTA [N. Am. Free Trade Asso., momwe muli Canada, Mexico, U.S.]... likumalamulanso milandu ya m'U.S., pokhala la mphamvu zoposa mabwalo a mu U.S." (Wm. Jasper, CAFTA [Central Am. FT]: The Stepping American, May 17, 2004. 32-5. Polankhulapo za NAFTA, Prezidenti wakale wa Mexico, Vincente Fox anati, "Cholinga chathu chachikuru ndikukhazikitsa mgwirizano pakati pathu monga uli wa Maiko aku Ulaya [European Union]." Mtsogoleri wakale wa Nyumba ya Malamulo (U.S.) Newt Gingrich, polankhula za NAFTA ku bungwe la House Ways ndi Means Committee, anati, "Tiyenera kunena mosabisa zakusintha kwathu kuchoka mu ulamuliro wa Mgwirizano wa Maiko [United States] kulowa mu wamgwirizano watsopano.... Mgwirizano watsopanowu si wa za malonda wokha.... Komanso wakusintha kwakukuru m'kayendetsedwe ka ndale ." Kukuza kwa NAFTA kukhala Malo Ochitiramo Malonda Osalipitsana Misonkho kwa a America onse [Free Trade Area of the Americas (FTAA)] yakhala iri nkhani yaikuru mu ulamuliro wa mtsogoleri wakale wa dziko la America G.W. Bush. Ukanatheka, Mgwirizanowu ukanalunzanitsa maiko onse a chigawo cha Kumadzulo kwa dziko lapansi m'mapangano/umodzi pa chuma. Mwa chitsanzo, m'January 2005 atsogoleri [CEOs] chikwi amphamvu kwambiri – "mafumu a dziko lapansi" – anakomana ndi atsogoleri opanga malamulo ndi ndondomeko zoyendetsera maboma a dziko lapansi ku msonkhano wa pachaka wa Zachuma Wa Dziko Lonse [World Economic Forum]. M'chaka chimenecho, atsogoleriwo anaphunzitsidwa za kayendetsedwe ka "boma limodzi la dziko lapansi" – yomwe inali njira yowakonzetsera za mgwirizano wa maboma ndiponso ntchito za malonda wa amitundu onse.

Malo sakulora kufotokoza mbali yomwe bungwe la Mgwirizano Wa Maiko [Unite nations] likuchitapo pa nkhaniyi. Anthu ena amati bungwe'li ndilo mutu wa chi-7th. Werengani zomwe ena analembapo pampfundoyi: "... Pa July 9, 2001... atsogoleri a Africa anakhazikitsa mgwirizano wina: Africa Mmodzi [African Union]...Ngakhale unakanidwa ndi ena a

mapfuko a m'Africa, unadzabvomerezedwa poona kuti mbali zina za dziko lapansi zikukhazikitsanso migwirizano yaikuru pa chuma, choncho atsogoleri a Africa anagwirizananso pofotokoza kuti pofuna kuti liu lake limveke pa mabvuto a za chuma ku dziko lapansi, Africa akhale m'modzi…. Mlembi wa UN Khofi Annan analimbikitsa atsogoleriwa kuthetsa kusagwirizana kwao ndi kugwirira limodzi ntchito yolimbana ndi umphawi, nkhondo ndi mabvuto a za umoyo. 'Ganizo losaiwalika m'mbiri ya dziko'li linafunika utsogoleri, chilimbiko ndiponso kudzipereka posiya machitidwe achikalekale ngati Africa akufuna kukhala monga wachitira Mgwirizano wa Maiko aku Ulaya [European Union] ku Ulayako,' anatero Annan. Pa nthawiyi nkuti dziko lapansi likugawidwa m'maufumu khumi malingana ndi zolembera za Bungwe la Romu m'1973, zomwe mutu wake ndi wakuti, Regionalized and Adaptive Model of the Global World System [Kukhazikitsidwa m'Zigawo ndi Kukhala Chitsanzo m'Kachitidwe Kazinthu m'Dziko Lonse]. Pano chochitikachi chikukwanitsidwa m'United Nations pamenedi zigawo zayambanso kukhazikitsa migwirizano ikuruikuru pachuma potsanzira Mgwirizano wa Maiko aku Ulaya…." (Michael Coffman, Globalists evision 10 world kingdoms. Online, April 4, 2010.) Maiko a America wa Kumwera akhazikitsa kale "mgwirizano wao," ndipo migwirizano ina inai kuchokera zigawo zina ikuyembekezeka posachedwapa.

## Fano la Chirombo: Mutu wa chi-8th.

Ulamuliro wamphamvu kwambiri wachitatu wa Chibvumbulutso 13 wopangidwa pophatikizana ndale ndi chipembedzo ndipo ukutchedwa – "fano la chirombo" uwu ndiwo wa chi-8th, ndipo uli mwa "zisanu ndi ziwirizo." Uwu ndiwo ukufotokozedwa kuti, "chirombocho chinaliko, ndi kulibe, ndipo chiriko" ndi umene udzakhazikitsa malamulo ankhanza monga mwa chifuniro cha chinjoka, chirombo ndi mneneri wonyenga. Tikuzindikira kuti fano la chirombo ndi mutu wa chi-8th chifukwa ndi uwu womwe upangitse kuti "onse osalilambira fano la chirombo aphedwe." Lamulo la imfa lidzaperekedwa mu nthawi ya miliri isanu ndi iwiri yotsiriza. Sipadzakhalanso ulamuliro uli wonse padziko lapansi pambuyo pa uwu. Iyi idzakhala nthawi yotsiriza ya Satana yodziyesa kuti ali mfumu yaikuru ya dziko lapansi.

B.J. Wilkinson mu Truth Triumphant, 385, akulifotokoza fano la chirombo kuti ndi mutu wa chi-8th: "Mpingo wa m'masiku otsiriza udzadutsa m'mkwiyo ndi chizunzo cha fano la chirombo, lomwe lidzapangidwa ndi mgwirizano wa chipembedzo ndi ndale za dziko, kapena kuti kupola kwa "bala lakuimfa la chirombo." Chibvumbulutso 17:1-6 likufotokoza za chiweruzo chirinkudza cha "amai wa mipingo yonse yachiwererwere", yemwe kumapetopeto adzapezeka "woledzera ndi mwazi wa oyera mtima" ndi…wa mboni za Yesu," wokhala ndi chikho "chodzala ndi zonyansitsitsa za chigololo chake," m'dzanja lake ndiponso wokhala pa chirombo chofiiritsa cha ulamuliro wa kupha "chodzala ndi maina amwano."

Fano la chirombo sikubwereza kwa mutu wa chi-5th womwe ukuimira ulamuliro wophatikiza zachipembedzo ndi ndale wakale wa upapa wa Aroma. "Chirombo choyamba [cha Chibvumbulutso 13] ndi Mpingo wa Aroma, womwe umadzionetsera ngati wa umulungu koma uli ulamuliro wa dziko, wokhala ndi mphamvu yakuononga onse akutsutsana nawo. Fano lachirombo likuimira mchitidwe wina wa chipembedzo wodzionetseranso ngati momwe umachitira Mpingo wa Aroma." 4SP 277. Mchitidwewu ukupangidwa ndi mipingo ya Mpanduko yomwe yagwirizananso ndi maulamuliro a ndale. "Pamene mipingo yotchuka yaku United States, idzagwirizana ndikutsatira ziphunzitso zofananirako komanso za chikunja, idzaumiriza boma kupanga malamulo okhwima othandizira kuti mipingoyo isasweke, pomwepo America wa Mpanduko adzapanga fano la ulamuliro wa upapa wa Aroma…." GC 88 445. Atsogoleri a bungwe la Sunday "sakudziwa kuti ngati boma la Mpanduko lingasiye malamulo afulu omwe lakhala likuwatsata, ndikumpanga Amerika mtundu wa ufulu, ndikudzera m'malamulo omwe iwo angalikakamize kuwakhazikitsa momwe mungadzakhale lamulo lokweza bodza la upapa ndi machitidwe ake osokeretsa, pomwepo iwo adzagwanso m'msampha wa mchitidwe woipa wa Aroma unakhalawo m'Nthawi ya Zaka za Mdima [Dark Ages]. RH Extra, Dec. 11, 1888. "…Anthu a dziko liri lonse adzakakamizidwa kutsatira chitsanzo chao…. Anthu a mitundu ina adzatsatira chitsanzo cha United States. Ngakhale dzikolo lidzangoyambitsa, koma chotsatira chakuipa kwake chidzagwera anthu kumbali zonse za dziko lapansi. Mar. 214.

"Fano" la chirombo cha chi-Roma lidzakhala ndi mphamvu zazikuru. "Mu mkangano womwe uchitike m'masiku otsiriza ano pakhala mgwirizano, wotsutsana ndi kuzunza anthu a Mulungu, womwe wapangidwa ndi maulamuliro onse akugwa ndi oukira malamulo a Mulungu. Mpfundo yaikuru pomwe padzakhazikikapo mkangano wao ndi ya lamulo la chinai la Sabata la lamulo…." 7BC 983. "Chizunzo ngati chomwe chinachitidwa ndi Aroma pa anthu a Mpanduko, ndipo chinangotsala pang'ono kuthetseratu chiphunzitso cha Yesu Khristu, chidzakhala chachikuru ndi chopsyetsetsa pansi pa mgwirizano wa a Mpanduko akugwa ndi upapa." Mar. 194. "Ndipo onse akufuna kukhala opembedza m'moyo mwa Khristu Yesu, adzamva mazunzo." 2 Timoteo 3:12.

"… 'Ali nao mtima umodzi.' Padzakhala mgwirizano wa dziko lonse lapansi, umodzi waukuru, mgwirizano wa mphamvu za Satana…mgwirizano ngati womwe unachitikapo kale, mgwirizano wozunza komanso wotsutsana ndi ufulu wachipembedzo – woletsa kupembedza Mulungu monga chikufunira chikumbumtima cha munthu – mchitidwe womwe unachitidwapo ndi upapa." "… Atsogoleri a chipembedzo ndi a ndale agwirizana kale zokakamiza kusunga Sunday…" Lamulo lomwe lidzaperekedwa ndi olamulira osiyanasiyana a Chikhristu lotsutsana ndi onse osunga malamulo a Mulungu lidzachotsa chitetezo cha boma pa olungama, ndikuwasiya opanda chowateteza m'manja mwa iwo ofuna kuwaononga…." LDE 136-8.

Mitu Yotsiriza Itatu Igonjera wa chi-8th

Uli wonse wa mitu itatu yotsiriza upereka ufumu wake ku ulamuliro wa chi-8th. "… Pansi pa mutu umodzi – ulamuliro ngati wa upapa [fano la chirombo] – anthu adzagwirizana kutsutsana ndi Mulungu chinthu chomwe chichitike kudzera potsutsana ndi mboni za Mulungu. Ndi mphamvu iti yomwe idzapereka ulamuliro wake ku ulamuliro uwu? Mphamvu ya Mpanduko, ulamuliro womwe, umadzionetsera ngati wa umulungu ndiponso nkhosa ndi ngati wolumikizana kwatunthu ndi Kumwamba, udzalankhula ngati chinjoka." Mar. 187.

Chibvumbulutso 17: "Ndipo nyanga khumi…alandira ulamuliro ngati mafumu, ora limodzi, pamodzi ndi chirombo. Iwo ali nao mtima umodzi ndipo apereka mphamvu ndi ulamuliro wao kwa chirombo."

"Ndinaona m'masomphenya kuti chirombo cha nyanga-ziwiri chinali ndi pakamwa ngati pa chinjoka, ndikuti mphamvu yake inali m'ulamuliro wake, ndi kutinso lamulo [la Sunday] lidzaperekedwa kuchokera pakamwa pake. Ndipo ndinaona Amai wa Achigololo onse; kuti iye sanali ana ake a akazi, koma wosiyana ndi iwo. Iye anali atachitapo kale mbali yake, ndipo pano ana ake a akazi omwe ndi mipingo ya Mpanduko, ndiwo inali nthawi yao yakutengeko mbali pochita monga mai wao anazunzirapo oyera mtima kale. Ndinaonetsedwa kuti pamene maiyo anali kunka akutha mphamvu, mphamvu za ana akewo zinakulirakulira. Ndipo posachedwa awa azingwiritsa izi ntchito potsutsana ndi kuzunza oyera mtima monga anachitira mai wao pachiyambi.

"Ndinaona mpingo wofoka pa chikhulupiriro ndi a Adventist ofokanso… kuti adzatipereka ife kwa Akatolika ndi kubvomerezana nao potsutsana ndi choonadi. Oyera mtima panthawiyi adzadedwa, kunyansitsidwa, ndi kusabvomerezedwa ndi pang'ono pomwe ndi Akatolika; ndipo mipingo yakugwa ndi a Adventist ofoka chikhulupiriro omwe adzakhalanso akudziwa za chikhulupiriro ndi chiphunzitso chathu…adzawapereka oyera mtima kwa Akatolika powanenera zonama kuti oyerawo akukana kubvomereza ziphunzitso zobvomerezeka ndi anthu onse; iwo adzati oyerawo akutero, chifukwa akupitiriza kusunga Sabata loona ndikukana kusunga Sunday.

"Akatolika adzalimbikitsa a Mpanduko kupitabe chitsogolo, ndikukhazikitsa lamulo lakuti onse okana kusunga tsiku loyamba la pa mulungu, m'malo mwa tsiku la chsanu ndi chiwiri, aphedwe. Ndipo Akatolika omwe chiwerengero chao ndi chachikuru ndithu, adzakhala kumbali ya a Mpanduko akugwawo. Pakutero Akatolikawo adzapereka mphamvu yao ku fano la chirombo. Pomwepo a Mpanduko adzaganiza zochita monga anachitira mai waoyo iwo asanakhale; kupha oyera mtima. Koma lamulo lao lisanagwire ntchito kapena kubereka chipatso, oyera mtimawo adzapulumutsidwa ndi Liu la Mulungu." SpM, 1-2.

A Mpanduko ogarukirawo, poiwala cholinga chao cha Kukonzanso [Reformation], adzakhala patsogolo kuzunza mpingo wotsala wa Mulungu. "Mau a Mulungu akufotokoza kuti upapa udzakhalanso ndi mphamvu za ulamuliro zomwe zinauchokera, ndiponso akuti chizunzo chopweteka ngati kuotcha kwa moto chidzayambitsidwanso kudzera m'kubvomerezedwa kwa upapawo ndi iwo odzitcha a Mpanduko adziko lapansi chifukwa chakuiwala." Mar. 194. "Ndipo onse okana lamulo la umunthu ndi kusachita zofuna za malamulo a dziko, okana kukweza sabata lopangidwa ndi munthu wakusayeruzika [wauchimo], ndi kukana kunyoza malamulo oyera a Mulungu, sadzalandira mkwiyo wachizunzo wa upapa wokha, komanso wa fano la chirombo lomwe ndi a Mpanduko a dziko lapansi." Mar 214. "Panopa Satana wagwirizana ndi a Mpatuko komanso upapa…" Mar 191.

## "Kuchuruka kwa" Zozizwa za Bodza

Ndi chiyani chomwe chionjezere mphamvu ku mabungwe otsutsana ndi anthu a Mulungu? Pamene Amerika " adzanyozera liri lonse la Malamulo oyendetsera dziko'lo…nadzayamba kusintha awa ndi kutsatira machitidwe osokeretsa ndi a bodza a upapa, pomwepo ife tikhale tcheru ndi kuzindikra kuti nthawi yakwana yakuti Satana achite zozizwa za upandu wake moonjezera ndiponso kuti nthawi yachimaliziro yayandikitsitsa." Mar 216. "Njira ikukonzedwa, yakuti zozizwa, zichitike moposera muyeso, zozizwa zomwe ngati nkotheka, Satana asokeretse nazo ngakhale osankhidwa omwe." 5T 449.

"Ziwalo za mpingo zimakonda zinthu zomwe dziko limazikondanso, ifenso tikuoneka ngati tikusirira titalumikizana nao; Satana wachirimika kulumikizitsa mbali ziwirizi kukhala imodzi, kuti pakutero chipambano chake chifalikire kudzera m'mphamvu ya ziwanda. Achipembedzo cha upapa, chomwe chimadzitamandira

ndi machitidwe a zozizwa kuti ali chizindikilo chakuti mpingo ndi wa chooonadi, akusokeretsa anthu mosabvuta ndi machenjerero a zozizwa'wa; ndipo a Mpanduko posiyana ndi chitchinjirizo cha choonadi, akusokeretsedwanso. A chipembedzo cha upapa, a Mpanduko ndiponso okonda za dziko pamodzi ali ndi maonekedwe a chipembedzo koma mphamvu yake adaikana, ndipo chifukwa chakusokeretsedwako iwo autenga mgwirizano waukuruwu ngati njira yolitembenuzira dziko lapansi, ndikulilowetsa m'chikondwerero chosatha cha zaka chikwi chomwe chakhala chikuyembekezedwa." GC 588.

Atumiki a Mulungu…kuchokera malekezero ena a dziko kufikira ku anzake adzafulumiza kulalikira uthenga wochokera kumwamba… Zozizwa zidzachitidwa, odwala adzachiritsidwa, ndipo zizindikilo ndi zozizwa zidzatsatira okhulupirira. Satana nayenso adzagwiritsa ntchito zozizwa za bodza, ngakhale kutsitsa moto kuti uchokere m'mwamba nugwe padziko, pamaso pa anthu. Chibv. 13:13. Umu ndi momwe anthu a dziko lapansi adzapange chisankho chao." PM 390.

Satana, kudzera mwa atumiki ake a umunthu ndiponso a mizimu ya ziwanda, akuchita zozizwa m'malo mwa chirombo chogarukira Mulungu cha Mpanduko, chomwenso chikudziwikanso kuti chiri "mneneri wonyenga wakuchita zizindikilo" pamaso pa chirombo choyamba "zimene anachipatsa mphamvu yakuzichita kuti chisokeretse iwo akukhala ndi lemba la chirombo." Zozizwa izi ziri ndi mphamvu yakupangitsa " iwo akukhala padziko" kuti apange fano la chirombo. "Ndipo [Satana] adzawasokeretsa iwo akukhala padziko, kudzera m'zozizwa zomwe anali nayo mphamvu yakuzichita…" (Chosangalatsa nanga, iwo amene ngakhale pano "ali amodzi m'malo a m'mwamba" nadalira kotheratu Mau a Mulungu, sadzasokeretsedwa konse. Aefeso 2:6).

"Uthenga wochokera ku mizimu ya ziwanda za chipembedzo cha Satana ndi wakuti Mulungu wazitumiza izo kudzawatsimikizira anthu onse okana Sunday kuti akulakwa… Chilango chachikuru ndi choopsya chiwagwera onse okona umboni wa ziwandazo." "Izo zachotsa mwai ndi ufulu wathu wakuti nkugula kapena kugulitsa ndikufotokoza motsindika kuti tidzakhala aumphawi

# CHIKUNJA CHICHITA MAZIKO M'CHI–ADVENTIST

wosaneneka ndiponso ozunzika. Ziwandazo zikupitiriza kufotokoza moopsyeza kuti sizikudziwa momwe ife tingakhalire popanda kugwirizana ndi dziko lapansi; takhala tikudalira dziko lapansi m'moyo wathu wonse, choncho tiyenera kugonjera ku miyambo, makhalidwe ndi malamulo a dzikolo, apo zii tichoke mu ili. Ngati tikudziona kuti ndife anthu okhawo omwe Mulungu amatikonda, tizindikire kuti zinthu zoipitsitsa ndi zowawa zosaneneka zitsutsana nafe. Ziwandazo zikufotokozanso kuti ziri ndi choonadi, ndipo nchifukwa chake zikutha kuchita zozizwa, komanso kuti angelo akumwamba akumalankhula nazo mwachindunji, kuyenda nazo, ndi kutinso mphamvu zambiri, ndi zizindikilo ndi zozizwa zakhala zikuchitidwa ndi izo, ndipo kuti ulamuliro wao ndi Ulamuliro wa zaka Chikwi wokhazikika womwe umayembekezedwa, ndipo zakhala zikuuchita uwu kwa nthawi yaitali. Dziko lapansi lonse latembenuzidwa ndipo likugwirizana ndi lamulo la Sunday, kotero kuti ndi kagulu kochepa kofoka komweka komwe kakulimbana ndi kutsutsana ndi malamulo a dziko, komanso a Mulungu, podziona ngati ndi kokhako kakuchita choonadi pakati pa anthu onse a padziko." Mar. 167, 209.

## Satana Adziyerekeza Kuti Ali Khristu

"Podziyerekeza ngati mngelo wakuunika, iye [Satana] adzayendayenda pa dziko lonse lapansi monga wochita-zozizwa…Iye adzanka akulankhula mau opatsa chiyembekezo, ndikuchita ntchito zabwino zotamandika. Adzazionetsera ngati ali Khristu, ngakhale pali chinthu chimodzi chokha chidzamsiyanitsa iye ndi Khristuyo. Iye adzatembenuza anthu kuwachotsa ku malamulo a Mulungu. Koma ngakhale zidzakhala choncho, iye adzayesetsa kutsatira ndi kuchita zinthu mwachilungamo monga akadachitira Khristu, kotero kuti ngati nkotheka, akanyenge ngakhale osankhidwa omwe. Atsogoleri odzozedwa, mafumu a dziko, oweruza okhala ndi maulemu ao, adzamgwadira ndikubvomereza ziphunzitso zake za bodza…." FE 471. "Kupatula anthu okhawo omwe adzatchinjirizidwa ndi mphamvu ya Mulungu, podalira ndi kutsimikizika pa mau ake, koma dziko lonse lidzalowetsedwa mkambvulumbvulu wa chinyengo cha Satanayo." DD 23.

Mu mbadwo uno iye wokana-khristu adzadzionetsera ngati ali Khristu, ndipo panthawiyi lamulo la Mulungu lidzakanidwa ndikuyesedwa lopanda pake ndi mitundu ndiponso mapfuko onse a dziko lapansi ." Mar. 205. "Koma pali chinthu chimodzi chokha." "… Pali chinthu chimodzi chokha pa okhulupirira onse…moyo wosatha unalonjezedwa kwa onse omwe adzapirira kufikira chimariziro…. Maso ao mwachikhulupiriro adzayang'anitsitsa pa mpando wachifumu wonyezimira, womwe patsogolo pake padzaime anthu onse obvekedwa minjiro-yoyera. Khalidwe la chiyero ili ndilo lidzawatchinjiriza iwo kuti asatengeke ndi zochimwa…. [Satana] adzamva mapemphero akulira kwao kuti Khristu adze…kuwapulumutsa iwo. Ichi ndicho chidzampangitse iye [Satanayo] kudzionetsera ngati Khristu kuti olungamawo adzaone ngati kuti mapemphero ao ayankhidwa." LDE 164-5.

"M'khalidwe lake lakudziyerekeza ngati kuti ali Khristu, iye [Satana] adzaliuza dziko lapansi kuti anasintha Sabata kuliika pa Sunday, ndipo akulamulira anthu onse kulilemekeza tsiku lomwe iye walidalitsa'li. Iye adzapitiriza kufotokoza kuti onse amene akukakamira kusunga tsiku lachisanu ndi chiwiri akuchitira mwano dzina lake pokana kumvera kuunika ndi choonadi zomwe atumiki ake akuwauza. Ichi chidzakhala chenjerero lalikuru ndi la mphamvu, pafupifupi loposa machenjerero ena onse." "… Mu nthawi ya chinyengo choopysachi tidzaima osagwa pokhapokhapo ngati tidzakhale m'choonadi ndi mphamvu ya Mulungu…. Malingaliro akukhala pachoopsya cha munthu ali yense payekha, asatichititse mantha ndi kufoka pa chikhulupiriro, koma akhale chowalimbikitsa ndi kuwapatsa chiyembekezo anthu a Mulungu; pozindikira kuti nthawi yao yakuyesedwayi idzakhalanso nthawi yomwe Mulungu aionetsere poyera mphamvu yake yakugonjetsa ndi kupulumutsa." Mar. 194.

## Chilango cha mitu 3 Yomalizira

Chibvumbulutso 17:16 likufotokoza kuti nyanga khumizo "zidzadana ndi mkazi wachigololoyo, nizidzamkhalitsa wabwinja wausiwa, nizidzadya nyama yake, nizidzampsereza ndi moto." Koma ndi chifukwa ninji "mafumu adziko lapansi" "adzalira iye, nadzamlilira maliro" pamene ndi iwo adzamchitira zowawitsa zonsezi? Chibv. 18:9. Chifukwa iwo adzaturukira mochedwa kuti, "ndi nyanga [yake] mitundu yonse inasokeretsedwa" – kuphatikiza iwo eni. Chilango chougwera Babulo chinalinso chao. "Ochita malonda…analemera ndi kudyerera kwake" ndi "mafumu a dziko omwe anachita naye chigololo [chauzimu] "analandirako a machimo ake," choncho adzachiona chowawa iwo "kulandirako ya miliri yake." Pamene machenjerero onse a ziwanda zakusokeretsa adzaikidwa poyera kuti adziwike cheni cheni chomwe ali – chinsinsi cha ntchito za mizimu ya ziwanda – ndi anthu amene anatengako mbali pochita izi adzaoneka kuti anali otaika, opusa ndi opanda nzeru." Letter 311, 1905.

Chilango cha mitu itatu yomalizira ya pa chirombo chofiiritsa chidzaperekedwa mwa chilungamo: "Ndipo chinagwidwa chirombocho, ndi pamodzi nacho mneneri wonyenga amene adachita zizindikilo pamaso pake, zimene anasokeretsa nazo iwo amene adalandira lemba la chirombo, ndi iwo akulambira fano lake; iwo awiri anaponyedwa ali moyo m'nyanja yamoto yakutentha ndi sulfure: ndipo otsalawa [kuphatikiza nyanga khumi] anaphedwa ndi lupanga la Iye wakukwera pa kavalo, ndilo loturuka m'kamwa mwake; ndipo mbalame zonse zinakhuta ndi nyama zao." Chibv. 19:17-21. Pambuyo pongopita kanthawi kochepa chinjoka chachikuru mwini wake, "mdyerekezi wakusokeretsa anaponyedwa m'nyanja ya moto ndi sulfure, kumeneko kulinso chirombocho ndi mneneri wonyengayo…." Chibv. 20:10.

Koma za oyera mtima opirira kufikira chimaliziro kwaperekedwa mdalitso, "Odala iwo amene atsuka miinjiro yao, kuti akakhale nao ulamuliro pa mtengo wa moyo, ndi kuti akalowe m'mzinda pa zipata."

Onani, werengani ndi Kukopa Mabuku: www.bible-sabbath.com www.earthsfinalwarning.com www.evolution-facts.org www.present-truth.org www.worldincrisis.org www.pathlights.com wwwstepstolife.org

Tumizani ndemanga ndi mafunso zanu ku adiresi yomwe iri pafupi ndi inu:

**View, Read, or Print Books:** www.bible-sabbath.com www.earthsfinalwarning.com www.evolution-facts.org www.present-truth.org www.worldincrisis.org www.pathlights.com www.stepstolife.org

**MUKAFUNA KUMVA NDI KUDZIWA ZAMBIRI LEMBERANI KU:**


LOUD CRY AND FAMILY LIFE MINISTRIES
P.O. BOX 2850,
BLANTYRE,
MALAWI. CENTRAL AFRICA.

RESTORATION SEVENTHDAY ADVENTIST MINISTRIES
P. O. BOX 510751,
CHIPATA,
ZAMBIA. CENTRAL AFRICA.

ADVENT PROPHECY UPDATE
P.O. BOX 70516,
NDOLA,
ZAMBIA, CENTRAL AFRICA.